

Ellen G. White Estate

A photograph of a white lighthouse on a cliff overlooking the ocean at dusk. The lighthouse has a glowing lantern room. In the foreground, there are silhouettes of palm trees and other vegetation. The sky is a mix of blue and purple hues, with some clouds. The overall mood is serene and contemplative.

MAPAZI OPITA KWA KRISTU

ELLEN G. WHITE

**Mapazi Opita Kwa
Kristu**

Ellen G. White

**Copyright © 2014
Ellen G. White Estate, Inc.**

Information about this Book

Overview

This eBook is provided by the [Ellen G. White Estate](#). It is included in the larger free [Online Books](#) collection on the Ellen G. White Estate Web site.

About the Author

Ellen G. White (1827-1915) is considered the most widely translated American author, her works having been published in more than 160 languages. She wrote more than 100,000 pages on a wide variety of spiritual and practical topics. Guided by the Holy Spirit, she exalted Jesus and pointed to the Scriptures as the basis of one's faith.

Further Links

[A Brief Biography of Ellen G. White](#)
[About the Ellen G. White Estate](#)

End User License Agreement

The viewing, printing or downloading of this book grants you only a limited, nonexclusive and nontransferable license for use solely by you for your own personal use. This license does not permit republication, distribution, assignment, sublicense, sale, preparation of derivative works, or other use. Any unauthorized use of this book terminates the license granted hereby.

Further Information

For more information about the author, publishers, or how you can support this service, please contact the Ellen G. White Estate at mail@whiteestate.org. We are thankful for your interest and feedback and wish you God's blessing as you read.

MAU OYAMBA

M’mapirikaniro ambiri mumamveka kuitana kwa mtengo wap-
atari, “Idzani kuno kwa Ine,”—kuitana kwa Mpulumutsi wacifundo
amene mtima wace wa cikondi umapita kwa onse amene ali ku-
socera kulekana ndi Mulungu; ndipo m’mitima ya ambiri amene ali
kulakalakadi cithangato ca kupeza Yesu, mumauka cifuniro ca kub-
werera ku nyumba ya Atate. Oterewa kawiri kawiri amabwerezanso
cifunso ca Tomasi, “Tidzadziwa njira bwanji?” Nyumba ya Atate
iyang’anika ngati iri kutari, ndipo njira yace iwoneka yobvuta ndi
yosadziwika. Nanga mapazi ace ngotani amene amatsogolera njira
ya kunka kwathu?

Dzina la bukhuli lifotokoza nchito yace. Limasonyeza kwa Yesu
kuti ndiye yekha angathe kukwanitsa zosowa za moyo, ndi kutso-
golera mapazi okaika ndi otsimphina ku “njira ya mtendere.” Li-
matsogolera wofuna cilungamo ndi makhalidwe amphumphu, phazi
limodzi limodzi m’njira ya moyo wa Cikristu, ku cidzalo ca dal-
itso cimene cimapezeka m’kudzipereka kotheratu ndi cikhulupiriro
cosagwedezeka m’cisomo copulumutsa ndi mphamvu ya kusunga
ya Bwenzi la ocimwa. Malangizo opezeka m’bukhu ili anatengera
cisangalatso ndi ciyembekezo ku miyoyo yambiri yobvutika, ndipo
lathangata otsata Yesu ambiri kuyenda molimbika ndi mokondwa
m’mapazi a Mtsogoleri wawo wa kumwamba. Tiri kuyembekeza
kuti lidzanyamula uthenga womwewu kwa enanso ambirimbiri
amene ali kusowa cithangato comweci.

“Njira iwonekere Makwerero
opita kumwamba.”

Zinali coteru ndi Yakobo, pamene, atapanikizidwa ndi mantha
kuti chimo lace lamlekanitsa ndi Mulungu, iye anagona kupumula,
ndipo “analota, ndipo taonani makwerero anaima pa dziko, ndipo
pamwamba pace panafika kumwamba.” Motero cilumikizano ca
kumwamba ndi dziko lapansi cinaululidwa kwa iye, ndipo mau a

cisangalatso ndi ciyembekezo analankhulidwa kwa woyendayo ndi Iye amene anaima pamwamba pa makwererowo. Masomphenya a kumwambawa abwerezedwenso kwa ambiri pamene ali kuwerenga nthanoyi ya njira ya moyo.

OSINDIKIZA.

[5]

Contents

Information about this Book	i
MAU OYAMBA	ii
MUTU 1—CIKONDI CA MULUNGU KWA MUNTHU	5
MUTU 2—WOCIMWA ASOWA KRISTU	11
MUTU 3—KULAPA	15
MUTU 4—KUBVOMEREZA	25
MUTU 5—KUDZIPEREKA	29
MUTU 6—CIKHULUPIRIRO NDI KULANDIRIDWA	34
MUTU 7—YESO LA KUKHALA WOPHUNZIRA WA YESU	39
MUTU 8—KUKULA KUFANANA NDI KRISTU	46
MUTU 9—NCHITO NDI MOYO	53
MUTU 10—KUDZIWA MULUNGU	58
MUTU 11—UBWINO WA PEMPHERO	64
MUTU 12—COCITA NAKO KUKAIKA	73
MUTU 13—KUKONDWERERA MWA AMBUYE	79

MUTU 1—CIKONDI CA MULUNGU KWA MUNTHU

Cilengedwe ndi cibvumbulutso zimacitira umboni za cikondi ca Mulungu. Atate wathu wa kumwamba ndi kasupe wa moyo, wa nzeru, wa cimwemwe. Taonani zinthu zozizwitsa zokometsetsa za cilengedwe. Taganizani za nchito zace zozizwitsa pa kukwanitsa zosowa ndi cikondwerero ca anthu ndi ca zolengedwa zonse. Dzuwa ndi mvula, zimene zimakondweretsa ndi kutsitsimutsa dziko, mapiri ndi nyanja ndi madambo, zonsezi zimatiuza ife za cikondi ca Mlengi. Amene amakwanitsa zosowa za zolengedwa zace ndiye Mulungu. Davide ananena mau okometsetsa otere, —

“Maso a onse ayembekeza Inu ndipo muwapatsa cakudya cawo m’nyengo zawo. Muolowetsa dzanja lanu, nimukwaniritsira za moyo zonse cokhumba cawo.” Salmo 145: 15, 16.

Mulungu anapanga munthu woyera mtima ndi wokondwa; ndipo dziko lokongola pamene linaturuka m’manja a Mlengi linalibe kadontho kobvunda kapena mthunzi wa temberero. Cimene cadzetsa tsoka ndi imfayi, ndi kuswa malamulo a Mulungu — malamulo a cikondi. Komabe ngakhale pakati pa zobvuta zimene zimadza cifukwa ca zoipa, cikondi ca Mulungu cimaonekera. Zidalembedwa kuti Mulungu anatemberera nthaka cifukwa ca munthu. (Gen. 3: 17.) Minga ndi mitula— mabvuto ndi mayeso, zimene zimacititsa moyo wace kukhala wa nchito ndi wa nkhwana — zinaperekedwa cifukwa ca ubwino wace, kuti zikhale za kumphunzitsa nzeru ya Mulungu ya kumtukula ku cionongeko ndi manyazi amene anadza ndi ucimo. Ngakhale dziko lidagwa si la cisoni cokha cokha. Mwa cilengedwe muli uthenga wa ciyembekezo ndi cisangalatso. Pa mitengo ya minga pali maluwa.

Mau akuti “Mulungu ali cikondi,” alembedwa pa duwa liri lonse, ndi pa udzu uli wonse. Mbalame zimayimba nyimbo mokondwa mlengalenga, maluwa onunkhira, mitengo yobiriwira ya m’nkhalango, — zonse zimacitira umboni cisamaliro ca Atate Mulungu wathu ndi kuti Iye amafuna kukondwetsa ana ace.

Mau a Mulungu amaonetsa makhalidwe ace. Iye mwini ananena za cikondi cace ndi cifundo cace. Pamene Mose anapemphera, “Ndionetsenitu ulemerero wanu,” Yehova anayankha, “Ndidzapititsa ukoma wanga wonse pa maso pako.” (Eksodo 33: 18, 19.) Uwu hdiwo ulemerero wace. Yehova anapita pa maso ya Mose, napfuula, [8] “Yehova, Yehova, Mulungu wa cifundo ndi wa cisomo, wolekereza, ndi wa ukoma mtima wocuruka, ndi wa coonadi; wa kusungira anthu osawerengeka cifundo, wakukhulukira mphulupulu ndi kulakwa ndi kucimwa.” (Eksodo 34: 6, 7.) Iye “sasunga mkwiyo wace ku nthawi yonse popeza akondwera naco cifundo.” (Mika 7: 18.) “Ndi woleka coipaco.” (Yona 4: 2.)

Mulungu anamangirira mitima yathu kwa Iye ndi zizindikiro zosawerengeka m’mwamba ndi m’dziko lapansi. Mulungu anafuna kudziululira kwa ife kupyolera mwa nsinga za cilengedwe, zimene ziri nsinga zolimba za cikondi za dziko lapansi zimene mitima ya anthu ingazidziwe. Koma ngakhale zimenezi sizimaonetsera kweni kweni za cikondi cace. Ngakhale mboni zonsezi zina-perekedwa, mdani wa zabwino anadetsa mitima ya anthu kotero kuti anali kuyang’ana Mulungu ndi mantha; anamuganizira ngati woopsa wosakhulukira. Satana anatsogolera anthu kuganiza kuti Mulungu ali woweruza wa nkharwe, —amene zocita zace zonse ziri za ukari. Iye anamuganizira Mulungu ngati wakungoyang’anira ndi diso la nsanje kulonda zolakwa ndi zophophonya za anthu, kuti awalange. Yesu anadza kudzakhala pakati pa anthu kudzacotsa mdima umenewu pakusonyeza ku dziko lonse cikondi cosatha ca Mulungu.

Mwana wa Mulungu anadza kucokera kumwamba kudzaonetsera Atate. “Palibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana Wobadwa yekha wakukhala pa cifuwa ca Atate, Iyeyu anafotokozera.” (Yohane 1: 18.) “Ndipo palibe wina adziwa Atate, koma Mwana yekha, ndi iye amene Mwana afuna kumuululira.” (Mateyu 11: 27.) Pamene mmodzi wa akuphunzira anafunsa, “Tionetsereni Atate,” Yesu anayankha, “Kodi ndiri ndi inu nthawi yaikuru yotere, ndipo sunandizindikira Filipino? Iye amene wandiona Ine waona Atate, unena iwe bwanji, Mutionetsere Atate?” (Yohane 14: 8, 9.)

Pakufotokoza za nchito yace ya dziko lapansi, Yesu anati, “Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino, anandituma Ine kulalikira amnsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti

apenyenso, kuturutsa ndi ufulu wophwanyika.” (Luka 4: 18.) Imeneyi ndiyo inali nchito yace. Iye anapitapita nacita zabwino, ndi kuciritsa onse osautsidwa ndi Satana. Inalipo midzi yina yathunthu imene kubuula kwa odwala sikunali kumvekamo m’nyumba iri yonse; cifukwa Iye anapita pakati pawo, naciritsa odwala awo onse. Nchito yaceyo inali umboni wakuti anadzozedwa ndi Mulungu. Cikondi ndi cifundo zinaonetsedwa m’nchito iri yonse ya moyo wace; mtima wace unali kuwamvera cifundo ana a an- [9]thu. Iye anatenga makhalidwe a munthu, kuti akwanitse zosowa za munthu. Osauka ndi onyozeka sanali kuopa kudza kwa Iye. Ngakhale tiana tinadza kwa Iye. Tinakonda kukwera pa maondo pace, ndi kuyanga’nitsa nkhope yace, yodzazidwa ndi cikondi.

Yesu sanasiye mau amodzi a coonadi, koma masiku onse anali kuwalankhula m’cikondi. Polankhulana ndi anthu Iye anacita ndi luso ndi moganiza ndi mokoma mtima. Sanali wacipongwe, sanalankhule mau aukari, ndipo sanapweteke mtima wa munthu ali yense. Sanapeze cifukwa ndi zofooka za anthu. Iye analankhula coonadi, koma masiku onse analankhula mwa cikondi. Iye anadzudzula cinyengo, kusakhulupirira, ndi mphulupulu; koma misozi inali m’maso mwace pamene anali kunena mau odzudzulawo. Iye analirira Yerusalemu, mzinda umene anaukonda, umene unakana kumlandira Iye, amene ali Njira ndi Coonadi, ndi Moyo. Iwo anakana Mpulumutsi wawo, koma Iye anawamvera cifundo. Moyo wace unali wakudzikaniza yekha, ndi woganiza za kusamalira ena. Moyo wa munthu ali yense unali wa mtengo wapatali pa maso pace. Ngakhale anali nawo makhalidwe oyera a Umulungu, Iye anali kusamalira munthu ali yense wa banja la Mulungu. Mwa anthu onse Iye anaona miyoyo yakugwa imene anadzera kuipulumutsa.

Oterewa ndiwo makhalidwe a Kristu amene anaonekera m’moyo mwace. Amenewa ndiwo makhalidwe a Mulungu. Mitsinje ya cifundo coonetsedwa mwa Kristu, imadza kwa ana a anthu kucokera mu mtima mwa Atate. Yesu, Mpulumutsi wa cifundo ndi wokoma mtima, “Anaonetsera Mulungu m’thupi lace.” (1 Tim. 3: 16.)

Yesu anakhala panso pano nasautsidwa, nafa cifukwa ca kutiombola ife. Iye anasanduka “Munthu wa zisoni,” kuti ife tikalandirane nawo cimwemwe cosatha. Mulungu analola Mwana wace wokonededwa, wodzazidwa ndi cisomo ndi coonadi, kucoka ku dziko la ulemerero wosaneneka, kudza ku dziko loipitsidwa

[10] ndi ucimo, lodetsedwa ndi mthunzi wa imfa ndi temberero. Iye anamlola kusiya Atate wace wokonda, ndi cilemekezo ca angelo, kudzamva manyazi, kudzacididwa cipongwe, ndi kunyozedwa, ndi kudandidwa, ndi imfa. “Cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa.” (Yesaya 53: 5.) Muyang’aneni Iye m’cipululu, m’Getsemane pa Mtanda! Mwana wa Mulungu wopanda cirema anasenza katundu wa zoipa. Iye amene anali mmodzi ndi Mulungu, anamva m’moyo mwace kulekanitsidwa koopsa kumene kumacitika ndi zoipa pakati pa Mulungu ndi munthu. Zimenezi zidamliritsa mwa cisoni, “Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, mwandisiiranjx Ine?” (Mateyu 27: 46.) Cimene cinaswa mtima wa Mwana wa Mulungu, ndi katundu wa zoipa, pa kuzindikira kuopsa kwace, ndi kulekanitsidwa kwace kwa moyo ndi Mulungu.

Koma nsembe yaikuruyi sinapangidwe cifukwa cofuna kulenga mu mtima mwa Atate cikondi pa munthu, kapena kumpangitsa kulola kupulumutsa. Iai konse! “Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha.” (Yohane 3: 16.) Atate atikonda ife si cifukwa ca nsembe yaikuruyo, koma Iye anatipatsa ife nsembeyo, cifukwa ca kutikonda ife. Kristu anali Mnkhoswe, kupyolera mwa Iyeyo anali kutsanulira cikondi cace cosatha pa dziko lolepherali. “Mulungu anali mwa Kristu ali kuyanjanitsa dziko kwa Iye yekha.” (2 Akor. 5: 19.) Mulungu anasautsidwa pamodzi ndi Mwana wace. M’kusautsidwa kwa ku Getsemane, imfa ya pa Golgota, mtima wa cikondi wa Mulungu unalipira mtengo wa ciombolo cathu.

Yesu anati, “Cifukwa ca ici Atate andikonda Ine, cifukwa nditaya Ine moyo wanga, kuti ndikautengenso.” (Yohane 10: 17.) Ndiko kuti, “Atate wanga akukondani inu kotero kuti anandikonda Ine koposa cifukwa ndinapereka moyo wanga kukuombolani inu. Pakusanduka wolowa m’malo mwanu ndi Cikole canu; pa kupereka moyo wanga, pa kutenga mangawa anu, ndi macimo anu, ndikonedwa ndi Atate wanga; cifukwa ndi nsembe yanga, Mulungu angathe kukhala wolungama, ndi womuyesera wolungama iye amene akhulupirira Yesu.”

Palibe wina angathe kutiombola koma Yesu yekha; pakuti Iye yekha amene anali pa cifuwa ca Atate ndiye angathe kufotokoza za Iye. Iye yekha amene amadziwa kuya ndi utari wa cikondi

ca Mulungu, ndiye angathe kucionetsera. Palibenso kena koposa nsembe imene Kristu anaicita cifukwa ca anthu olephera, kangathe kutsimikiza cikondi ca Atate kwa anthu otaika.

“Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha.” Sanangompereka kudzakhala pakati pa anthu pokha, kunyamula zoipa zawo, ndi kufera nsembe yawo, koma anampereka kwa mtundu wonse wotaika. Kristu anadzilinganiza yekha ndi zokondweretsa ndi zosowa za anthu. Iye amene anali mmodzi ndi Mulungu anadzilumikiza ndi ana a anthu ndi mfundo zosaduka. Yesu, “sacita manyazi kuwachula iwo abale.” (Ahebri 2: 11.) Iye ndiye nsembe yathu, Mnkhoswe wathu, Mbale wathu, wakunyamula makhalidwe athu a umunthu patsogolo pa mpando wacifumu wa Atate, ndipo ku- pyolera zaka zosatha adzakhala mmodzi wa mtundu umene anaupulumutsa, — nadzachedwabe Mwana wa munthu. Zonsezi zinacitika kuti munthu akhululukidwe ku cionongeko ca ucimo, kuti aonetsere cikondi ca Mulungu, ndi kugawana nawo cimwemwe copatulika. [11]

Mtengo umene unaperekedwa kutiombola ife, nsembe yosatha ya Atate wathu wa kumwamba pakupereka Mwana wace kudzat- ifera ife, ziyenera kutipatsa maganizo akuru a cimene tidzakhala kupyolera mwa Kristu. Pamene mtumwi Yohane, wogwidwa ndi Mzimu Woyera anaona utari, kuya, bwambi wa cikondi ca Atate kwa mtundu woonongeka, anadzazidwa ndi kupembedza ndi kule- mekeza; ndipo, polephera kupeza cinenero cokwamira kufotokoza kukula kwa cikondi cimenezi iye anauza dziko lonse kuciyang’ana. “Taonani cikondico Atate ali naco pa ife, kuti tichedwe ana a Mu- lungu.” (1 Yohane 3: 1.) Zimenezi zimuyesera munthu kukhala wa mtengo wa patari! Cifukwa ca kuswa malamulo ana a anthu anasan- duka akapolo a Satana. Ndi cikhulupiriro mu nsembe ya Kristu ana a Adamu adzasanduka ana a Mulungu. Pakutenga makhalidwe a umunthu, Kristu anatukula anthu. Kupyolera mwa Kristu anthu olephera adzaikidwa kumene adzakhiladi oyenera kuchedwa “ana a Mulungu.”

Cikondi cotere ncosayerekezeka. Ana a Mfumu ya kumwamba! Lonjezo loposa! Cinthu coyenera kuciganizira! Cikondi cosay- erekezeka ca Mulungu kwa dziko limene silinamkonde Iye! Ga- nizo limeneli liri ndi mphamvu yotyola moyo, ndi kupangitsa mtima kugonjera cifuniro ca Mulungu. Tikamaphunzira kwambiri

makhalidwe a Mulungu m'kuwala kwa mtanda, tidzaonanso kwambiri cifundo, nsisi, ndi cikhululukiro zitalumikizana ndi ubwino ndi ciweruzo, ndipo tidzazindikiranso koposa maumboni osawerengeka a cikondi cosatha, ndi cifundo copitirira cifundo ca mai

[12] kwa mwana wace wa mphulupulu.

[13]

MUTU 2—WOCIMWA ASOWA KRISTU

Munthu poyamba anapatsidwa mphamvu zambiri ndi malingaliro abwino. Anali wangwiro m'makhalidwe ace ndi wogwirizana ndi Mulungu. Maganizo ace anali angwiro, ziyang'aniro zace zinali zopatulika. Koma cifukwa ca kusamvera, mphamvu zace zinaipitsidwa, ndipo umbombo unalowa m'malo mwa cikondi. Makhalidwe ace anafooka kwambiri cifukwa ca ucimo, kotero kuti cinali cosatheka, mu mphamvu yace yokha, kukaniza mphamvu ya zoipa. Anayesedwa kapolo wa Satana, ndipo akadakhale comweco nthawi zonse Mulungu akadapanda kuletsa. Cifuniro ca Satana cinali ca kuononga nzeru ya Mulungu ya kulenga munthu, nadzaza dziko ndi tsoka ndi cipululu. Ndipo iye akadanena kuti zoipa zonsezi zacitika cifukwa ca nchito ya Mulungu pa kulenga munthu.

M'makhalidwe ace osacimwa, munthu anali kulankhula ndi Iye “amene zolembera zonse za nzeru ndi cidziwitso zibisika mwa Iye.” (Akolose 2: 3.) Atacimwa, sanapezenso cikondwero m'kuyera, ndipo iye anafuna kubisala osafuna kuonana ndi Mulungu. Mtima uli wonse wosakonzedwa makhalidwe ace ndi wotere. Sulumikizana ndi Mulungu ndipo sukondwera kulankhula naye. Wocimwa sangakondwe pa maso pa Mulungu. Atakhala pakati pa angelo oyera athawapo. Monga ataloledwa kulowa kumwamba, sakapezako cimwemwe. Moyo wace sungabvomerezane ndi cikondi copanda umbombo cimene cimalamulira kumeneko, cifukwa mtima wa munthu ali yense umabvomerezana ndi mtima wa cikondi wa Mulungu. Maganizo ace, zokondweretsa zace, zidzakhala za cilendo kwa anthu opanda ucimo okhala kumeneko. Nyimbo yace singagwirizane ndi nyimbo ya kumwamba. Kwa iye kumwamba kudzakhala malo a mazunzo; adzidzafuna kubisala pa maso pa Iye amene ali kuwala kwace ndi cimwemwe cace. Si cifukwa ca kuti Mulungu saweruzira molungama cimene cidzawaletse ocimwa kulowa kumwamba: adzatsekedwa kunja cifukwa ca kuti sali oyenera ku lowako. Ulemerero wa Mulungu udzakhala moto wonyeka kwa

iwo. Iwo adzakondwera kuonongedwa kuti abisale ku nkhope ya Iye amene anafa kuwaombola.

[14] Kuli kosatheka kwa ife tokha kupulumuka m'dzenje la zoipa m'mene tamira. Mitima yathu iri yoipa ndipo ife sitingathe kuisintha. "Adzaturutsa coyera m'cinthu codetsa ndani? nnena mmodzi yense." "Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mu- lungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero." (Yobu 14: 4; Aroma 8: 7.) Sukulu, cifuniro ndi kuyesa kwa munthu, zonse ziri ndi nchito yawo koma zonsezo ziribe mphamvu. Kapena zingathe kukometsa kunja kokhaku, koma sizingathe kusintha mtima; sizingathe kuyeretsa kasupe wa moyo. Anthu asanasinthike ku ucimo kunka kukuyera, mphamvu idzigwira nchito m'kati mwawo ndipo mudzilowa moyo watsopano wocokera kumwamba. Mphamvuyo ndiye Kristu. Cisomo cace cokha ndico cingathe kupatsa moyo ku mitima ndi kuikokera kwa Mulungu ndi ku ungwiro. Mpulumutsi anati "Ngati munthu sabadwa kucokera kumwamba," ngati salandira mtima watsopano, cifuniro catsopano, nchito zatsopano, ndi makhalidwe atsopano, otsogolera ku moyo watsopano, "iye sangathe kuona ufumu wa Mulungu." ((Yohane 3: 3.) Ganizo la kuti ndi cofunika kukulitsa ubwino umene uli mwa cibadwidwe ca munthu ndi cinyengo coipa. "Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwa uzimu." "Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwa tsopano." (1 Akor. 2: 14; Yohane 3: 7.) Za Kristu zinalembedwa, "Mwa Iye munali moyo ndipo moyo unali kuunika kwa anthu," "ndipo palibe dzina lina pansu pa thambo la kumwamba lopatsidwa mwa anthu limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." (Yohane 1: 4; Mac. 4: 12.)

Siziri zokwana kungoona kukoma mtima kwa Mulungu, cikondi, cisamaliro ca Utate, ndi makhalidwe ace. Siziri zokwana kuzindikira nzeru ndi kulungama kwa malamulo ace, kuona kuti anakhazikika pa maziko osatha a cikondi. Paulo mtumwi anaona zonsezi pamene anati, "Ndibvomerezana naco cilamulo kuti ciri cabwino." "Cotero cilamulo ciri coyera, ndi cilangizo cace ncoyera, ndi colungama ndi cabwino." Koma ananenanso m'kusautsidwa ndi kuthedwa nzeru kwa moyo wace, "Koma ine ndiri wa thupi, wogulitsidwa kapolo wa ucimo." (Aroma 7: 16, 12, 14.) Iye analakalaka ungwiro, cilungamo, zimene analibe mphamvu mwa iye yekha kuzilandira,

ndipo iye anapfuula, “Munthu wosauka ine! adzandilanditsa ndani m’thupi la imfa iyi?” (Aroma 7: 24.) Kulira kotereku kunaturuka m’mitima yolemedwa m’maiko onse ndi m’mibadwo yonse. Kwa anthu onsewo kulipo kuyankha kumodzi kokha, “Taonani Mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene acotsa cimo lace la dziko lapansi.” (Yohane 1: 29.)

Ambiri ali zithunzithunzi zimene Mzimu Woyera afuna ku- fo- tokozera coonadi ici, ndi kucifotokozera miyoyo imene ifuna ku- masulidwa ku katundu wa zoipa. Pamene Yakobo anali kuthawa ku nyumba ya atate wace, atacimwa pa kunyenga Esau, iye analemedwa pa kuzindikira ucimo wace. Popeza anali yekha yekha, wolekan- itsidwa ndi zonse za kukondweretsa moyo wace, ganizo lalikuru loposa onse mu mtima mwace, linali la kuopa kuti ucimo wace wa- mulekanitsa ndi Mulungu, ndi kuti wakanidwa ndi Mulungu. Mwa cisoni anagona pansu kupumula, pakati pa mapiri, ndi nyenyezi ziri kuwala kumwamba. Pamene anali mtulo, kuwala kozizwitsa ku- nadza m’masomphenya ace, ndipo taonani, pa dambo pamene iye adagona padaoneka ngati paima makwerero opita kumwamba ndipo angelo a Mulungu anali kukwera natsika pamenepo pamene kucok- era mu ulemerero pamwamba, mau a Yehova anamveka ali kunena uthenga wa cisangalatso ndi ciyembekezo. Cimene cinakwanitsa cosowa ndi cilakolako ca moyo wa Yakobo cinaperekedwa coteru kwa iye, — Mpulumutsi. Ndi cimwemwe ndi kuthokoza anaona njira yotseguka imene iye, wocimwa, anapeza mwai wa kulankhula ndi Mulungu. Makwererowo anali kutanthauza Yesu amene ali Mnkhoswa woima pakati pa Mulungu ndi anthu.

[15]

Cimeneci ndi cithunzithunzi cimodzimodzi cimene Yesu anali kunena polankhula ndi Natanieli, pamene anati, “Mudzaona thambo lotseguka, ndi angelo a Mulungu atsika nakwera pa Mwana wa munthu.” Yohane 1: 51.) Pa mpatuko uja, munthu anadzilekanitsa yekha ndi Mulungu; dziko lapansi linali pakati, panalibenso kulankhulana. Koma mwa Kristu, dziko lapansi lalumikizananso ndi kumwamba. Mwa ubwino wace, Kristu anasanja phompho limene linacitika ndi ucimo, kuti angelo otumikira adzilankhulana ndi munthu. Kristu alu- mikizanitsa munthu wakugwa, m’kufooka kwace ndi m’kulephera kwace ndi Kasupe wa mphamvu yosatha.

Anthu sangathe kupambana, ngakhale ayesetse kudzuka, anthu sangathe, ngati iwo akana kasupe wa ciyembekezo ndi cithangato kwa mtundu wakugwawu. “Mphatso iri yonse yabwino, ndi cininkho ciri conse cangwiro.” (Yakobo 1: 17) zicokera kwa Mulungu. Popanda Iye palibe munthu angathe kukhala ndi makhalidwe angwiro. Njira yopita nayo kwa Mulungu ndiyo Kristu yekha. Iye ati, “Ine ndine Njira, ndi Coonadi, ndi Moyo: palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine.” (Yohane 14: 6.)

[16] Mtima wa Mulungu ulirira ana ace a dziko lapansi ndi ciko- ndi colimba koposa imfa. Pa kupereka Mwana wace, anatikhuthulira ife kumwamba konse mu mphatso imodzi yomweyo. Moyo wa Mpulumutsi ndi imfa yace ndi kupembedzera kwace, utumiki wa angelo, kudandaulira kwa Mzimu, Atate wakugwira nchito pamwamba pa zonse ndi mwa zonse, cikondi cosaleka ca anthu a kumwamba, — onsewa amagwirizana kuthangata ciombolo ca munthu.

Anthuni! Tiyeni tiganize za nsembe yodabwitsa imene idaperekedwa cifukwa ca ife! Tiyeni tiyese kuyamika nchito ndi cangu cimene Mulungu ali kucita pa kubwezanso otaikawo ndi kuwabwezera ku nyumba ya Atate. Zokopa zolimba coteri, ndi mphamvu zotere, sizingapezeke zoposa izi; mphotho kwa amene acita zabwino, kukalowa kumwamba, kukhala pamodzi ndi angelo, ciyanjano ndi cikondi ca Mulungu ndi Mwana wace, kukwezeka ndi kukula kwa mphamvu zathu zonse kwa nthawi zonse, — kodi zimenezi sizolimbitsa mtima zokwana kutiumiriza ife kupereka nchito ya mtima wofuna kwa Mlengi wathu ndi Mpulumutsi?

Ndiponso maweruzo a Mulungu otsutsana ndi ucimo, cilango cimene cirikudza, kuipitsidwa kwa makhalidwe athu, ndi cilango cotsiriza, zidalembedwa m’mau a Mulungu kuticenjeza ife kupewa nchito za Satana.

Kodi sitiyenera kusamalira cifundo ca Mulungu? Nanga akadacitanji koposa izi? Tiyeni tidziyanjanitse ndi Iye amene anatikonda ife ndi cikondi cozizwitsa. Tiyeni ticite nazo zinthu zimene anatipatsa, kuti tisandulike m’cifaniziro cace ndi kubwezeredwa ku ciyanjano ca angelo otumikira, ndi kuyanjana ndi kulankhulana ndi Atate ndi

[17] Mwana wace.

MUTU 3—KULAPA

Kodi munthu adzakhala bwanji wolungama ndi Mulungu? Kodi wocimwa adzayesedwa bwanji wolungama? Tingathe kuyeretsedwa ndi kulumikizana ndi Mulungu mwa Kristu mokha; koma nanga tingadze bwanji kwa Kristu? Ambiri ali kufunsa cifunso comwe cinafunsidwa ndi makamu a anthu pa tsiku la Pentekoste, pamene anatsutsidwa za ucimo, iwo anapfuula, “Tidzacita ciani?” Mau oyamba a kuyankha kwa Petro anali akuti, “Lapani.” (Mac. 2: 38.) Pa nthawi ina, pambuyo pace, iye anati, “Lapani,... ndipo bwererani kuti afafanizidwe macimo anu.” (Mac. 3: 19.)

Kulapa kutanthauza kucita cisoni ndi zoipa, ndi kuzisiya. Sitingausiye ucimo kufikira titaona kuipa kwace. Ngati sitingausiye kuyambira m’mitima moyo sungasinthike kweni kweni.

Alipo ambiri amene sazindikira makhalidwe a kulapa koono. Ambiri amacita cisoni kuti acimwa, ndipo amakonza kunjira kwawo, cifukwa amaopa kuti zoipa zawo ziwatengera mabvuto. Koma uku si kulapa monga mwa nzeru ya Bible. Amalira cifukwa ca mabvutowo, osati cifukwa ca ucimo. Cisoni cotere ndi conga ca Esau pamene anaona kuti ukulu wace wamtaikira ku nthawi zonse. Balamu, poopsedwa ndi mngelo woima m’njira yace ndi lupanga losolola, anabvomereza zoipa zace kuti angataye moyo wace; koma sikunali kulapa cifukwa ca zoipa, sikunali kutembenukai, sananyansidwe ndi zoipa zace. Yudase Isikarioti, atapereka Mbuye wace, ananena, “Ndinacimwa pakupereka mwazi wosalakwa.” (Mateyu 27: 4.)

Anabvomereza cifukwa ca kuopa ciweruzo. Zimene zinali kudza kwa iye ndizo zinali kumuopsa, koma munalibe cisoni ceni ceni mu mtima mwace ca kuti wapereka Mwana wa Mulungu v/opanda cirema, nakana Woyerayo wa Israyeli. Farao, pamene anali kusautsidwa ndi maweruzo a Mulungu, anazindikira cimo lace, m’ malo mwa kuti apulumuke cilangoco, koma anaumitsanso mtima miliriyo ikaletsedwa. Onsewa anali kulira cifukwa ca zobvuta zimene zinadza cifukwa ca ucimo, koma sanacite cisoni cifukwa ca zoipazo.

[18] Koma pamene mtima ugonjera mphamvu ya Mzimu wa Mulungu, cikumbumtima cidzauka, ndipo wocimwayo adzazindikira kupatulika kwace kwa malamulo a Mulungu, maziko a ufumu wace m’mwamba ndi pa dziko lapansi.

[19] “Kuunika kumene kuunikira munthu ali yense wakulowa m’dziko lapansi” (Yohane 1: 9), kumaunikira m’zipinda za mtseri za moyo, ndipo zobisika za mdima zimaonekera. Mtima umatsutsidwa. Wocimwayo amazindikira cilungamo ca Yehova, naopa kuonekera m’zoipa zace pamaso pa Wosanthula mitima. Iye aona cikondi ca Mulungu, kukoma ndi cimwemwe ca ungiwiro; iye alakalaka kutsukidwa ndi kuyanjanitsidwa ndi Mulungu.

Pemphero la Davide atagwa, lisonyeza makhalidwe a cisoni coona ca zoipa. Kulapa kwace kunali kooni ndi kocokera pansu pa mtima. Sanayese kubisa cimo lace; sanafune kupulumuka ku-ciweruziro; litero pemphero lace. Davide anaona kukula kwa zoipa zace; anaona kuipitsidwa kwa moyo wace; ananyansidwa nawo ucimo wace. Sanapempherere kukhululukidwa kokha, koma anapemphereranso mtima wangwiro. Iye analakalaka cimwemwe ca cilungamo, — kuti alumikizane ndi kuyanjana ndi Mulungu. Uku ndiko kunali kunena kwa moyo wace:

“Wodala munthuyu wokhululukidwa cimo lace; cokwiriridwa coipa cace. Wodala munthuyu Yehova samwerengera mphulupulu zace; ndimo mu mzimu mwace mulibe cinyengo.” (Salmo 32: 1, 2.) “Mundicitire ine cifundo, Mulungu, monga mwa kukoma mtima kwanu; monga mwa unyinjira wa nsoni zokoma zanu mu-fafanize macimo anga. Mubwereze kunditsuka mphulupulu yanga, ndipo muniyeretse kundicotsira coipa canga. Cifukwa ndazindikira macimo anga; ndipo coipa canga ciri pamaso panga cikhalire.... Muniyeretse ndi hisope ndipo ndidzayera munditsuke ndipo ndidzakhala wa mbu woposa matalala. ... Mundilengere mtima woyera Mulungu, mukonze mzimu wokhazikika m’kati mwanga. Musanditaye kundicotsa pamaso panu, musandicotsere Mzimu wanu woyera. Mundibwezere cimwemwe ca cipulumutso canu; ndipo mzimu wakulola undigwirizize.... Mundilanditse ku mlandu wa mwazi, Mulungu, ndinu Mulungu wa cipulumutso canga; lilime langa lidzakweza nyimbo ya cilungamo canu.” (Salmo 51: 1-14.)

Kulapa kotere sikungathe kucitika ndi mphamvu yathu; kumacokera mwa Kristu mokha, amene anakwera kumwamba naninkha za ufulu kwa anthu.

Napa pamene amacimwirapo ambiri, cifukwa cace amalephera kulandira thandizo limene Kristu amafuna kuwapatsa. Iwo amaganiza kuti sangathe kudza kwa Kristu koma ngati ayamba kulapa, ndipo kuti kulapa ndiko kumakonza cikhululukiro ca macimo. Ndi zoonadi kuti munthu amayamba kulapa asanakhululukidwe; cifukwa ndi mtima wokha wosweka ndi wodzicepetsa umene umazindikira [20] kuti usowa Mpulumutsi. Koma nanga wocimwayo kodi adziyamba kulindira kufikira atalapa asanadze kwa Yesu? Kodi kulapaku kukhale ngati copinga pakati pa wocimwa ndi Mpulumutsi?

Bible saphunzitsa kuti wocimwa koma ayambe walapa asanasamalire kuitana kwa Kristu, “Idzani kuno kwa Ine, nonsenu akulema ndi akutodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu.” (Mateyu 11: 28.) Cimene cimatsogolera anthu kulapa ndi ubwino wocokera kwa Kristu. Petro anafotokoza zomveka kwa Israyeli, pamene anati, “Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lace la manja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi cikhululukiro ca masimo.” (Mac. 5: 31.) Sitingathe kulapa wopanda Mzimu wa Kristu kudzutsa cikumbumtima cathu, monga momwe sitingathe kulandira cikhululukiro wopanda Kristu.

Kristu ndiye kasupe wa zabwino zonse. Iye yekha ndiye angathe kuika udani wa ucimo mu mtima mwathu. Cilakolako ciri conse ca kucita zabwino ndi zoonadi, kutsutsidwa kuli konse kwa zoipa za m’mitima yathu, ndiwo umboni wakuti Mzimu wace uli kugwira nchito m’mitima yathu.

Yesu anati, “Ine, ngati nditukulidwa ku dziko lapansi, ndidzokokera anthu onse kwa Ine ndekha.” (Yohane 12: 32.) Kristu adzionetsedwa kwa wocimwa ngati Mpulumutsi amene anafera zoipa za dziko lonse; ndipo pamene tiona Mwana wa Nkhosa wa Mulungu pa mtanda, cinsinsi ca ciombolo ciyamba kuzindikirika m’mitima yathu, ndipo ubwino wa Mulungu utitsogolera ife kukulapa. Pa kufera ocimwa Kristu anaonetsa cikondi cosazindikirika: ndipo pamene wocimwa aona cikondi cimeneci, cimafewetsa mtima wace, ndipo moyo wace umamva cisoni ndi zoipa zace.

Zoonadi anthu ena nthawi zina amacita manyazi ndi njira zawo zoipa, nasiya makhalidwe awo ena oipa, asanazindikire kuti ali

kukokedwa kunka kwa Kristu. Koma akafuna kukonzanso, ndi mtima wofuna kucita zabwino, ndi mphamvu ya Kristu imene iri kuwakokayo. Mphamvu imene iwo saidziwa imagwira nchito m'moyo, ndipo cikumbumtima cimauka ndipo moyo wa kunja umakonzedwanso. Ndipo pamene Kristu awakoka iwo kuyang'ana pa mtanda wace, kumuona Iye amene anapyozedwa ndi zoipa zawo, pompo malamulo amadza m'cikumbumtima mwawo. Kuipa kwa moyo wawo, zoipa za m'kati mwa moyo wawo zimaululidwa kwa iwo. Iwo amayamba kuzindikira za cilungamo ca Kristu, nanena, [21] “Kodi ucimo nciani? poti udzifuna nsembe yotere pofuna kuombola amene adacimwa? Kodi cikondi conseci, kusautsidwa konseku, kucepetsedwa konseku, kunacitika kuti ife tisataike, koma tikhale nawo moyo wosatha?”

Wocimwayo atafuna nkukana cikondi cimeneci, ndi kukana kukokedwa kwa Kristu; koma ngati sangakane, adzakokedwa kudza kwa Yesu; kudziwa za nzeru ya cipulumutso kudzamtso golera iye pa tsinde la mtanda pa kulapa zoipa zace zimene zinasautsa Mwana wokondedwa wa Mulungu.

Mtima umodzimidzi wa Mulungu umene uli kugwira nchito m'zinthu za cilengedwe uli kulankhula ndi mitima ya anthu, nuwalengera cilakolako ca kanthu kena kamene iwo alibe. Zinthu za dziko lapansi sizingathe kukwanitsa zolakalaka zawo. Mzimu wa Mulungu uli kuwapembedza iwo kuti afunefune zinthu zimene zingawapatse mtendere ndi mpumulo, — cisomo ca Kritisu ndi cimwemwe ca kuyera mitima. Ndi mphamvu zooneka ndi zosaoneka, Mpulumutsi wathu ali kugwira nchito nthawi zonse kukopa mitima ya anthu kuti asiye zokondweretsa zopanda pace za dziko lapansi, ndi kulandira madalitso osatha amene ali awo mwa Kristu. Kwa miyoyo yonse, imene iri kufunafuna kumwera m'mitsuko yosweka ya dziko lapansi, Uthenga wa Mulungu uti, “Iye wakumva ludzu adze. Ndi iye wofuna atenge madzi a moyo kwaulere.” (Cibvu. 22: 17.)

Inu amene m'mitima mulakalaka kanthu kabwino koposa kamene mungakapeze m'dziko lapansi muzindikira kuti cilakalako cimeneci ndi mau a Mulungu m'moyo mwanu. M'pempheni kuti akupatseni kulapa, kuti akuonetsereni Kristu m'cikondi cace cosatha ndi mu ungwiro wace wonse. M'moyo wa Mpulumutsi, maziko a cilamulo ca Mulungu—cikondi kwa Mulungu ndi kwa munthu

zinasonyezedwa. Moyo wace unali wokonda, wopanda umbombo. Tidzaona kuipa kwa mitima yathu, pamene ife timuona Iye ndi kuwala kofumira kwa Mpulumutsi wathu.

Kapena tiri kungodzinyenga tokha monga anacita Nekodimo, kuti moyo uli wolungama, makhalidwe athu ali abwino, ndi kuganiza kuti sitifunika kudzicepetsa pamaso pa Mulungu monga wocimwa: koma pamene kuunika kwa Kristu kuwala m' moyo mwathu, tidzaona zonyansa zathu: tidzazindikira umbombo wathu, ndi udani umene tiri nawo ndi Mulungu, zimene zimaipitsa nchito iri yonse ya moyo wathu. Pamenepo tidzadziwa kuti cilungamo cathu ciri nsanza zonyansa, koma mwazi wa Kristu wokha ndiwo ungatitsuke ife ku zoipa zonse nulenganso mitima yathu kukhala yofanana ndi Iye.

Ulemerero wa Mulungu pang'ono, ndi ungwiro wa Kristu [22] pang'ono zitalowa m'moyo, konyansa kali konse ka mu mtima kadzaonekera bwino lomwe, nizionetsera poyera zifukwa ndi zofooka za makhalidwe a munthu. Zimaonetsera poyera zifuniro zoipa, kusakhulupirira kwa mtima, zonyansa za milomo. Makhalidwe osamvera a wocimwa amene amayesa cabe malamulo a Mulungu amaonekera poyera, ndipo mzimu wace umabvutidwa ndi mphamvu yakufunafuna ya Mzimu wa Mulungu. Amanyansidwa yekha pamene aona makhalidwe angwiro opanda banga a Kristu.

Pamene mneneri Danieli anaona ulemerero umene unazinga mthenga wa kumwamba amene anatumidwa kwa iye, anathedwa nzeru pa kuzindikira kufooka kwace ndi kusakonzeka kwace. Pa kufotokoza mphamvu ya cooneka cozizwitsaco, iye anati, “Koma wosakhala ndi mphamvu ine; pakuti kukomoka kwanga kunasandulika cibvundi, wosakhalanso ndi mphamvu ine.” (Danieli 10: 8.) Moyo wokhudzidwa cotere udzadana ndi umbombo wace, ndi kudzikonda wokha, ndipo udzafunafuna, mwa cilungamo ca Kristu, mtima wangwiro umene uyanjana ndi malamulo a Mulungu ndi makhalidwe a Kristu.

Paulo ati kuti “Monga mwa cilungamo ca m'lamulo, “—monga mwa nchito za kunja kwa thupi, — iye anali “wosalakwa;” (Afilipi 3: 6) koma pamene anazindikira makhalidwe a uzimu a malamulo, anadziona yekha kuti ali wocimwa. Poweruzidwa ndi malamulo monga anthu anali kuonera ndi moyo wace wa kunja, iye anali wosacimwa; koma pamene anayang'anitsa m'kati mwa mala-

mulo, nadziona yekha monga m'mene Mulungu anali kumuonera, iye anawerama m'kudzicepetsa nabvomereza zoipa zace. Iye ati, "Ndipo kale ine ndinali wa moyo popanda lamulo; koma pamene lamulo linadza, ucimo unatsitsimuka, ndipo ine ndinafa." (Aroma 7: 9.) Pamene iye anaona makhalidwe a uzimu a malamulo, ucimo unaonekera m'kuopsa kwace kweni kweni, ndipo kudzikweza kwace kunacoka.

Mulungu samaganiza kuti macimo onse ndi amodzimidzi kukula kwawo; iripo miyezo yosiyanasiyana ya ucimo, monga. m'mene ayesera anthu; koma ngakhale coipa cioneke cacing'ono m'maso mwa anthu, palibe chimo laling'ono pamaso pa Mulungu. Ciweruzo ca munthu ndi ca tsankho, ndiponso si cangwiro; koma Mulungu amayeza zinthu monga momwe ziri. Woledzera amanyozedwa, ndipo amauzidwa kuti ucimo wace udzamletsa kulowa kumwamba; pamene amaleka onyada, a umbombo ndi osirira osawadzudzula. Koma amenewa ndiwo macimo oipitsitsa pamaso pa Mulungu; ci-
 [23] fukwa atsutsana ndi makhalidwe ace a cikondi, cikondi cimene cidzaza maiko onse osacimwa a kumwamba. Iye amene amagwa m'zoipa zazikuru, angamve manyazi ndi umphawi nadziwa kuti asowa cisomo ca Kristu; koma onyada saona kusowa, ndipo coteru amatsekera Kristu ndi madalitso osatha amene anadza kudzapereka.

Wa msonkho wosauka yemwe anapemphera, "Mulungu mundicitire cifundo ine wocimwa" (Luka 18: 13), anadziyesa yekha Wocimwa kwambiri, ndipo ena anali kumuyang'ana iye monga momwemo; koma iye anazindikira kusowa kwace, ndipo ndi katundu wa zoipa zace ndi manyazi anadza kwa Mulungu, napempha cifundo. Mtima wace unatsegukira Mzimu wa Mulungu kugvvi-ramo nchito yace yacifundo ndi kummasula ku mphamvu ya ucimo. Pemphero ya Mfarisi lodzikuza ndi lodziyera yekha wolungama linasonyeza kuti mtima wace unatsekeka kuti mphamvu ya Mzimu Woyera singathe kulowamo. Cifukwa ca kuti anali patari ndi Mulungu, sanazindikire kuipa kwace, pa kusiyana ndi makhalidwe opatulika a Mulungu. Analibe kusowa, ndipo coteru sanalandire kanthu.

Ngati uona kuipa kwako, usalindire kudzikometsa wekha. Alipo ambiri amene amaganiza kuti sali abwino kokwana kudza kwa Kristu. Kodi uli kuyembekeza kuti ukhala wabwino ndi kuyesa kwa iwe wekha? "Kodi Mkusi angathe kusintha khungu lace, kapena

nyalugwe maanga ace? Pamenepo mungathe inunso kucita zabwino, inu amene muzolowera kucita zoipa.” (Yer. 13: 23.) Cithangato cathu ciri mwa Mulungu mokha. Tisamalindira kukopa kolimba, nthawi yabwino, kapena makhalidwe oyera, koposa zimene tiri nazo. Sitingathe kucita kanthu mwa ife tokha. Tidzingodza kwa Kristu monga momwe tiri.

Koma ena asadzinyenge ndi kuganiza kuti, Mulungu, popeza ali wa cikondi ndi wa cisomo, adzapulumutsa ngakhale amene akana cisomo cace. Kuipa kwa ucimo kungathe kuyezedwa m’kuwala kwa mtanda. Pamene anthu amanena kuti Iye ali wabwino sangataye wocimwa, ayenera kuyang’ana pa mtanda. Kristu anasenza zoipa ndi kusamvera, nasautsidwa nafa m’ malo mwa ocimwa, cifukwa ca kuti panalibe njira ina yopulumutsira munthu, cifukwa wopanda nsembe imenyi cinali cosatheka kupulumutsa anthu ku mphamvu ya zoipa, ndi kuyanjanitsidwa ndi oyera a kumwamba, — ndi kukhala olandirana nawo moyo wa uzimu. Cikondi, ndi masautso, ndi imfa ya Mwana wa Mulungu, zonsezi zicitira umboni kuopsa kwa ucimo, ndi kunena kuti, ngati moyo sudzipereka kwa Kristu, palibe kupulumuka ku mphamvu ya ucimo, palibe ciyembekezo ca moyo wa kumwamba.

[24]

Wocimwa nthawi zina amadzikhululukira okha pa kunena za amene adziyesera okha Akristu, “Ndine wabwino ngati iwo omwe. Sadzikana, sadziletsa, ndipo alibe makhalidwe koposa ine. Amakonda zokondweretsa ndi zofuna zawo monga ine ndemwe.” Motero amayesa zolakwa za ena mokanira kuleka nchito yawo. Koma zifukwa ndi zoipa za anthu ena sizikhululukira munthu ali yense; cifukwa Yehova sanatipatse ife citsanzo ca munthu wofooka wa ucimo. Mwana wa Mulungu wopanda banga ndiye citsanzo cathu, ndipo iwo amene amadandaula za njira yoipa ya amene adziyesera okha Akristu, iwowo ndiwo ayenera kusonyeza miyoyo yokoma ndi citsanzo cabwino. Ngati iwo amazindikira cimene Mkristu ayenera kucita, nanga cimo lawo siliri lalikuru? Iwo amadziwa cimene ciri cabwino, koma nakana kucicita.

Pewani kuzengereza. Musaleke nchito ya kusiya zoipa zanu, ndi kufuna mtima woyera mwa Kristu. Ambirimбири amacimwira pamenepa, nataika kosatha. Sindinena kwambiri za kuti moyo uli waufupi ndi wosadziwika kukhala kwace; koma ciripo coopsa cacikuru — coopsa cosazindikirika — pa kucedwa kugonjera mau

odandaula a Mzimu wa Mulungu, ndi kusankha kukhala m'zoipa; cifukwa kucedwako ndi kumeneku. Cimo, ngakhale licepe, adzataika nalo kosatha munthu wakulumirirayo. Cimene siticigonjetsa, cidzatigonjetsa ife, ndipo cidzationonjetsa.

Adamu ndi Hava anadzinyenga okha kuti m'kanthu kakang'ono kotere, kungodya zipatso zokanizidwa, sikungaoneke zoopisa zotere zonga zimene Mulungu adaneneratu. Koma kanthu kakang'onoka kunali kuswa malamulo opatulika a Mulungu, ndipo kanamlekanitsa munthu ndi Mulungu, ndi kutsegulira imfa ndi matsoka osaneneka m'dziko lathu. Mbadwo ndi mbadwo uli kulira pa dziko lapansi, ndipo cilengedwe conse ciri kubuula ndi kusautsika ndi zowawa cifukwa ca kusamvera kwa munthu. Kumwamba kudamvanso cimализiro ca kupandukira Mulungu kwaceko. Mtanda umaima ngati cikumbutso ca nsembe yozizwitsa imene inacitika kupembedzera cifukwa ca kuswa malamulo a Mulungu. Tisauyang'ane ucimo ngati cinthu cacing'ono.

Kacimo kali konse, kukana cisomo ca Kristu, ziri kucita kanthu pa moyo wako; ziri kuumitsa mtima wako, ziri kucepetsa cifuniro, ziri kuumitsa mphamvu ya kuzindikira, ndipo ziri kucepetsa mphamvu yako ya kugonjera kudandaula kwa Mzimu Woyera wa Mulungu.

[25] Ambiri ali kutonthoza cikumbumtima cobvutika pa kuganiza kuti adzasintha njira yoipayo nthawi ina akadzafuna; kuti adzingosewera ndi kuitana kwa cifundo, ndipo namangopembedze- dwabe kawiri kawiri. Iwo amaganiza kuti atanyoza Mzimu wa cisomo, atataya mphamvu yawo pa mbali ya Satana, pa nthawi yoopisa adzasintha njira yawo. Koma zimenezi sizimacitika mofewa. Macitidwe, maphunziro, a moyo wace, amanga makhalidwe kotero kuti nthawi imeneyi ndi owerengeka okha amafuna kulandira Uthenga wa Yesu.

Ngakhale koipa kamodzi, kacifuniro kamodzi koipa, kocitidwa dala, kadzacotsa mphamvu yonse ya Uthenga. Kacimo kali konse kamalimbitsa mtima kusakonda Mulungu. Munthu amene aonetsera kuuma mtima ndi kusakhulupirira coonadi, ali kungokolola zomwe iye yemwe adafesa. M'Bible monse mulibe kucenjeza kwina koopisa, konena kupewa kusewera ndi ucimo, koposa mau a munthu wa nzeru, kuti munthu wocimwa “adzamangidwa ndi zingwe za ucimo wace.” (Miyambo 5: 22.)

Kristu ali wofulumira kutimasula ku ucimo, koma iye sakakamiza cifuniro cathu, ndipo ngati cifuniro cathu ciumirirabe kucita zoipa, ndipo ife osafuna kumasulidwa, ngati ife sitifuna kulandira cisomo cace, nanga Iye angacitenji? Tadziononga tokha pakutsimikiza kukana cikondi cace. “Taonani, tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la cipulumutso.” “Lero ngati mudzamva mau ace musaumitse mitima yanu.” (2 Akori. 6: 2; Heb. 3: 7, 8.)

“Pakuti munthu ayang’ana zooneka ndi maso, koma Yehova ayang’ana mu mtima” (1 Sam. 16: 7), mtima wa munthu, ndi cimwemwe ndi cisoni cace, mtima woyendayenda wamphulupulu m’mene mukhalitsa zonyansa ndi cinyengo. Iye adziwa zotsimikiza zace zonse. Pita kwa iye ndi mtima wako woipitsidwa monga momwe uli. Monga Davide utsegulire kwa diso loona zonse, nunene, “Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga; muniyese nimudziwe zolingalira zanga. Ndipo mupenye ngati ndiri nawo mayendedwe oipa, nimunditsogolere pa njira yosatha.” (Salmo 139: 23, 24.)

Ambiri amangolandira cipembedzo, maonekedwe ace okha, pamene mtima uli wosatsukidwa. Pemphero lanu likhale la kuti, “Mundilengere mtima woyera Mulungu; mukonze mzimu wokhazikika m’kati mwanga.” (Salmo 51: 10.) Cita nawo moona moyo wako. Khala woona mtima, ndi wolimba mtima monga ngati uli kudziwa kuti moyo wako uli moopsa. Umenewu ndi mlandu woyenera kukonzedwa pakati pa moyo wako ndi Mulungu ku nthawi yosatha. Ngati uzengereza, osacita kanthu, udzaonongeka.

Phunzira mau a Mulungu ndi kupemphera. Mau amenewo adzakusonyeza m’malamulo a Mulungu ndi m’moyo wa Kristu maziko ace a kuyera mtima, wopanda zimenezo “palibe mmodzi adzaona Ambuye.” (Heb. 12: 14.) Mauwo amatsutsa zoipa, amaonetsa njira ya cipulumutso. Asamalire, monga mau a Mulungu akulankhula ndi moyo wako.

Pamene muona kukula kwace kwa ucimo, pamene mudziona nokha monga momwe muli, musalephere. Kristu anadza kudzapulumutsa ocimwa. Iye sitifunika kumuuzza Mulungu kuti ayanjane nafe, koma — Taonani cikondi cozizwitsa! — Mulungu mwa Kristu ali kuyanjanitsa dziko kwa Iye yekha.” 2 Akor. 5: 19. Iye ali kupembedza ndi cikondi cace mitima ya ana ace ocimwa. Palibe kholo lina

[26]

pa dziko lapansi limene limapirira ndi zolakwa za ana ace, monga amacitira Mulungu ndi iwo amene afuna kuwapulumutsa. Palibe wina angathe kupembedzera wocimwa koposa Iye. Palibe milomo ya munthu imene imadandaulira munthu wosocera monga amacitira Iye. Malonjezano ace onse ndi macenjezo ace onse ali a cikondi cosaneneka.

Pamene Satana afika nakuuza kuti ndiwe wocimwa kwambiri, yang'ana kwa Mombolo wako, nulankhule za cifundo cace. Cimene cingakuthangate iwe ndiko kuyang'ana ku kuunika kwace. Zindikira zoipa zako, koma muuze mdaniyo kuti “Kristu anadza m'dziko lapansi kupulumutsa ocimwa” (1 Tim. 1: 15), ndi kuti iwe ungapulumutsidwe ndi cikondi cace cosatha. Yesu anafunsa Simoni za angongole awiri. Wina anamkongola mbuye wace ndalama pang'ono, koma wina anakongola ndalama zambiri; koma iye anawakhulukira onse awiriwo, ndipo Kristu anamfunsa Simoni,, Ndi uti wa awa awiri anakonda mbuye wace koposa?” Simoni anayankha, “Iye amene anamkhulukira zoposa.” (Luka 7: 43.) Ife tinacimwa kwambiri, koma Kristu anafa kuti ife tikhulukidwe. Nsembe yace iri yokwana kuonekera kwa Atate m'malo mwa ife. Iwo amene anawakhulukira zambiri adzankonda koposa, ndipo adzaima pafupi ndi mpando wace kumtamanda Iye cifukwa ca cikondi cace cacikuru ndi nsembe yace yosatha. Timazindikira kuipa kwace kwa ucimo, pamene ife tizindikira kweni kweni cikondi ca Mulungu. Pamene ife tiona kutalika kwa unyolo umene unatsitsidwa cifukwa ca ife, pamene ife tizindikira za nsembe yosatha imene Kristu anaipereka cifukwa ca ife, mtima umasungunuka ndi kusweka ndi kudzicepetsa.

[27]

MUTU 4—KUBVOMEREZA

“WOBISA macimo ace sadzaona mwai; koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacididwa cifundo.” (Miyambo 28: 13.) Makhalidwe a kulandirira cifundo kwa Mulungu ali ofewa ndi olungama ndi oyenera. Yehova satifunsa ife kucita cinthu cacikuru kuti tilandire cikhululukiro ca macimo. Sitifunika kutoyenda maulendo atari ndi otopetsa, kapena, kucita zina zopweteka, kupereka miyoyo yathu kwa Mulungu wa kumwamba, kapena kupembedzera zoipa zathu; koma wakuwabvomereza ndi kuwasiya macimo ace adzacididwa cifundo.

Mtumwi ati, “Cifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritidwe.” (Yakobo 5: 16.) Bvomerezani zoipa zanu kwa Mulungu, amene angathe kukhulukira, ndi zolakwa zanu kwa wina ndi mnzace. Ngati walakwira mnzako, kabvomereze kwa mnzako yemweyo ndipo ndi nchito yace kukhulukira iwe. Pompo ukafunse cikhulukiro kwa Mulungu, cifukwa mnzako wamcimwirayo ndi cuma ca Mulungu, ndipo pakumpweteka iye wacimwira Mlengi wace ndi Mombolo wace. Mlanduwo umatengedwa pamaso pa Mnkhoswe woota, Mkuru Wansembe wathu, amene “anayesedwa m’zonse monga momwe ife koma wopanda ucimo, ndi amene “amamva cifundo ndi zofooka zathu” (Heb. 4: 15), ndipo ali wakutha kutsuka cimo liri lonse.

Iwo amene sanapereke miyoyo yawo pamaso pa Mulungu pa kubvomereza zoipa zawo, sanaponde khweleri loyamba la kulandiridwa. Ngati ife sitinalape coteri, ndipo sitinabvomereze zoipa zathu ndi mzimu wosweka ndi wodzicepetsa, ndi kunyansidwa nazo mphulupulu zathu, sitinacifune moonadi cikhulukiro ca macimo; ndipo ngati sitinacifune, sitinaupeze mtendere wa Mulungu. Cifukwa cace cimene sitimasuka ku zoipa zathu za kale, ndi cifukwa cakuti sitiri olola kucepetsa mitima yathu ndi kuyanjana ndi macitidwe a mau a coonadi. Malangizo anafotokozedwa mokwana za mlandu umenewu. Kubvomereza macimo ngakhale pa anthu ambiri

kapena mtseri, kudzikhala kocokera mu mtima, ndi kofotokozedwa bwino lomwe. Wocimwayo asamakakamidzidwa. Asamangonena mosasamala, kapena kukakamizidwa ndi iwo amene sazindikira kunyansa kwace kwa ucimo. Kubvomereza kumene kumacokera pansu pa mtima kumapeza njira yopita kwa Mulungu wa cifundo cosatha. Davide ati, “Yehova ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka, apulumutsa iwo a mzimu wolapadi.” (Salmo 34: 18.)

[28] Kubvomereza koonna masiku onse nkwa makhalidwe odziwika
 [29] bwino kochula zoipa zeni zenizo. Ngakhale zikhale zokabvomereza Mulungu yekha; kapena ndi zokabomerezera pamaso pa anthu ena amene asautesidwa nazo zoipa zathuzo; kapena ndi zodziwika kwa onse, ndipo ziyenera kubvomerezera pamaso pa anthu onse. Koma kubvomereza kuli konse kudzikhala koonadi kwa kuchula zoipa zeni zeni zimene iwe wacitazo.

M’masiku a Samueli, a Israyeli anapatukana ndi Mulungu. Iwo anali kusautsidwa cifukwa ca zoipa zawo; cifukwa anataya cikhulupiriro cao mwa Mulungu, nataya cizindikiro ca mphamvu zace ndi nzeru zace za kulamulira mtunduwo, nataya cikhulupiriro m’nzeru zace za kucinjiriza ndi kuonetsera nchito yace. Iwo adasiyana ndi wolamulira wa dziko lonse, nafuna kulamulidwa monga amitundu akuwazungulira. Asanapeze mtendere, anabvomereza momveka cotere: “Popeza pamwamba pa zoipa zathu zonse, tinaonjeza coipa ici, ca kuti tinadzipemphera mfumu.” (1 Sam. 12: 19.) Anabvomereza cimo leni leni limene anacitalo. Kusayamika kwawo kunasautsa miyoyo yao ndi kuwalekanitsa ndi Mulungu wawo.

Kubvomereza sikungalandiridwe kwa Mulungu ngati sikuli kulapa koonna ndi kukonzanso. Koma m’moyo musinthike; cinthu ciri conse coipira Mulungu cicotsedwe. Izi zidzacitika ngati timva cisoni ndi zoipa zathu. Nchito imene tiyenera kucita pa mbali yathu idafotokozedwa bwino lomwe: “Sambani, dziyeretseni; cotsani macitidwe anu oipa pa maso panga, lekani kucita zoipa; phunzirani kucita zabwino; funani ciweruzo; thandizam osautsidwa, weruzirani ana a masiye, munenere akazi a masiye.” (Yesaya 1: 16, 17.) “Woi-payo akabweza cikole, nakabweza ico anacilanda mwa cifwamba, nakayenda m’malemba a moyo, wosacita cosalungama, adzakhala ndi moyo ndithu, sadzafa.” (Ezek. 33: 15.) Pa kunena za nchito ya kulapa Paulo ati: “Mudamvetsedwa cisoni ca kwa Mulungu, khama

lalikuru lanji cidalicita mwa inu, komanso codzikonza, komanso mkwiyo, komanso mantha, komanso kukhumbitsa, komanso cangu, komanso kubwezera cilango! M’zonse munadzitsimikizira nokha kuti muli oyera mtima m’menemo.” (2 Akor. 7: 11.)

Pamene ucimo upha zitsimikizo za makhalidwe abwino, wocita zoipayo sazindikira zilema za makhalidwe ace, kapena kuzindikira kukula kwace kwa zoipa zimene iye wazicita; ndipo ngati sagonjera ku mphamvu yotsutsa ya Mzimu Woyera, adzangokhalabe mu mdima wosazindikira zoipa zace. Kubvomereza kwace sikuli koon mtima. Akapezedwa kuti wacita zoipa amangopeza mookanira, ndipo nthawi iri yonse akadzudzulidwa, amanena kuti kukadakhala kopanda cifukwa cakuti cakuti sindikadacita cimenezi. [30]

Adamu ndi Hava atadya zipatso zokanizidwa zija anadzazidwa ndi manyazi ndi kuopsedwa. Poyamba anali kuganiza za kupeza mookanira coipa cawo, ndi kuti apulumuke ku ciweruzo coopsa ca imfa. Pamene Yehova anafunsa za cimo lao, Adamu anayankha, nakankhira coipaco mbali ina kwa Mulungu, mbali ina kwa mkazi wace: “Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya.” Mkazi anakankhira cimolo pa njoka nati, “Njoka inandinyenga ine, ndipo ndinadya.” (Gen. 3: 12, 13.) Mudaipangiranji njoka? Mudailoleranji kudzalowa mu Edene? Zimenezi ndizo zifunso anafunsa popeza mookanira cifukwa ca zoipa zace, coteru anali kuda Mulungu cifukwa ca kulephera kwawo. Mzimu wa kudziyesera yekha wolungama unayambidwa ndi atate wa bodza, ndipo uli kuonekere mwa ana onse a Adamu. Kubvomereza kotere si kocokera mwa Mzimu wa Mulungu, ndipo sikudzalandiridwa ndi Mulungu. Kulapa koon kudzamtso golera munthu kunyamula coipa cace yekha, ndi kucibvomereza wopanda cinyengo. Monga ngati wa msonkho uja, wosafuna ngakhale kuyang’ana maso ace kumwamba, adzapfuula, “Mulungu mundicitire cifundo ine wocimwa;” ndipo amene azindikira macimo awo adzayesedwa olungama, cifukwa Yesu adzapembedzera mwazi wace kuthangata moyo wolapa.

Zitsanzo za m’Mau a Mulungu za kulapa koon ndi kudzi-cepetsa zisonyeza mzimu wa kubvomereza kopanda kuzemba ucimo, kapena kudziyesera wolungama. Paulo sanafune kudzibisa yekha; iye afotokoza ucimo wace monga momwe uli, wosafuna kucepeta coipa cace. Iye ati: “Ndipo ndinatsekera ine oyera mtima am-

biri m'ndende, popeza ndinalandira ulamuliro wa kwa ansembe akulu; ndiponso pophedwa iwo ndinabvomerezapo. Ndipo ndinawalanga kawiri kawiri m' masunagoge onse, ndi kuwakakamiza anene za mwano; ndipo pakupsa mtima kwakukuru pa iwo ndinawalondalonda ndi kuwatsata ngakhale kufikira ku midzi ya kunja.” (Mac. 26: 10, 11.) Sazengereza ponena kuti “Kristu anadza m'dziko lapansi kupulumutsa ocimwa; mwa iwowa ine ndine woposa.” (ITim. 1: 15.)

Mtima wosweka ndi wodzicepetsa, wogonjetsedwa ndi kulapa koono, udzazindikira za cikondi ca Mulungu ndi mtengo wace wa mtanda; ndipo monga mwana amabvomereza kwa atate wokonda, coteru wolapa woona ad2abwera nazo zoipa zace zonse pamaso pa Mulungu. Ndipo kudalembedwa, “Ngati tibvomereza macimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti akatikhululukire macimo athu ndi kutisambitsa kuticotsera cisalungamo ciri conse.”

[31] (1 Yohane 1: 9.)

MUTU 5—KUDZIPEREKA

LONJEZANO la Mulungu liri lakuti, “Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.” (Yer. 29: 13.)

Mtima wonse udziperekedwa kwa Mulungu, titapanda kutero, kusintha sikungacitike mwa ife kumene kungatibwezere m’cifaniziro cace. Mwa cibadwidwe ife tinalekana ndi Mulungu. Mzimu Woyera ufotokoza makhalidwe athu ndi mau otere: “Akufa ndi zolakwa ndi zocimwa zanu;” “Mutu wonse uli kudwala, ndi mtima wonse walefuka;” “m’menemo mulibe cangwiro.” Ife tagwidwa mu msampha wa Satana; “M’menemo anagwidwa naye, ku cifuniro cace.” (Aefeso 2: 1; Yesaya 1: 5, 6; 2 Tim. 2: 26.) Mulungu afuna kuticiritsa ndi kutimasula ife. Koma popeza izi zifunika kusandulika kweni kweni, kukonzanso mkhalidwe wathu wonse, tiyenera kudzipereka athunthu kwa Iye.

Nkhondo yomenyana ndi cifuniro cathu ndiyo nkhondo yaikuru koposa zonse, Kudzipereka tokha, kupereka zonse ku cifuniro ca Mulungu, pafunika nkhondo; koma moyo udzigonjera Mulungu usanakonzedwe kukhala woyera.

Ufumu wa Mulungu, si wonga umene angauonetsere Satana, wokhazikika pa cigonjero ca khungu, ndi kulumulira kosayenera. Umadandaulira kwa anzeru ndi a cikumbumtima. “Tiyeni tsono, tiweruzane.” (Yesaya 1: 18), ndiko kuitana kwa Mlengi kwa anthu amene adawapanga. Mulungu sakakamiza cifuniro ca olengedwa ace. Iye sangathe kulandira cipembedzo cimene sicikokera mu mtima wofuna ndi wolola. Cigonjero cokakamiza cidzaletsa kukula kweni kweni kwa mtima kapena makhalidwe; cidzangomcititsa munthu ngati makina. Cimeneci siciri cifuniro ca Mlengi. Iye afuna kuti munthu, amene ali nchito yacifumu ya mphamvu yace ya kulenga, adzakule kwambiri monga angakhoze. Iye atiikira patsogolo pathu msinkhu wa dalitso umene afuna kuti tiufikire mwa cisomo cace. Iye atiitana ife kuti tidzipereke kwa Iye, kuti acite cifuniro cace mwa ife. Zatsalira ife kuti tisankhe ngati tifuna kumasulidwa

ku ukapolo wa zoipa, ndi kudzagawana nawo ufulu wa ulemerero wa ana a Mulungu.

[32] Pakudzipereka tokha kwa Mulungu, tiyenera kucotsa zonse
 zimene zingatilekanitse ndi Iye. Cifukwa cace Mpulumutsi ati,
 [33] “Cifukwa cace yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo sakhoza
 kukhala wophunzira wanga.” (Luka 14: 33.) Ciri conse ca kukoka
 mtima kuucotsa kwa Mulungu ciyenera kusiyidwa. Cuma ndilo
 fano la anthu ambiri. Cikondi ca pa ndalama, cilakolako ca cuma,
 ndiwo unyolo wa golidi umene umawamangirira kwa Satana. An-
 thu ena amapembedza kumveka ndi ulemu wa dziko lapansi. Fano
 la ena ndilo kufuna mtendere wa iwo okha ndi kupewa katundu
 wawo. Koma nsinga za ukapolozi ziyenera kudulidwa. Sitingathe
 kudzigawa pakati kukhala theka lina kwa Ambuye ndi theka lina ku
 dziko lapansi. Sitingathe kukhala ana a Mulungu ngati sitidzipereka
 athunthu kwa Iye. Alipo anthu amene amadziyesera kuti ali kutu-
 mikira Mulungu, pamene ali kukhulupirira mphamvu zawo kumvera
 malamulo a Mulungu, kupanga okha makhalidwe abwino, ndi ku-
 peza cipulumutso. Mitima yawo sigundidwa ndi nzeru zakuya za
 cikondi ca Kristu, koma afuna kugwira nchito za Cikristu, monga
 ngati kuti Mulungu amawauza kuti adzalowa kumwamba ndi nchito
 zawozo. Cipembedzo coteri cira cacabe. Pamene Kristu akhala mu
 mtima, moyo udzadzazidwa ndi cikondi cace, ndi cimwemwe ca
 kulankhula naye, koteri kuti udzaumirira kwa Iye; ndipo pa ku-
 ganizira za Iye, udzaiwala za kudzikonda wekha. Kukonda Kristu
 ndiko kudzakhale kasupe wa nchito zako. Iwo amene amva cikondi
 cokakamiza ca Mulungu, samafunsa kupereka zazing’ono pofuna
 kukwanitsa cifuniro ca Mulungu; samafunsa mbendela ya pafupi,
 koma amayang’anira ku muyeso wamphumphu wa cifuniro ca
 Mombolo wawo. Ndi cifuniro coona amapereka zonse, naonet-
 sera cikondwerero colingana ndi mtengo wa cinthu cimene iwo ali
 kufuna. Kungobvomereza Kristu wopanda cikondi cakuyaci, ndi
 kungolankhula cabe, cipembedzo couma, ndi nchito yotopetsa.

Kodi uli kuti nsembe ya kupereka zonse kwa Kristu yakulitsa?
 Tadzifunsa wekha cifunso ici, “Kodi Kristu anapereka ciani cifukwa
 ca ine?” Mwana wa Mulungu anapereka zonse — moyo, cikondi,
 ndi masautso—kutiombola ife. Kodi monga ifetu, anthu osayenera
 kulandira cikondi cacikuru coteri, ndi kukaniza kupereka mitima
 yathu kwa Iye? Kanthawi kali konse ka moyo wathu tiri kulandira

madalitso a cisomo cace, ndipo cifukwa ca ici sitingathe kuzindikira kokwana kukula kwace kwa zoopsa ndi cisoni ku zimene tapulumutsidwamo. Kodi tingamuyang'ane Iye amene anapyozedwa ndi zoipa zathu, ndiye tingokhalabe olola kudana ndi cikondi cace ndi nsembe yace? Pa kuyang'ana kudzicepetsa kosaleka kwa Ambuye wa ulemerero, kodi ife tidzang'ung'udza cifukwa tingathe kulowa m'moyo ndi kulimbana ndi kudzicepetsa tokha?

[34]

Cifunso ca mitima yambiri yonyada ndico, “Cifukwa ciani ndifunika kulapa ndi kudzicepetsa ndisanatsimikize kuti ndalandiridwa ndi Mulungu?” Ine ndikusonyeza kwa Kristu. Iye anali wosacimwa, ndipo koposa izi, anali Mfumu ya kumwamba; koma cifukwa ca munthu anayesedwa ucimo kupulumutsa mtundu wonse. “Ndipo anawerengedwa pamodzi ndi olakwa; koma ananyamula macimo a ambiri, napembedzera olakwa.” (Yesaya 53: 12.)

Kodi m'mene timapereka zonsemo, ndiye timapereka ciani? — Mtima wodetsedwa ndi zoipa kuti Yesu auyeretse, kuutsuka ndi mwazi wace, ndi kuupulumutsa ndi cikondi cace cosayerekezeka. Komabe anthu amaganiza kuti ncolimba kupereka zonse! Ndimacita manyazi pakumva anthu ali kuzilankhula, ndiponso ndiri kucita manyazi kuzilemba.

Mulungu safuna kuti ife tisiye cimene cingaticite ife ubwino wopambana ngati tingacisunge. M'zonse zimene Iye acita amayang'anira ubwino wa ana ace. Mulungu afuna kuti onse amene sanasankhe Kristu akadazindikira kuti Iye ali ndi zinthu zambiri zabwino za kuwapatsa iwo koposa zimene ali kudzifunira okha. Munthu ali kucita zosalungama ndi zopweteka zazikuru kwa moyo wace pamene ali kucita ndi kuganiza mosiyana ndi cifuniro ca Mulungu. Cimwemwe ceni ceni sicingapezeke m'njira yokanizidwa ndi Iye amene adziwa zomwe ziri zabwino kwa ife, ndi amene amakonza nzeru zabwino kwa olengedwa ace. Njira ya kuswa malamulo ndi njira ya cisoni ndi cionongeko.

Ndi kucimwa kuganiza kuti Mulungu amakondwera kuona ana ace ali kusautsidwa. Kumwamba konse kumakondwera ndi cimwemwe ca anthu. Atate wathu wa kumwamba samatseka njira za cimwemwe kwa wolengedwa wace ali yense. Malamulo a kumwamba amatiuza ife kuti tisiye zoipa zimene zimadzetsa masautso ndi matsoka, zimene zimatitsekera ife khomo la kumwamba ndi la cimwemwe. Mombolo wa dziko amalandira

anthu monga momwe ali, ndi zosowa zawo zonse, zosalungama zawo ndi zofooka zawo; ndipo sadzangowatsuka mu zoipa zokha ndi kuwapatsa ciombolo mwa mwazi wace, koma adzakwanitsa zokhumba-mtima za onse amene abvomera kubvala gori lace, ndi kunyamula katundu wace. Colinga cace ndico kupatsa mtendere ndi mpumulo kwa onse akudza kwa Iye kudzafuna mkate wa moyo. Iye afuna kuti ife tidzicita nchito zimene zingatsogolere mapazi athu ku madalitso a kumwamba amene anthu osamvera sangawalandire. Cimwemwe coona ca moyo ndiko kukhala ndi Yesu m'mitima yathu, amene ali ciyembekezo ca ulemerero.

[35]

Ambiri ali kufunsa, “Kodi ndidzipereka ndekha bwanji kwa Mulungu?” Iwe ufuna kuzipereka kwa Iye, koma uli wofooka mu mphamvu zako, ndiwe kapolo wa kukaika, ndi wolamulidwa ndi makhalidwe a moyo wako wocimwa. Malimbiko ako ndi malonjezano ako ali ngati zingwe za mcenga. Sungathe kulamulira maganizo ako, zofuna zako, cikondi cako. Podziwa kuti umaswa malonjezano ako, nulephera kucita zowinda zako zimafooketsa cilimbiko ca mwa iwe wekha, ndi kukuganizitsa kuti Mulungu sangathe kukulandira; koma usagwe mphwai. Cimene ufunika kuzindikira ndiyo mphamvu yoonadi ya cifuniro. Imeneyi ndiyo mphamvu yolamulira m'makhalidwe a munthu, mphamvu ya kusankha. Ciri conse catsamira pa kucita bwino kwa cifuniro. Mphamvu ya kusankha, Mulungu anaipereka kwa anthu, kuti adzicita nayo. Iwe sungathe kusintha mtima wako, sungathe mwa iwe wekha kupereka cikondi cace kwa Mulungu; koma ungate kusankha kumtumikira Iye. Ungathe kumpatsa Iye cifuniro cako; pompo adzagwira nchito mwa iwe kufuna ndi kucita komwe monga mwa cikondwerero cace. Potero makhalidwe ako onse adzakhala mu ulamuliro wa Mzimu wa Kristu; cikondi conse cidzakhala mwa Iye, maganizo ako adzakhala ogwirizana ndi Iye.

Kulakala kucita zabwino ndi kuyera mtima ndi kwabwino; koma ngati ungolekera pompo, sizidzapindula kanthu. Ambiri adzataika kwina ali kuyembekeza ndi kufuna kukhala Akristu. Safikira pa kupereka cifuniro cawo kwa Mulungu. Sali kusankhiratu tsopano kukhala Akristu.

Utacita naco bwino cifuniro cako, moyo wako ungate kusinthika kweni kweni. Pa kupereka cifuniro cako kwa Kristu, uli kudzilumikiza wekha ndi mphamvu ya kuposa maukulu onse ndi

maufumu. Udzalandira mphanvu zocokera kumwamba za kukulimbitsa, ndipo potero, pakudzipereka tsiku ndi tsiku kwa Mulungu, udzakhoza kukhala moyo watsopano, moyo wa cikhulupiriro.

[36]

[37]

MUTU 6—CIKHULUPIRIRO NDI KULANDIRIDWA

PAMENE cikumbumtima cako cadzutsidwa ndi Mzimu Woyera, waona kuipa kwa ucimo, mphamvu yace, kutsutsidwa kwace, tsoka lace; ndipo umaayang'ana ndi kunyansidwa nawo. Umadziwa kuti ucimo udakulekanitsa ndi Mulungu, kuti uli mu ukapolo wa zoipa. M'mene uli kulimbika kudzipulumutsa wekha, momwemo udzazindikira kuti ulibe mphamvu ya kudzithangata wekha. Maganizo ako ali osayera, mtima wako uli wonyansa. Iwe uona kuti mtima wako unadzazidwa ndi kudzikonda wekha ndi zoipa. Ufuna kukhululukidwa, kutsukidwa, ndi kumasulidwa. Ufuna kuyanjana ndi Mulungu, ndi kufanana naye, — nanga ungacite ciani kulandira zonsezi?

Usowa mtendere, — cikhululukiro ca Mulungu, ndi cikondi m'moyo mwako. Sungathe kuzigula ndi ndalama, sungathe kuzipeza ndi nzeru zako; sungayembekeze kuzipeza, ndi kuyesa kwako kokha. Koma Mulungu angokupatsa kwaulere, “opanda ndalama ndi wopanda mtengo.” (Yesaya 55: 1.) Zonsezi zidzakhala zako ngati ungangotambasula manja ako ndi kuzilandira. Yehova ati, “Ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi zidzakhala ngati ubweya wa nkhusa woti mbu.” (Yesaya 1: 18.) “Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mzimu watsopano.” (Ezek. 36: 26.)

Udabvomereza zoipa zako, ndi kuzicotsa mu mtima mwako. Udatsimikiza mtima kudzipereka kwa Mulungu. Tsopano pita kwa Iye, ndi kumpempha kuti atsuke zoipa zako, nakupatse mtima watsopano. Pompo khulupirira kuti adzakucitira izi cifukwa adalonjeza. Limeneli ndilo phunziro limene Yesu anaphunzitsa pamene anali pa dziko lapansi, kuti mphatso imene Mulungu adalonjeza, ife tidzikhulupirira kuti talandira, ndipo idzakhala yathu. Yesu anaciritsa anthu nthenda zawo pamene iwo anali kukhulupirira mphamvu yace; Iye anawathangata m'zinthu zimene anali kuziona, motero anali kumkhulupirira Iye m'zinthu zimene sanali kuziona,

— nawatsogolera kukhulupirira mphamvu yace ya kukhululukira zoipa. Izi ananena momveka pa kuciritsa munthu wodwala manjenje: “Koma kuti mudziwe kuti ali nazo mphamvu Mwana wa munthu pansi pano za kukhululukira macimo (pomwepo ananena kwa wodwalayo), Tanyamuka, nutenge chika lako, numuke ku nyumba kwako.” (Mateyu 9: 6.) Coteronso Yohane mlalikiyo ati, pakunena za zozizwitsa za Yesu, “Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupirira mukakhale nawo moyo m’dzina lace.” (Yohane 20: 31.)

[38]

Mu nthano zofewa za m’Bible zofotokoza m’mene Yesu anaciritsira odwala, tingaphunziremo kukhulupirira Iye kwa cikhululukiro ca macimo athu. Tiyeni titaona nthano ya wodwala wa pa Betesda uja. Iye anali wosatha kudzithangata; sanagwire nazo nchito ziwalo zace zaka makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatatu. Koma Yesu anamuuza iye, “Uka, yalula mphasa yako, nuyende.” Wodwalayo akadafuna akadati, “Ambuye, ngati mungandiciritse ndidzamvera mau anu.” Koma ai, iye anakhulupirira mau a Kristu, anakhulupirira kuti waciritsidwa, ndipo anayesa msanga; iye anafuna kuyenda, ndipo anayendadi. Iye anacita pakumva mau a Kristu, ndipo Mulungu anampatsa mphamvu. Ndipo iye anaciritsidwa.

Monga momwemo iwe ndiwe wocimwa. Sungathe kupembedzera zoipa zako zam’mbuyo, sungathe kusintha mtima wako, ndi kudziyeretsa wekha. Koma Mulungu analonjeza kukucitira zonsezi mwa Kristu. Iwe ukhulupirira lonjezanolo. Nubvomereza zoipa zako, ndi kudzipereka kwa Mulungu. Iwe nufuna kumtumikira. Ngati iwe ungacitedi zimenezi, Mulungu adzakwanitsa mau ace kwa iwe. Ngati ukhulupirira lonjezanolo, — khulupirira kuti wakhululukidwa ndi kutsukidwa, — Mulungu adzakucitira; waciritsidwa, monga momwe Kristu anapatsira mphamvu wodwala uja kuyenda pamene anakhulupirira kuti waciritsidwa. Zidzatero ngati iwe ukhulupirira.

Usalindire kuti uyambe wamva kuti waciritsidwa, koma nena kuti, “Ndikhulupirira; ndi zoonna, sicifukwa ca kuti ndamva, koma cifukwa ca kuti Mulungu adalonjeza.

Yesu ati, “Zinthu ziri zonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira ndipo mudzakhala nazo.” (Marko 11: 24.) Pali malandiridwe ace a lonjezano limeneli, — kuti tipem-

phere monga mwa cifuniro ca Mulungu. Koma Mulungu afuna kutitsuka ife mu zoipa zathu, kutiyesa ana ace, ndi kutithangata ife kukhala moyo woyera.

[39] Coteru ife tidzipempha madalitso amenewa, ndi kukhulupirira kuti tawalandira, ndi kuthokoza Mulungu kuti tawalandira. Ndi mwai wathu kunka kwa Yesu ndi kukatsukidwa, ndi kuima patsogolo pa malamulo opanda manyazi kapena cisoni. “Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa, amene sayenda monga mwa thupi koma monga mwa Mzimu.” (Aroma 8: 1.)

Cifukwa cace simuli a inu nokha; mudagulidwa ndi mtengo wapatari. “Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva,... koma ndi mwazi wa mtengo wace wapatari, monga wa mwana wa nkhosa wopanda cirema ndi wopanda banga.” (1 Pet. 1: 18, 19.) Ndi nchito ya pafupiyi ya kukhulupirira Mulungu, Mzimu Woyera walenga moyo watsopano mu mtima mwako. Ndiwe monga mwana wobadwa m’banja la Mulungu, ndipo akukonda iwe monga akonda Mwana wace. Popeza wadzipereka kwa Yesu, usabwerere m’mbuyo, usadzicotse kwa Iye, koma tsiku ndi tsiku nena, “Ndine wa Kristu; ndinadzipereka kwa Iye;” ndi kumpempha Iye kukupatsa Mzimu wace, ndi kukusunga ndi cisomo cace. Popeza usanduka mwana wace pakudzipereka kwa Mulungu, ndi kukhulupirira Iye, coteru uyenera kukhala mwa Iye. Mtumwi ati, “Cifukwa cace monga munalandira Kristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye.” (Akolose 2: 6.)

Ena amaoneka ngati afuna kuyamba kuyesedwa ndi kudzisonyeza kwa Yehova kuti akonzeka, asanapemphe dalitso lace. Koma ayenera kupempheratu dalitso la Mulungu tsopano lino. Ayenera kulandira cisomo cace, Mzimu wa Kristu, kuwathangata m’zofooka zawo, atapanda kuteru sangathe kukaniza zoipa. Yesu akonda kuti ife tidze kwa Iye monga momwe tiri, ocimwa, osowa cithangato, osatha kucita kanthu mwa ife tokha. Tidze ndi zofooka zathu zonse, kupusa kwathu, kucimwa kwathu, ndi kugwa pa mapazi ace ndi kulapa. Ndi ulemerero wace kutifukata m’mikono yace ya cikondi, ndi kumanga mabala athu, ndi kutitsuka ku zoipa zonse.

Anthu ambiri amalepherera apa: sakhulupirira kuti Yesu amawakhulukira ali yense pa yekha. Sakhulupirira mau a Mulungu. Iwo amene ayanjana ndi macitidwe ace ayenera kudziwa kuti

cikhululukiro ciripo cokwana kwa cimo liri lonse. Cotsani ganizo la kuti malonjezano a Mulungu sali anu. Iwo ali a wocimwa ali yense amene alapa. Mphamvu ndi cisomo kupyolera mwa Kristu zimadza ndi angelo otumikira kwa munthu ali yense wa kukhulupirira. Palibe ena amene ali ocimwa kwambiri kotero kuti sangathe kupiza mphamvu, kuyera mtima, ndi cilungamo mwa Yesu, amene anawafera. Iye ali kulindira kuwabvula zobvala zawo zodetsedwa ndi zoipa, ndi kuwabveka zobvala zoyera za cilungamo; Iye awauza kuti akhale ndi moyo, asafe.

Mulungu samaticitira ife monga amacitirana anthu. Maganizo ace ndi maganizo a cifundo, a cikondi ndi a cisomo. Iye ati, “Woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamcitira cifundo, ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa.” “Ine ndafafaniza monga mtambo wocindikira zolakwa zako, ndi monga mtambo macimo ako.” (Yesaya 55: 7; 44: 22.)

[40]

“Pakuti sindikondwera nayo imfa ya wakufayo, ati Ambuye Yehova; cifukwa cace bwererani, nimukhale ndi moyo.” (Ezek. 18: 32.) Satana ali wofulumira kuba citsimikizo codala ca Mulungu. Iye afuna kucotsa kacyembekezo kali konse ndi kamuuni kali konse m’moyo; koma iwe usamulole kucita izi. Usamvere woyesayo, koma nena: “Yesu anafa kuti ine ndikhale ndi moyo. Iye andikonda ine, ndipo safuna kuti ndionongeke. Ndiri naye Atate wa kumwamba wa cifundo; ndipo ngakhale ndinanyoza cikondi cace, ngakhale ndinapeputsa madalitso ace, ndidzauka, ndipite kwa Atate wanga ndipo ndidzanena naye, ‘Ndinacimwira Kumwamba ndi pa maso panu, ndipo sindiri woyeneranso konse kuchulidwa mwana wanu: muniyese ngati mmodzi wa anchito anu. ’” Fanizoli likufotokozerani m’mene wosocera ati adzalandiridwire: “Pamene iye akali kutari, atate wace anamuona iye, ndipo anamva naye cifundo, nathamanga, nagwa pa khosi pace, namsomsonetsa iye.” (Luka 15: 18-20.)

Koma ngakhale fanizo limeneli, lomvetsa cisoni monga momwe lirimu, silingathe kufotokoza kokwana cifundo cosatha ca Atate wa kumwamba. Yehova anena mwa mneneri wace, “Ndakukonda iwe ndi cikondi cosatha: cifukwa cace ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima.” (Yer. 31: 3.) Wocimwa akali kutari ndi nyumba ya Atate, ali kungoononga cuma cace m’dziko la cilendo, mtima wa Atate uli

kumdandaulira iye; ndipo cilakolako ciri conse m’ moyo ca kubwerera kwa Mulungu, ndiwo madandaulo a Mzimu Woyera, kubwezera wocimwayo ku mtima wa cikondi wa Atate wace.

Ndi malonjezano olemera cotere a Baibulo patsogolo pako, kodi uli kukaikabe? Kodi uli kukhulupirira kuti pamene munthu wocimwa afuna kubwerera, nafuna kusiya zoipa zace, Yehova adzamkaniza iye kudza pa mapazi ace ali kulapa? Cotsa maganizo otero! Palibe kanthu kena kangapweteke mtima wako koposa kuganiza maganizo otere za Atate wathu wa kumwamba. Iye amadana ndi zoipa, koma amakonda wocimwa, ndipo anadzipereka yekha mwa Kristu, kuti onse amene afuna apulumutsidwe; nadzakhala nawo madalitso osatha mu ufumu wa ulemerero. Kodi akadanena cotani koposa m’mene adaneneramu pa kutsimikiza cikondi cace kwa ife? Iye ati, “Kodi mkazi angaiwale mwana wace wa pabere, [41] kuti sangacitire cifundo mwana wombala iye? inde, awa angaiwale, koma ine sindingaiwale iwe.” (Yesaya 49: 15.)

Yang’anani kumwamba, inu amene muli kukaika ndi kunthunthumira; cifukwa Yesu ali ndi moyo kutipembedzera ife. Thokozani Mulungu cifukwa ca mphatso ya Mwana wace wokondedwa, ndi kupemphera kuti Iye asangokuferani kwacabe. Mzimu ali kukuitanani lero. Idzani ndi mtima wanu wonse kwa Yesu, ndipo mufunse madalitso ace.

Pamene muwerenga malonjezanowo, kumbukirani kuti ndiwo citsimikizo ca cikondi ndi cifundo cosaneneka. Mtima waukuru wa Cikondi Cosatha umakokedwa kwa wocimwa ndi cifundo cosatha. “Tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wace, cikhululukiro ca zocimwa.” (Aefeso 1: 7.) Inde, ingokhulupirani kuti Mulungu ndiye mthangati wanu. Iye afuna kubwezera cifanizo cace colungama mwa munthu. Pamene muyandikira cifupi ndi Iye, pakubvomereza ndi [42] kulapa, adzayandikira kwa inu ndi cifundo ndi cikhululukiro.

[43]

MUTU 7—YESO LA KUKHALA WOPHUNZIRA WA YESU

“Ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano: zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano.” (2 Akor. 5: 17.)

Kapena munthu sangadziwe nthawi yace kapena malo ace, kapena kulondola zonse m’nchito ya kutembenuka; koma zimenezi sizisonyeza kuti munthuyo sanatembenuke. Kristu anati kwa Nikodemo, “Mphepo iwomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ace, koma sudziwa kumene icokera, ndi kumene imuka; coteru ali yense wobadwa mwa Mzimu.” (Yohane 3: 8.) Monga mphepo imene iri yosaoneka, koma nchito zace zioneke bwino lomwe, coteronso Mzimu wa Mulungu pogwira nchito yace mu mtima wa munthu. Mphamvu ya kulenganso, imene sioneke ndi maso a munthu, imabala moyo watsopano mu mtima; imalenga munthu watsopano m’cifaniziro ca Mulungu. Ngakhale nchito ya Mzimu iri yacete ndi yosaoneka, nchito zace zimaonekera. Ngati mtima wakonzedwa ndi Mzimu wa Mulungu, makhalidwe a munthuyo adzagitira mboni. Ngakhale sitingathe kusintha mitima yathu, kapena kudziyanjanitsa tokha ndi Mulungu; ngakhale sitiyenera kudzikhulupirira tokha kapena nchito zathu zabwino, miyoyo idzaonetsera ngati cisomo ca Mulungu ciri mwa ife. Kusintha kudzaoneka m’makhalidwe ndi m’macitidwe athu. Kusiyana kudzaoneka bwino pakati pa zimene anali kucita ndi zimene ali kucita tsopano. Makhalidwe amaonekera, osati ndi nchito zabwino zocitika kamodzi kamodzi, kapenandi nchito zoipa zocitika kamodzi kamodzi, koma ndi mau olankhulidwa masiku onse ndi nchito za masiku onse.

Ndi zoonadi kuti munthu angathe kusonyeza makhalidwe abwino kunja kwace, wopanda mphamvu ya kulenganso ya Kristu. Kukonda citsanzo cabwino, ndi cifuniro ca kulemekeza ena zingampatse munthu makhalidwe olongosoka. Kudzicitira tokha ulemu kungatitsogolere ife kupewa maonekedwe a coipa. Mtima wa dyera

ungathe kupatsa mofewa manja. Nanga tsono, tidzadziwa ndi ciani mwini wace wa mbali imene ife taima?

[44] Ndani ali ndi mitima yathu? Maganizo athu ali ndi yani? Timakonda kulankhula za yani? Ndani watenga cikondi cathu copambana ndi nchito zathu zopambana? Ngati tiri a Kristu, maganizo athu adzakhala ndi Iye, tidzaganiza za Iye kopambana. Zonse zomwe tiri nazo ndi ife tomwe eni ace zidzaperekedwa kwa Iye. Tidzalakalaka kunyamula cifanizo cace, kupuma mzimu wace, kucita cifuniro cace, ndi kumkondweretsa Iye m'zinthu zonse.

Iwo amene asanduka olengedwa atsopano mwa Kristu Yesu adzabala zipatso za Mzimu, “Cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso.” (Agalatiya 5: 22, 23.) Sadzadzilinganzanso ndi zilakolako za kale, koma ndi cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu iwo adzatsata mapazi ace, adzaonetsera makhalidwe ace, nadziyeretsa okha monga Iyeyo ali woyera. Zinthu zomwe akadana nazo kale, azikonda tsopano; ndipo zomwe anali kukonda kale, adana nazo tsopano. Onyada ndi odzikuza amasanduka ofatsa ndi odzicepetsa mtima. Oledzera amasanduka odziletsa, Oipitsitsa amasanduka angwiro. Miyambo ndi mafano a dziko zasiyidwa. Akristu sadzafuna “kukometsera kwa kunja,” koma “munthu wobisika wa mtima, m'cobvala cosaola ca mzimu wofatsa ndi wacete.” (1 Pet. 3: 3, 4.)

Kulibe umboni wa kulapa ngati sikugwira nchito ya kukonzanso. Ngati wabweza cowinda cace, ngati wabweza comwe adaba, ngati wabvomereza zoipa zace, ndi kukonda Mulungu ndi anthu anzace, wocimwayo azindikire kuti wacokera ku imfa kulowa m'moyo.

Pamene ife, anthu ocimwa, tidza kwa Kristu, tikhala olandirana nawo cisomo cace cokhululukira, cikondi cimadzaza mu mtima. Katundu aliyense amapepuka; cifukwa gori la Kristu liri lofewa. Nchito imakhala cikondwererero nsembe nikhala yokondeweretsa. Njira imene kale inali kuoneka ya mdima, imasanduka yowala ndi dzuwa la cilungamo.

Cikondi ca makhalidwe a Kristu cidzaoneka mwa akuphunzira ace. Cinali cikondwerero cace kucita cifuniro ca Mulungu. Kukonda Mulungu, cangu ca ulemerero wace, ndizo zinali mphamvu yolamulira m'moyo mwa Mpulumutsi. Cikondi cinakometsa ndi kulemekeza nchito zace zonse. Cikondi ciri ca Mulungu. Mtima wosapatulidwa sungathe kucionetsera. Cimapezeka mu mtima m' mene

Yesu alamulamo. “Tikonda ife, cifukwa anayamba Iye kutikonda.” (1 Yohane 4: 19.) Mu mtima umene unatsukidwa ndi cisomo ca Mulungu, cikondi ndilo tsinde la nchito. Cimakonza makhalidwe, cimalamulira maganizo, cimagonjetsa udani, ndi kukulitsa cikondano. Cikondi cimeneci cikakhala m’moyo, cimaukometsa, nicipereka cikoka cabwino ponse pozungulira.

[45]

Ziripo zoipa ziwiri zimene ayenera kuzipewa ana onse a Mulungu — makamaka iwo amene adza tsopano m’cisomo cace. Coyamba ndi comwe tafotokoza kale cija, ca kuyang’ana nchito zawo, kukhulupirira zomwe iwo angathe kucita, kudziyanjanitsa okha ndi Mulungu. Iye amene afuna kudziyeretsa yekha ndi nchito zace pa kusunga malamulo, ali kuyesa kucita cinthu cosatheka. Zonse zimene munthu angacite wopanda Kristu zimaonongeka ndi dyera ndi ucimo. Cingathe kutiyeretsa ife ndi cisomo ca Kristu cokha mwa cikhulupiriro.

Coipa caciwiri cosiyana, koma coopsanso, ndico cikhulupiriro ca kuti Kristu amamasula anthu kuti asamasunga malamulo a Mulungu; kuti popeza tidzalandira cisomo ca Kristu ndi cikhulupiriro cokha, nchito zathu ziribe kanthu ndi ciombolo cathu.

Koma zindikirani kuti kumvera si maonekedwe a kunja kokha, koma nchito ya cikondi. Malamulo a Mulungu ali citsimikizo ca makhalidwe ace; iwo ali citsimikizo ca cikondi cace, cifukwa cace ali maziko a ufumu wace m’mwamba ndi pa dziko lapansi. Ngati mitima yathu yakonzedwa m’cifaniziro ca Mulungu, ngati cikondi ca Mulungu, cadzalidwa mu mtima, kodi malamulo a Mulungu sadzacitika m’moyo mwace? Pamene maziko a cikondi adzalidwa mu mtima, pamene munthu akonzedwa monga mwa cifaniziro ca Iye amene anamlenga, lonjezano la cipangano catsopano likwanitsidwa “Ndidzapereka malamulo anga akhale pa mtima pawo, ndipo pa nzeru zawo ndidzawalemba.” (Heb. 10: 16.) Ndipo ngati malamulo alembedwa mu mtima, kodi sadzakonza moyo? Kumvera — nchito za cikondi — ndico cizindikiro coona ca kukhala wakuphunzira wa Yesu. Motero malembo anena, “Cikondi ca Mulungu ndi ici, kuti tisunge malamulo ace.” Iye wakunena kuti, ndimdziwa Iye, koma wosasunga malamulo ace ali wabodza, ndipo mwa iye mulibe coonadi.” (1 Yohane 5: 3; 2: 4.) M’malo mwa kummasula munthu kuti asamamvera, ndi cikhulupiriro cokha cimene cimatilandiritsa ife cisomo ca Kristu, cimene cimathithetsa ife kukhala omvera.

[46] Sitimalandira cipulumutso cifukwa ca kumvera kwathu, cifukwa cipulumutso ndi mphatso yaulere ya Mulungu, yolandiridwa mwa cikhulupiriro. Koma kumvera ndico cipatso ca cikhulupiriro. “Ndipo mudiwa kuti Iyeyu anaonekera kudzacotsa macimo; ndipo mwa Iye mulibe cimo. Yense wakukhala mwa Iye sacimwa; yense wakucimwa sanamuona Iye, ndipo sanamdziwa Iye.” (1 Yohane 3: 5, 6.) Nali yeso loona. Ngati tikhala mwa Kristu, ngati cikondi ca Mulungu cikhala mwa ife, maganizo athu, nchito zathu, zidzagwirizana ndi cifuniro ca Mulungu monga ciri kufotokozedwa m’ malamulo ace oyera. “Tiana, munthu asasokeretse inu; iye wakucita colungama ali wolungama, monga Iyeyu ali wolungama.” (1 Yohane 3: 7.) Cilungamo cifotokozedwa ndi mbendera ya malamulo oyera a Mulungu, ndiwo malamulo khumi operekedwa pa Sinai.

Cikhulupiriro ca mwa Kristu cimene anthu amanena kuti cimawamasula anthu kuti asamamvera Mulungu, si cikhulupiriro, koma ciyerekezo. “Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo ca kucita mwa cikhulupiriro.” Koma “cikhulupiriro cikapanda kukhala nazo nchito cikhala cakufa m’kati mwacemo.” (Aefeso 2: 8; Yakobo 2: 17.) Yesu anati za Iye yekha asanadze ku dziko lapansi. “Kucita cikondwero canu kundikonda, Mulungu wanga, ndipo malamulo anu ali m’kati mwa mtima mwanga.” (Salmo 40: 8.) Ndipo asanakw-erenso kumwamba Iye anati, “Monga Ine ndasunga malamulo a Atate wanga ndipo ndikhala m’cikondi ca. ce.” (Yohane 15: 10.) Malembo ati, “Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ace.... Iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayen-eranso mwini wace kuyenda monga anayenda Iyeyo.” (1 Yohane 2: 3-6.) “Pakutinso Kristu anamva zowawa m’ malo mwanu, nakusiyi-rani citsanzo kuti mukalondole mapazi ace.” (1 Pet. 2: 21.)

Makhalidwe a moyo wosatha ali cimodzimidzi tsopano monga anali masiku onse, —monga anali m’Paradaiso makolo athu oyamba asanacimwe, — omvera malamulo a Mulungu, cilungamo cangwiro. Ngati malandiridwe a moyo wosatha akadacepa kusiyana ndi awa, pompo cimwemwe ca maiko onse a kumwamba cikadakhala m’zoopsa. Njira ya ucimo ikadatseguka, pamodzi ndi tsoka ndi zisoni zace zonse zopanda malekezere.

Cinali cotheka kwa Adamu, asanagwe, kupanga makhalidwe olungama pa kumvera malamulo a Mulungu. Koma analephera kucita izi, ndipo cifukwa ca ucimo wace makhalidwe athu analephera,

ndipo ife sitingathe kudzilungamitsa tokha. Popeza ndife ocimwa, osayera mtima, sitingathe kumvera malamulo oyera. Tiribe cilungamo ca ife eni coti tingathe kukwanitsa naco malamulo a Mulungu. Koma Kristu anatipangira ife njira yopulumukira. Iye anakhala pa dziko lapansi pakati pa mayeso onga timakomana nawo ife. Iye anakhala moyo wosacimwa. Iye anatifera ife, ndipo tsopano Iye afuna kutenga zoipa zathu ndi kutipatsa ife cilungamo cace. Ngati udzipereka kwa Iye, ndi kumlandira Iye ngati Mpulumutsi wako, pompo, ngakhale moyo wako uli woipa kwambiri, cifukwa ca Iye udzayesedwa wolu- ngama. Makhalidwe a Kristu aima m'malo mwa makhalidwe ako, ndipo ulandiridwa pamaso pa Mulungu ngati sunacimwa konse.

[47]

Koposa izi Kristu amasintha mtima. Amakhala mu mtima mwako mwa cikhulupiriro. Udzalumikizana ndi Kristu mwa cikhulupiriro ndi pa kupereka cifuniro cako kwa Iye kosalekeza; ndipo monga momwe ucita izi, adzacita mwa iwe kufuna ndi kucita komwe monga mwa cifuniro cace cokoma. Cotero mudzakena, “Moyo umene ndiri nawo tsopano m'thupi, ndiri nawo m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda ine, nadzipereka yekha cifukwa ca ine.” (Galatiya 2: 20.) Yesu ananena coteri kwa ophunzira ace, “Pakuti wolankhula si ndinu, koma Mzimu wa Atate wanu akulankhula mwa inu.” (Mateyu 10: 20.) Pompo, Kristu ali kugwira nchito mwa inu, mudzaonetsa mzimu umodzimidzi, mudzacita nchito zimodzimidzi. — nchito za cilungamo, za kumvera.

Conco tiribe kanthu mwa ife tokha kakudzitamandira. Palibe podzikuzira tokha. Ciyembekezo cathu ciri m'cilungamo ca Kristu cowerengedwa kwa ife, cocitika ndi Mzimu wace wakucita mwa ife.

Kulipo kusiyana kumene tiyenera kukumbukira pamene ife tilankhula za cikhulupiriro. Ciripo cikhulupiriro ca mtundu wina. Zakuti Mulungu alipo, ndi mphamvu, ndi coonadi ca mau ace, zimenezi ndi zoonza zimene ngakhale Satana ndi amithenga ace sangathe kuzikana m'mitima yawo. Bible ati kuti “Ziwandanso zikhulupirira ndipo zinthunthumira.” (Yakobo 2: 19.) Koma ici si cikhulupiriro.

Kumene si kuli cikhulupiriro congokhulupirira M'Mau ace okha, koma kupereka cifuniro kwa Iye; kumene mtima umaperekedwa kwa Iye, cikondi cimangirira pa Iye, kumeneko ndiko kuli cikhulupiriro,

— cikhulupiriro cimene cimagwira nchito mwa cikondi, ndi kuy-eretsa moyo. Ndi cikhulupiriro cimene mtima umakonzedwa m’cifaniziro ca Mulungu. Ndipo mtima umene m’makhalidwe ace osakonzedwa sugonja ku malamulo a Mulungu, pakuti ndithu sungathe kutero, tsopano umakondwera m’malamulo ace, nunena pamodzi ndi Davide, “Ha! Ndikondadi cilamulo canu; ndilingiriramo ine tsiku lonse.” (Salmo 119: 97.) Ndipo cilungamo ca lamulo cikwanitsidwa mwa ife, “amene sitiwendayenda monga mwa thupi koma monga mwa Mzimu.” (Aroma 8: 4.)

[48] Alipo ena amene adadziwa cikondi cokhululukira ca Kristu, ndi amene alakalakadi kukhala ana a Mulungu, koma nazindikira kuti makhalidwe awo sali angwiro, moyo wawo uli ndi zifukwa zambiri, ndipo ali ofulumira kukaika ngati kapena mitima yawo yakonzedwa ndi Mzimu Woyera kapena ai. Kwa oterewa ine ndinena, Musabwerere m’mbuyo ndi kulephera. Kawiri kawiri tidzigwada pansu ndi kulira pa mapazi a Yesu cifukwa cakupelewerwa kwathu ndi zolakwa zathu; koma tisagwe mphwayi. Ngakhale tagonjetsedwa ndi mdaniyo, sitinatayidwe ai, Mulungu sanatikane. Iai, Kristu ali pa dzinja la manja la Mulungu, amenenso amatipembedzera ife. Anatero Yohane wokondedwayo, “Zinthu izi ndakulemberani kuti musacimwe. Ndipo akacimwa wina Mnkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama.” (1 Yohane 2: 1.) Ndipo musaiwale mau a Kristu, “Pakuti Atate yekha akonda inu.” (Yohane 16: 27.) Iye afuna kukubwezerani kwa Iye yekha, kuti aone ungwiro ndi kuyera kwace kuli kuonekera mwa inu. Ndipo ngati mudzipereka nokha kwa Iye, Iye amene adayamba nchito yabwino mwa inu adzaicitabe kufikira tsiku la Yesu Kristu. Pempheperani ndi mtima wonse; khulupirirani kolimba. Popeza sitikhulupirira mphamvu yathu, tiyeni tikhulupirire mphamvu ya Mombolo wathu, ndipo tidzamtamanda Iye amene ali thanzi la nkhope zathu.

Ngati udza cifupifupi ndi Yesu udzaoneka wocimwa kwambiri m’maso mwa iwe wekha; cifukwa masomphenya ako adzakhala angwiro, ndipo zonyansa zako zidzaoneka bwino lomwe polinganiza ndi makhalidwe ace angwiro. Umenewu ndi umboni kuti macenjerero a Satana ataya mphamvu yawo; ndi kuti cikoka ca mphamvu ya Mzimu wa Mulungu ciri kukudzutsa iwe.

Cikondi ca kuya ca Kristu sicingakhale mu mtima umene suzindikira zoipa zace. Moyo umene usinthidwa ndi cisomo ca

Kristu, udzatamanda makhalidwe opatulika a umulungu wace; koma ngati sitiona zofooka zathu, ndiwo umboni wokwana kuti ife siti-naone ubwino ndi ukuru wa Kristu.

Ngati sitidzitamanda mwa ife tokha, tidzatamanda ungwiro ndi cikondi cosatha ca Mpulumutsi wathu. Tikaona zoipa zathu, tidzathamangira kwa Iye amene angathe kukhululukira; ndipo pamene moyo utazindikira kusowa mphamvu kwace, nufuna Kristu, adzadzionetsera yekha mu mphamvu. Tikazindikira kusowa kwathu tidzathamangira kwa Iye ndi ku Mau a Mulungu, ndipo tidzaona koposa makhalidwe ace, ndipo tidzaonetsera cifaniziro cace kokwana.

[49]

MUTU 8—KUKULA KUFANANA NDI KRISTU

Kusinthika kwa mtima kumene timasanduka nako ana a Mulungu, m’Bible kumalankhulidwa ngati kubadwanso. Ndiponso kumalankhulidwa ngati kumera kwa mbeu yabwino yodzalidwa ndi tsamunda. Monga momwemo iwo amene atembenukira kwa Kristu ali “monga makanda a lero,” kuti “akakule” (1 Petro 2: 2; Aefeso 4: 15) ku msinkhu wa amuna ndi akazi mwa Kristu Yesu. Kapena monga mbeu yabwino yofesedwa m’ munda, iwo ayenera kukula ndi kubala zipatso. Yesaya ati kuti iwo “adzachedwa mitengo ya cilungamo, yakuioka Yehova, kuti alemekezedwe.” (Yesaya 61: 3.) Coteru m’ moyo wa cilengedwe, mumatengedwa mafanizo, kutithangata ife kumvetsetsa cinsinsi ca coonadi ca moyo wa uzimu.

Nzeru ndi luso la munthu sizingathe kupereka moyo ngakhale kwa kanthu kakang’ono mwa cilengedwe. Nyama kapena mtengo zingathe kukhala ndi moyo kupyolera mwa moyo umene Mulungu anaupereka. Coteru moyo wa uzimu umabadwa m’ mitima ya anthu, kupyolera mwa moyo wocokera kwa Mulungu. Ngati munthu “sabadwa kucokera kumwamba” (Yohane 3: 3), sangathe kulandira moyo umene Kristu anadzaupereka.

Monga ndi moyo, coteronso ndi kukula. Ndi Mulungu amene amaturutsa mphundu nabalitsa maluwa zipatso. Mbeu imakula ndi mphamvu yace, “uyamba mmera, zitsata ngala, pamenepo maso okhwima m’ngala’mo.” (Marko 4: 28.) Ndipo mneneri Hoseya ati za a Israyeli kuti, “adzacita maluwa ngati kakombo.” “Adzatsit-simuka ngati tirigu, nadzaphuka ngati mpesa.” (Hoseya 14: 5, 7.) Ndipo Yesu atiuza “Lingalirani maluwa, makulidwe awo.” (Luka 12: 27.) Mitengo ndi maluwa sizimakula ndi cisamaliro cawo, kapena kudera nkhawa kwawo, kapena ndi kuyesa kwawo, koma pa kulandira zimene Mulungu adazipereka za kutumikira moyo wawo. Mwana sangathe ndi nkhawa zace kapena mphamvu zace, kuonjezera msinkhu wace. Ngakhale inunso, ndi nkhawa zanu kapena kuyesa mwa inu nokha simungathe kukula mwa uzimu. Mtengo, mwana, zimakula pa kulandira zimene zimatumikira moyo wawo,

— mpweya, dzuwa, ndi cakudya. Cimene zimacita mphatso za cilengedwezi kwa nyama ndi mitengo, ndizo amacita Kristu kwa iwo amene akhulupirira Iye. Iye ndiye “Kuunika kwawo kosatha,” “dzuwa ndi cikopa.” (Yesaya 60: 19; Salmo 84: 11.) Iye “adzakhala kwa Israyeli ngati mame.” “Iye adzatsika monga mvula pa maudzu.” [50] (Hoseya 14: 5; Salmo 72: 6.) Iye ndiye madzi a moyo. “Mkate [51] wa Mulungu... wotsika kumwamba, ndi kupereka moyo ku dziko lapansi.” (Yohane 6: 33.)

Mu mphatso yaikuru ya Mwana wace, Mulungu anadzaza dziko lonse ndi cisomo cace, monga momwe mpweya umayenda kuzungulira dziko lonse. Onse amene asankha kupuma mpweya wopatsa moyowu adzakhala ndi moyo, nadzakula misinkhu yokwana amuna ndi akazi mwa Kristu Yesu.

Monga duwa limayang’ana ku dzuwa, kuti kuwala kwace kulithangate kulikometsa ndi kulifananitsa, coinco ifenso tidziyang’ana ku Dzuwa la Cilungamo kuti Kumwamba kuwale pa ife, kuti makhalidwe athu akule m’cifanizo ca Kristu.

Yesu aphunzitsa cinthu cimodzimidzici pamene ati, “Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa Inu. Monga nthambi siingathe kubala cipatso pa yokha ngati siikhala mwa mpesa, motero mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine... Wopanda Ine simungathe kucita kanthu.” (Yohane 15: 4, 5.) Inu mumangilira pa Kristu kuti mukhale ndi moyo woyera, monga nthambi imangirira pa mtengo kuti ikule ndi kubala cipatso. Wopanda Iye mulibe moyo. Mulibe mphamvu ya kukana mayeso kapena kukula m’cisomo ndi m’kuyera mtima. Mukakhala mwa Iye, mudzakula. Mukamatunga moyo wanu kwa Iye, simudzafota kapena kukhala opanda zipatso. Mudzakhala ngati mtengo wookedwa m’mbali mwa madzi.

Ambiri amaganiza kuti ayenera kugwira mbali ina ya nchito okha. Anakhulupirira kuti Yesu awakhululukira zoipa zawo, koma tsopano ali kufuna kukhala bwino ndi kuyesa kwawo kokha. Koma kuyesa kuli konse kotere kuyenera kucotsedwa. Yesu ati, “Wopanda Ine simungathe kucita kanthu.” Kukula kwathu m’cisomo, cimwemwe cathu, kufunika kwathu, — zonse ziri pa kugwirizana ndi Kristu. Pa kulankhula ndi Iye, tsiku liri lonse, ora liri lonse, — pa kukhala mwa Iye, — tidzakula m’cisomo. Si woyamba yekha, komanso wotsiriza wa cikhulupiriro cathu. Kristu ndiye woyamba ndi wotsiriza ndi wa masiku onse. Iye adzakhala nafe, si kumayam-

biro kokha ndi kumapeto kwa ulendo wathu, koma pa phazi liri lonse la pa njira. Davide ati, “Ndaika Yehova patsogolo panga nthawi zonse: popeza ali pa dzanja langa la manja, sindidzagwedezeka.” (Salmo 16: 8.)

[52] Kodi muli kufunsa, “Kodi ine ndikhala bwanji mwa Kristu?”—Monga momwe udamlandirira poyamba. “Cifukwa cace monga momwe munalandira Kristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye.” “Wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiriro.” (Akolose 2: 6; Heb. 10: 38.) Udadzipereka kwa Mulungu, kukhala wace wathunthu, kumtumikira ndi kumvera Iye, ndipo udamlandira Kristu kukhala Mpulumutsi wako. Sukadatha wekha kupembedzera zoipa zako kapena kusintha mtima wako; koma pa kudzipereka kwa Mulungu, udakhulupirira kuti Iye adakucitira zonsezi cifukwa ca Kristu. Ndi cikhulupiriro udasanduka wa Kristu, ndipo mwa Kristu udzakula mwa Iye, — pa kupereka ndi kulandira. Upereke zonse, — mtima wako, cifuniro cako, nchito yako, — kudzipereka kwa Iye kumvera zofuna zace zonse; ndipo utenge zonse, — Kristu, cidzalo ca madalitso onse, kukhala mu mtima mwako, kukhala mphamvu zako, cilungamo cako, mthangati wako wosatha, — kukupatsa mphamvu ya kumvera.

Udzidzipereka kwa Mulungu pa m’ mawa; imeneyi ikhale nchito yako yoyamba. Pemphero lanu likhale lakuti, “Nditengeni Yehova, ndikhale wanu ndense. Ndiika zolinganiza zanga zonse pa mapazi anu. Mucite nane lero mu nchito yanu. Khalani ndi ine, nchito zanga zonse zicitike mwa Inu.” Zimenezi zidzicitika tsiku liri lonse. M’ mawa uli wonse udzipereke kwa Mulungu kwa tsiku limenelo. Pereka zolinganiza zako zonse kwa Iye, kuti uzicite kapena uzileke monga mwa kutsogolera kwace. Coteru tsiku ndi tsiku udzapereka moyo wako m’ manja a Mulungu, motero moyo wako udzaumbidwa kufanana ndi moyo wa Kristu.

Moyo wa mwa Kristu ndi moyo wa mpumulo. Kapena simudzakhala cimwemwe cacikurukuru cakutooneka ndi kunja komwe, koma mudzakhala mtendere wacete wa cikhulupiriro. Ciyembekezo cako siciri mwa iwe wekha; koma mwa Kristu. Zofooka zako zalumikizana ndi mphamvu yace, kusadziwa kwako ndi nzeru zace, kulefuka kwako ndi mphamvu zace zosatha. Coteru usayang’ane kwa iwe wekha, usaganize za iwe wekha, koma yang’ana kwa Kristu. Uganize za cikondi cace, za ubwino wace, za ungwiro wace,

za makhalidwe ace. Moyo wathu udziganiza za Kristu m'kudzikana kwace, Kristu m'kudzicepetsa kwace, Kristu m'kuyera kwace, za Kristu m'cikondi cace cosayerekezeka. Udzasandulika m'cifaniziro cace pa kumkonda Iye, pa kumtsanza Iye, pa kutsamira pa Iye.

Yesu ati, “Khalani mwa Ine.” Mau amenewa amatipatsa ife mpumulo, kukhazikika, cikhulupiriro. Kawirinso aitana, “Idzani kuno kwa Ine... ndipo ndidzakupumulitsani inu.” (Mateyu 11: 28, 29.) Mau a Davide atsimikiza ganizo lomweli: “Khala cete mwa Yehova, numlindirire Iye.” Ndipo Yesaya atsimikiza, “M'kukhala cete ndi m'kukhulupirira mudzakhala mphamvu yanu.” (Salmo 37: 7; Yesaya 30: 15.) Mpumulo umenewu supezeka mu ulesi; cifukwa lonjezano la Mpulumutsi lakuitanira mpumulo lalumikizana ndi kuitana kwa nchito: “Senzani gori langa pa inu,... ndipo mudzapeza mpumulo.” (Mateyu 11: 29.) Mtima umene upumuladi pa Kristu udzakhala wofunitsitsa ndi wa cangu kugwira nchito yace.

[53]

Pamene mtima uganizira za iwo wokha, umalekana ndi Kristu, kasupe wa mphamvu ndi moyo. Cifukwa cace nchito ya Satana masiku onse ndiyo kulekanitsa maganizo athu ndi Mpulumutsi, kuti moyo wathu ungalumikizane ndi kulankhulana ndi Kristu. Iye afuna kupatutsa mtima kuti uyang'ane zokondweretsa za dziko, zosamalira za moyo ndi zobvuta ndi cisoni, ndi zoipa za ena, kapena za iwe mwini. Usasoceretsedwe ndi macenjerero ace. Satana amatsogoleranso ambiri amene amazindikiradi, nafuna kukhala moyo wolungama kuganizitsa za zifukwa zawo ndi zofooka zawo, Iye amayembekeza kuwagonjetsa iwo pa kuwalekanitsa ndi Kristu. Ife tisamaganizitsa za ife eni koposa, ndi kuda nkhwana ndi kuopa ngati titi tidzapulumukedi. Zonse zoterezi zimalekanitsa moyo ndi Kasupe wa mphamvu zathu. Pereka kwa Mulungu moyo wako kuti akusungire, ndi kukhulupirira mwa Iye. Lankhula ndi kuganiza za Yesu. Kudzikonda wekha kutaike mwa Iye. Taya kukaika konse; cotsa mantha ako. Nena pamodzi ndi mtumwi Paulo, “Koma ndiri ndi moyo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nawo tsopano m'thupi, ndiri nawo m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene amandikonda nadzipereka yekha cifukwa ca ine.” (Agalatiya 2: 20.) Pumula mwa Mulungu. Iye ali wakutha kusunga cimene iwe udamsungitsa. Ngati ungasiziye wekha m'manja mwace, adzakupatsa mphamvu zoposa wogonjetsa mwa Iye amene anakukonda iwe.

[54] Pamene Kristu anabvala makhalidwe a umunthu, Iye anadzimangirira yekha kwa anthu ndi mfundo ya cikondi imene singathe kuduka ndi mphamvu iri yonse koma ndi kusankha kwa munthu mwini wace. Masiku onse Satana amationetsera ife nyambo za kutikopa ife kuti tidule mfundo imeneyi, — kuti tisankhe kudzilekanitsa tokha ndi Kristu. Pamenepa ndipo tiyenera kuyang'anirapo, tilimbike, ndi kupemphera, kuti kena kasatikope ife kusankha mbuye wina; cifukwa nthawi zonse tiri omasuka kucita izi. Koma tiyeni timangirire maso athu pa Kristu, ndipo Iye adzatisunga ife. Pa kuyang'ana kwa Yesu tiri opulumuka. Pa libe kena kangathe kuticotsa m'manja mwace. Pa kupenyerera kwa Iye kosalekeza, "tisan-dulika m'cithunzithunzi comweci kucokera ku ulemerero kunka ku ulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu." (2 Akor. 3: 18.)

Ndimu m'mene akuphunzira oyamba anakhalira ofanana ndi Mpulumutsi wawo wokonedwa. Pamene ophunzirawo anamva mau a Yesu, iwo anamva mu mtima mwawo kuti amsowa Iye. Anamfuna, nampeza, namtsata Iye. Iwo anali naye m'nyumba, pa gome lodyera, m'cipinda, m'munda. Iwo anali naye monga asikolala ndi mphunzitsi wawo, masiku onse kulandira maphunziro a coonadi kucokera m'milomo yace. Iwo anamuyang'ana Iye, monga akapolo ayang'ana kwa mbuye wawo, kuphunzira nchito yawo. Akuphunzirawo anali anthu "akumva zomwezi tizimva ife." (Yakobo 5: 17.) Anali ndi nkhondo yomweyi ya zoipa. Anali kusowa cisomo comweci, pofuna kukhala ndi moyo woyera.

Ngakhale Yohane, wophunzira wokonedwayo, amene anaonetsera kvveni kweni cifaniziro ca Mpulumutsi, sanangobadwa nawo makhalidwe okonedwawa. Iye sanali wongokonda kuganiza za iye mwini kokha ndi wokonda ulemu, komanso anali wa nsontho ndi wokwiya msanga. Koma pamene makhalidwe a wa Kumwambayo anaonetsedwa kwa iye, anaona kuperewera kwace, ndipo anadzicepetsa yekha podziwa izi. Mphamvu ndi cipiriro, ulamuliro ndi cifundo, Ukulu ndi kufatsa zimene anazona m'moyo wa masiku onse wa Mwana wa Mulungu, zinadzaza moyo wace ndi citamando ndi cikondi. Tsiku ndi tsiku mtima wace unakokedwa kunka kwa Kristu, kufikira analeka kuona za iye mwini cifukwa ca kukonda Mbuye wace. Makhalidwe ace okwiya ndi okonda ulemu anaperekedwa ku mphamvu yolenga ya Kristu. Mphamvu ya kulenganso ya Mzimu

Woyera inalenganso mtima wace. Mphamvu ya cikondi ca Kristu inasintha makhalidwe ace. Cimeneci ndico cimaliziro coonadi ca kulumikizana ndi Yesu. Pamene Kristu akhala mu mtima, makhalidwe onse amasinthika. Mzimu wa Kristu, cikondi cace, zimafewetsa mtima, zimagonjetsa moyo, ndi kuutsa maganizo ndi zolakalaka zofuna Mulungu ndi kumwamba.

Pamene Kristu anakwera kumwamba, maganizo a maonekedwe ace anali cikhalirebe ndi akuphunzira ace. Anali maonekedwe a umunthu wace, wodzala ndi cikondi ndi kuunika. Yesu, Mpulumutsi, yemwe anali kuyenda nawo, nalankhula nawo, napemphera nawo, amene analankhula mau a ciyembekezo ndi cisangalatso ku mitima yawo, uthenga wa mtendere ukali m’mi- lomo yace, anatengedwa kunka kumwamba kucokera kwa iwo, ndipo mau ace aja anabweranso kwa iwo, pamene mtambo wa angelo unamlandira Iye, —‘Ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse kufikira cimaliziro ca nthawi ya pansi pano.’ (Mateyu 28: 20.) Iye anakwera kumwamba m’makhalidwe a umunthu. Iwo anadziwa kuti Iye ali patsogolo pa mpando wacifumu wa Mulungu, ali cikhalirebe Bwenzi lawo ndi Mpulumutsi wawo; ndi kuti cifundo cace sici-nasinthike; Iye anali kumvabe cifundo ndi zisautso za anthu. Iye anali kupereka patsogolo pa Mulungu ubwino wa mwazi wace wa mtengo wapatli, nasonyeza mapazi ndi manja ace olasidwa, kukumbutsa mtengo umene adapereka kuombola anthu ace. Iwo anadziwa kuti Iye anapita kumwamba kuwakonzera iwo malo, ndi kuti adzabweranso kuwalandira iwo kwa Iye yekha.

[55]

Pamene anakomana pamodzi, atakwera kale, iwo anali ofunit-sitsa kupereka zofunsa zawo kwa Atate m’dzina la Yesu. Ndi mtima woonadi iwo anagwada m’pemphero, nabwereza mau a citsimikizo, “Ngati mudzapempha Atate kanthu adzakupatsani inu m’dzina langa... Pemphani, ndipo mudzalandira, kuti cimwemwe canu cikwaniridwe.” (Yohane 16: 23, 24.) Iwo anakweza pamwamba dzanja la cikhulupiriro ndi kutsutsana kolimba, “Kristu ndiye amene adafera, inde makamaka ndiye amene adauka kwa akufa, amene akhalanso pa dzanja la manja la Mulungu, amenenso atipemphera ife.” (Aroma 8: 34.) Ndipo Pentekoste anawatengera iwo Mnkhoswe, amene Kristu anati Iyeyo “adzakhala ndi inu.” Ndiponso Iye anati, “Kuyenera kwa inu kuti ndicoke Ine; pakuti ngati sindicoka, Mnkhosweyo sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzam-

tuma Iye kwa inu.” (Yohane 14: 17; 16: 7.) Cifukwa cace mwa Mzimu, Kristu anali kukhala m’mitima ya ana ace masiku onse. Kugwirizana kwawo ndi Iye kunali kopambana tsopano koposa pamene anali pamodzi nawo mwini wace. Kuunika, ndi cikondi, ndi mphamvu ya Kristu wokhala m’kati mwawo, zinawala mwa iwo, kotero kuti anthu, poona, “anazizwa; ndipo anawazindikira kuti anakhala pamodzi ndi Yesu.” (Mac. 4: 13.)

Zonse zimene Kristu akacitira ophunzira ace oyamba aja, afuna kucitira ana ace lero; cifukwa m’pempheo lotsiriza lija, kagulu ka akuphunzira katamzungulira, Iye anati, “Koma sindipempherera iwo okha, koma iwo akukhulupirira Ine, cifukwa ca mau awo.” (Yohane 17: 20.)

[56] Yesu anatipempherera ife, ndipo anapempha kuti ife tikhale amodzi mwa Iye, monga Iye ali mmodzi ndi Atate. Ha! Kugwirizanadi nanga! Mpulumutsi anati za Iye yekha, “Sakhoza Mwana kucita kanthu pa yekha,” “koma Atate wokhala mwa Ine acitA nchito zace.” Pompo, ngati Kristu ali kukhala m’mitima yathu, adzagwira nchito mwa ife “kufuna ndi kucita komwe monga mwa kukoma mtima kwace.” (Afilipi 2: 13.) Tidzagwira nchito monga anagwirira Iye; tidzaonetsera mzimu womwe adauonetsa Iye. Ndipo potero, pa kumkonda Iye ndi kukhala mwa Iye, “Tidzakula m’zinthu zonse, [57] kufikira Iye amene ali mutu, ndiye Kristu.” (Aefeso 4: 15.)

MUTU 9—NCHITO NDI MOYO

Mulungu ali kasupe wa moyo ndi wa kuunika ndi wa cimwemwe ku maiko onse. Monga mitsitsi ya kuwala yocokera ku dzuwa, monga mitsinje ya madzi yocokera ku kasupe wa moyo, madalitso amayenda kuturuka kwa Iye kunka kwa zilengedwe zace zonse. Ndipo kuli konse kumene kuli moyo wa Mulungu m’mitima ya anthu, udzaturukira kwa ena m’cikondi ndi kudalitsa.

Cimwemwe ca Mpulumutsi cinali kutukula ndi kuombola anthu otaika. Cifukwa ca ici sanauyesera moyo wace ngati wamtengo wapatali kwa Iye yekha, koma anapirira mtanda, nanyoza manyazi. Coteru angelo ali kugwira nchito masiku onse kukondweretsa ena. Cimeneci ndico cimwemwe cawo. Nchito imene mitima ya anthu odzikonda okha angaiyesere yonyozeka, kutumikira iwo amene ali oipitsitsa, ndi onyozeka m’makhalidwe awo, imeneyi ndiyo nchito ya angelo osacimwa. Mzimu wa Kristu wa cikondi codzipereka yekha nsembe, ndiwo mzimu umene uli kumwamba, ndipo ndiwo mtima wa cimwemwe cace. Umenewu ndiwo mzimu umene ati adzalandire otsatira ace, ndi nchito yomwe ati adzacite.

Pamene cikondi ca Kristu cilowa mu mtima, monga zonunkhira zokoma, sicingathe kubisika. Mphamvu yace yopatulika idzamveka m’mitima ya anthu onse amene tikomana nawo. Mzimu wa Kristu ukakhala mu mtima uli ngati kasupe m’cipululu, amene amatsit-simutsa zinthu zonse, ndi onse amene ali pafupi kuonongeka amafunafuna kumwa madzi ace amoyo.

Cikondi ca Kristu cidzaonekera pa kufuna kugwira nchito monga anagwira Iyeyo, kudalitsa ndi kukweza mtundu wa anthu. Cidzatit-sogolera kukonda, kukoma mtima, ndi kumvera cifundo olengedwa onse a cisamaliro ca Atate wathu wa kumwamba.

Moyo wa Mpulumutsi pa dziko lapansi sunali moyo wa mten-dere, ndi wodzisamalira yekha, koma Iye anagwira nchito ndi khama, moonu mtima, ndi wosatopa kupulumutsa anthu otaika. Kuyambira m’khola la ng’ombe kufikira pa Golgota, Iye anatsata njira ya kudzikana, ndipo sanafuna kumasulidwa ku nchito yobvuta,

[58] maulendo opweteka, ndi nkhwawa zotopetsa. Iye anati. “Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri.” (Mateyu 20:28.) Cimeneci ndico cinali ciyang’aniro cacikuru ca moyo wace. Zinthu zina zonse zinali zaciwiri ndi zakungothangata. Cakudya cace ndi cakumwa cace kunali kucita cifuniro ca Mulungu ndi kutsiriza nchito yace. Kudzikonda kunalibe mbali m’nchito yace.

Cotero iwo amene alandira cisomo ca Kristu adzakhala ofulumira kupereka nsembe iri yonse, kuti ena amene Kristu anawafera agawane nawo mphatso ya kumwamba. Adzacita zonse monga angathe kukometsa dziko cifukwa ca kukhala iwo momwemo. Mzimu woterewu ndico citsimikizo ca kukula kwa moyo wotembenuka koono. Munthu akadza kwa Kristu, msanga mumadza cifuniro mu mtima mwace ca kudziwitsa ena bwenzi lopambana limene walipeza mwa Yesu; coonadi ca kupulumutsa ndi ca kuyeretsa sicingathe kutsekeka mu mtima mwace. Ngati tabvekedwa ndi cilungamo ca Kristu, ndi kudzazidwa ndi cimwemwe ca Mzimu wace wa kukhala m’kati mwathu, sitidzakhoza kukhala cete. Ngati talawa ndi kuona kuti Ambuye ali wabwino, tidzakhala nako kanthu kakufotokoza. Monga Filipino pamene anapeza Mpulumutsi, ife tidzaitana ena kudza kwa Iye. Tidzafunafuna kuwaonetsera zokopa za Kristu, ndi zinthu zosaoneka za dziko lirinkudza. Tidzakhala ndi cifuniro cacikuru ca kutsata njira imene Yesu anayenda. Tidzalakalaka kuti iwo otizungulira aone “Mwana wa Nkhosa wa Mulungu, amene acotsa cimo lace la dziko lapansi.”

Ndipo nchito ya kudalitsa ena idzatalitsa ife tomwe. Cimeneci ndico cimene anali kufuna Mulungu pakutipatsa ife mbali ya kucita mu nzeru ya ciombolo. Iye anawapatsa anthu mwai wopambana cimwemwe coposa, cimene Mulungu apereka kwa iwonso, kugawira anzawo madalitsowo. Umenewu ndiwo ulemu wopambana cimwemwe coposa, cimene Mulungu apereka kwa anthu. Iwo amene agwira cotero nchito za cikondi amadza pafupifupi ndi Mlengi wawo.

Akadafuna, Mulungu akadapereka uthengawu, ndi nchito ya utumiki wa cikondi, kwa angelo a kumwamba. Akadacita nazo zinthu zina za kutsirizira nchito yace. Koma cifukwa ca cikondi cace cosatha, Iye anasankha kutiyesa ife ogwira nchito pamodzi ndi Iye ndi Kristu, ndi angelo, kuti tigawane nawo madalitso,

cimwemwe, kukwezeka kwa uzimu, zimene zimaturuka mu utumiki uwu wopanda kudzikonda.

Timakhala oyanjana ndi Kristu pa kusautsidwa naye pamodzi. Nchito iri yonse ya kudzipereka nsembe cifukwa ca ubwino wa ena, imalimbitsa mzimu wa kukoma mtima mu mtima mwa wopat-sayo, ndi kumlumikizitsa iye ndi Mombolo wa dziko, amene “anali wolemera, koma anasanduka wosauka cifukwa ca inu, kuti inu, ndi kusauka kwace, mukakhale olemera.” Moyo wathu udzakhala dal- [59] itso kwa ife, ngati ife tingakwanitse cifuniro ca Mulungu m’mitima yathu.

Ngati ungagwire nchito monga Kristu afunira kuti akuphunzira ace adzicita, ndi kumpindulira miyoyo, udzamva mu mtima kuti usowa nzeru za zinthu za kumwamba, ndi kumva njara ndi ludzu la cilungamo. Udzamdandaulira Mulungu, ndipo cikhulupiriro cako cidzalimba, ndipo moyo wako udzamwa pa citsime ca cipulumutso. Pokomana ndi mabvuto ndi mayeso, adzakuthamangitsira ku Bible ndi ku pemphero. Udzakula m’cisomo ndi cidziwitso ca Kristu, ndipo udzakulitsa macitidwe abwino.

Mzimu wa nchito yopanda umbombo ya kuthangata ena, umpatsa makhalidwe okhazikika ofanana ndi Kristu, ndipo umadza ndi mtendere ndi cimwemwe kwa iye wakuulandira. Zifuniro zimadzutsidwa. Mulibe malo a ulesi ndi kudzikonda. Iwo amene acita naco cisomo ca Kristu adzakula ndipo adzakhala ndi mphamvu kugwira nchito ya Mulungu. Iwo adzaona za uzimu mwangwiro, adzakhala ndi cikhulupiriro colimba, cokula, ndi mphamvu yocuruka m’pemphero. Mzimu wa Mulungu, pogwira nchito mu mtima, udzayeretsa moyo kuti uyanjane ndi Mulungu. Iwo amene adzipereka okha coteru ku nchito yosadzikonda okha cifukwa ca ubwino wa ena, ali kugwiradi nchito ya cipulumutso cawo.

Njira imodzi yokha ya kukulira m’cisomo ndiyo kugwira nchito imene Kristu anatipatsa ife osaganizira za ife tokha, — kucita, monga mwa nzeru zathu, kuthangata ndi kudalitsa amene asowa cithangato cathu. Mphamvu zimadza ndi kucitacita; cangu ndiwo makhalidwe eni eni a moyo. Iwo amene ayesa kukhala moyo wa Cikristu pakungolandira madalitso amene amadza kwa iwo mwa cisomo, osacita kanthu kwa Kristu, ali kuyesa kukhala ndi moyo pa kungodya osagwira nchito. Ndipo anthu amene acita coteru adzafa mwa uzimu.

Munthu amene angakane kucita nazo ziwalo zace, posacedwa zidzakhala zopanda mphamvu zosatha kucita kanthu. Coteru munthu amene sacita nazo mphamvu zimene Mulungu anampatsa, samangolephera kokha kukula mwa Kristu, koma amataya mphamvu yomwe adalandira kale.

[60] Mpingo wa Kristu ndiwo umene Mulungu adausankha kugwira nchito ya cipulumutso ca anthu. Nchito yace ndiyo kunyamula uthenga kunka nawo ku dziko lonse. Ndipo nchitoyo iri pa Akristu onse. Ali yense, monga mwa talente lace, ndi nthawi yace, akwanitse nchito ya Mpulumutsi. Cikondi ca Kristu, coonetsedwa kwa ife, citiyesa ife amangawa kwa onse amene samdziwa. Mulungu watipatsa ife kuunika, si kwa ife tokha, komanso kuwaunikira iwo.

Otsata Kristu akadakhala a maso ku nchito, kumene kuli mmodzi lero, kukadakhala zikwi, kulalikira uthenga m'maiko a akunja. Ndipo onse amene sakadakhaza kugwira nchitoyi ndi manja awo, mwenzi ali kuithangata ndi ndalama zawo, ndi cifundo cawo, ndi mapemphero awo. Ndipo m'maiko a Cikristu mukadakhala nchito yoposa yofuna miyoyo.

Sikufunika kuti titonka ku maiko a akunja, kapena kusiya mabanja athu, ngati nchito yathu iri kumeneko, pofuna kugwira nchito ya Kristu. Tingathe kugwira nchito ya Kristu, m'mabanja mwathu, mu mpingo, pakati pa amene tizolowerana nawo, ndi iwo amene tigwira nawo nchito.

Mbali yaikuru ya moyo wa Mpulumutsi wathu, anali m'nchito yotopetsa m'nyumba yopala matabwa ku Nazarete. Angelo otunikira anali kusamalira Ambuye wa moyo pamene Iye anali kuyenda pamodzi ndi atsamunda, ndi anchito osadziwika ndi osalemekezeka. Iye anali kukwanitsabe nchito yace mokhulupirika pamene anali kugwira nchito yace yonyozekayo monga pamene anali kuciritsa odwala, kapena, poyenda pa nyanja ya Galileya. Coteru, m'nchito ndi m'malo onyozeka a moyo, tiyende ndi kugwira nchito pamodzi ndi Yesu.

Mtumwi ati, “Yense, m'mene anaitanidwamo, abale, akhale momwemo ndi Mulungu.” (1 Akor. 7: 24.) Munthu wanchito agwire nchito yace m'njira imene ingalemekeze Mbuye wace cifukwa ca kukhulupirika kwace. Ngati ali wotsata Kristu woona, adzanyamula cipembedzo cace mu kanthu kali konse kamene acita, ndi kuonetsera mzimu wa Kristu kwa anthu. Wogwira nchito ndi

zitsulo angathe kukhala kazembe wa cangu ndi wokhulupirika wa Iye amene anagwira nchito m'moyo wodzicepetsa pakati pa mapiri a Galileya. Ali yense amene achula dzina la Kristu adzigwira nchito kotero kuti ena pakuona nchito zace zabwino alemekeze Mlengi ndi Mombolo wawo.

Ambiri amadziletsa kupereka mphatso zawo ku nchito ya Kristu cifukwa anzawo ali ndi mphatso ndi mwayi koposa zawo. Ambiri amaganiza kuti koma iwo okha amene ali ndi matalente ambiri ndiwo ayenera kupereka nzeru zawo ku nchito ya Mulungu. Ambiri amaganiza kuti matalente adaperekedwa kwa anthu ena a mwayi, koma ena sanawaitane kugwira nawo nchito kapena kulandira mphotho. Koma m'fanizo muja sadanene coinco. Pamene mwini nyumba anaitana akapolo ace, anampatsa munthu ali yense nchito yace.

[61]

Ndi mzimu wokonda tidzagwira nchito zonyozeka, “monga ngati kwa Ambuye.” (Akolose 3: 2.) Ngati cikondi ca Mulungu ciri mu mtima, cidzaonekera m'moyo. Pfungo labwino la Kristu lidzatizungulira ife, ndipo citsanzo cathu cidzautsa, ndi kudalitsa ena.

Usalindire nthawi ina yabwino, kapena kuyembekeza luso loposa limene uli nalo usanapite kukagwira nchito ya Mulungu. Usaganize za zimene dziko liti liganizire za iwe. Ngati moyo wako wa tsiku liri lonse ucitira umboni za ungwiro ndi kulimbika kwa cikhulupiriro cako, ndipo ena natsimikizidwa kuti iwe ufuna kuwacitira zabwino, nchito yako sidzapita pa cabe.

Wakuphonzira wa Yesu, ngakhale ali wonyozeka ndi wosauka koposa onse angathe kukhala dalitso kwa ena. Kapena iwo sangadziwe kuti iwo ali kucita kanthu kabwino, koma ndi cikoka cawo cosadziwika, iwo angayambitse mafunde a madalitso amene adzakulirakulira, ndi kubala zipatso zodala zimene iwo sangazidziwe, kufikira tsiku limene adzalandira mphotho yotsiriza. Iwo sali kumva kapena kudziwa kuti ali kucita cinthu cacikuru. Iwo samadzibvutitsa okha ndi kudera nkhwana za kupambana. Iwo amayenda kacete-cete, namacita mokhulupirika nchito imene Mulungu awapatsa, ndipo moyo wawo sudzapita pacabe. Miyoyo yawo idzakulakulabe m'cifaniziro ca Kristu; iwo ali anchito anzace a Mulungu m'moyo uno, ndipo motero ali kukwanira kudzalandira nchito yaikuru ndi cimwemwe cosadetsedwa ca moyo ulinkudza.

[62]

[63]

MUTU 10—KUDZIWA MULUNGU

Mulungu ali kufuna kudziululira kwa ife ndi kutiyanjanitsa ife ndi Iye m’njira zambiri. Cilengedwe ciri kulankhula nafe osaleka. Mtima wotseguka udzatsimikizidwa ndi cikondi ndi ulemerero wa Mulungu woonekera mu nchito ya manja ace. Khutu lomvetsera lingathe kumva ndi kuzindikira zonena za Mulungu kupyolera mwa zinthu za cilengedwe. Minda yobiriwira, mitengo yaitari, mphundu ndi maluwa, mitambo, mvula, mtsinje woyenda, ulemerero wa kumwamba, zimalankhula ndi mitima yathu, ndi kutiitana ife kuti tizolowerane ndi Iye amene adalenga zonsezo.

Mpulumutsi wathu anamanga maphunziro ace a mtengo wapitari ndi zinthu za cilengedwe. Mitengo, mbalame, maluwa a m’madambo, mapiri, nyanja, ndi miyamba yabwino, pamodzi ndi zooneka ndi zocitika m’moyo wa tsiku liri lonse, zonsezi zinalumikidwa ndi mau a coonadi, kuti maphunziro ace adzikumbukiridwa, ngakhale pakati pa zinchito za moyo wa munthu.

Mulungu afuna ana ace kuti adzizindikira nchito zace, ndi kukondwera ndi zokoma za cete zimene Iye anakometsa nazo kwathu kwa dziko lapansi. Iye amakonda zinthu zokometsera, ndipo koposa zokometsera za kunja amakondetsa zokometsera za makhalidwe; Iye afuna kuti ife tikhale angwiro ndi osalala monga maluwa.

Ngati tingamvetsere, nchito zolengedwa za Mulungu, zidzati-phunzitsa ife maphunziro abwino a kumvera ndi cikhulupiriro. Kuyambira nyenyezi zimene zimangoyendabe m’njira zawo zopanda mkwaso mlengalenga ku mibadwo mibadwo, kufikira kanthu kopepetsa ka pa dziko lapansi, zinthu za cilengedwe zimamvera cifuniro ca Mlengi wawo. Ndipo Mulungu amasamalira kanthu kali konse, ndi kuthangata kanthu kali konse kamene Iye adakalenga. Iye amene amanyamula maiko osawerengeka m’cilengedwe cace conse, pa nthawi yomweyo amasamalira zosowa za katimba kakang’ono, kamene kamayimba nyimbo yace wopanda mantha. Pamene anthu apita ku nchito zawo za masiku onse ndi pamene ali kupemphera;

pamene ali kugona usiku, ndi pamene adzuka m'mawa; pamene munthu wolemera ali kudya phwando m'cinyumba cace, kapena pamene wosauka asonkhanitsa ana ace kudya topanda pace, ali yense wa iwo amayang'ani - dwa ndi Atate wa kumwamba. Palibe misozi imene imagwa yosadziwika ndi Mulungu. Palibe cimwemwe cimene Iye sacidziwa. [64]

Ngati tingakhulupirire ndithu izi, nkhawa zonse zidzacoka. Miyoyo yathu sidzagwiritsidwa mwala monga iri tsopano; cifukwa cinthu ciri conse cacikuru kapena cacing'ono, cidzasiyidwa m'manja a Mulungu, amene sabvutika ndi kucuruka kwa zosamalira, kapena kutopa ndi kulemera kwao. Pompo tidzakhala ndi mtendere wa mu mtima umene ambiri saudziwa.

Pamene mtima wako ukondwera ndi zinthu zokongola za dziko lapansi, ganiza za dziko lirinkudza limene silidzadziwa zowawa za ucimo ndi imfa; kumene nkhope ya cilengedwe sidzabvalanso mthunzi wa temberero. Mtima wako uganize za kwawo kwa opulumutsidwa, ndi kukumbukira kuti kudzakhala kokometsetsa koposa m'mene uganiziramo. Mu mphatso zosiyana za Mulungu mwa cilengedwe timaonamo mwa cimbuuzi ulemerero wa Mulungu. Kwalembedwa. “Zimene diso silinaziona, ndi khutu silinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zonse Mulungu anakonzeratu iwo akumkonda Iye.” (1 Akor. 2: 9.)

Wolemba Poetry ndi wophunzira za cilengedwe amanena zam-biri za cilengedwe, koma Mkristu ndiye amakondwera nako kukoma kwa dziko ndi ciyamiko cacikuru, cifukwa iye amazindikira nchito ya Atate wace, naona cikondi cace m'duwa ndi citsamba ndi mtengo. Palibe wina angazindikire kukongola kwa phiri ndi dambo, mtsinje ndi nyanja, amene samaziyang'ana izo kuti ziri citsimikizo ca cikondi ca Mulungu kwa anthu.

Mulungu amalankhula nafe kupyolera mwa nchito zace za cilengedwe, ndi kupyolera mu mphamvu ya Mzimu wace mu mtima. Mwa zinthu zotizungulira, ndi mwa zinthu zooneka tsiku ndi tsiku, tingapezemo maphunziro abwino, ngati mitima yathu iri yotseguka kuzizindikira. Davide, pofotokoza nchito ya ukuru wa Mulungu ati, “Dziko lapansi ladzala ndi cifundo ca Yehova.” (Salmo 33: 5.) “Wokhala nazo nzeru asamalire izi, ndipo azindikire za cifundo za Yehova.” (Salmo 107: 43.)

[65] Mulungu amalankhula kwa ife M' mau ace. M' menemo muli bvumbulutso langwiwo la makhalidwe ace, za macitidwe ace ndi anthu, ndi za nchito yaikuru ya ciombolo. M' menemo muli mwambi wa akulu a kale ndi aneneri ndi wa anthu ena oyera mtima akale. Iwo anali anthu “akumva zomwezi tizimva ife.” (Yakobo 5: 17.) Ife tiona m' mene iwo anali kulimbana ndi zogwetsa mphwai monga ife tomwe, m' mene iwo anagwera m' mayeso monga timagwa ife, koma nalimbanso mtima nagonjetsa ndi cisomo ca Mulungu: ndipo popenyenera, ifenso tilimbika mtima mu nkondo yathu ya cilungamo. Pamene tiwerenga za macitidwe abwino opatsidwa kwa iwo, za kuunika ndi cikondi ndi madalitso amene anali kukondwera nawo, ndi nchito imene adacita mwa cisomo copatsidwa kwa iwo, mzimu umene unawauzira iwo, umayatsanso moto wa kupambanitsa m' mitima yathu, ndi cifuniro ca kufanana nawo m' makhalidwe, — kufanana nawo pa kuyenda ndi Mulungu.

Yesu anati za Malembo a Cipangano Cakale, — koposa kotani nanga Malembo a Cipangano Catsopano, — “Ndipo akundicitira Ine umboni ndi iwo omwewo” (Yohane 5: 39), Mombolo wathu, mwa Iye amene muli ciyembekezo cathu ca moyo wosatha. Inde, Bible lonse lifotokoza za Kristu. Kuyambira mau oyamba a cilengedwe, — cifukwa “kanthu kali konse kanapangidwa sikanapangidwa kopanda Iye” (Yohane 1: 3), — kufikira ku lonjezo lotsiriza, “Taona ndidza msanga” (Cibvu. 22: 12), tiri kuwerengamo za nchito zace ndi kumvetsera mau ace. Ngati ufuna kuzolowerana ndi Mpulumutsi, phunzira Malembo Opatulika.

Dzaza mtima wonse ndi mau a Mulungu. Iwo ali madzi a moyo, akuziziritsa ludzu lako. Iwo ali mkate wa moyo wocokera kumwamba. Yesu ati, “Ngati simukudya thupi la Mwana wa munthu, mulibe moyo mwa inu nokha.” Ndipo anafotokoza za Iye yekha pa kunena, “Mau amene ndalankhula ndi inu ndiwo Mzimu, ndiponso moyo.” (Yohane 6: 53, 63.) Matupi athu amapangidwa ndi zimene tidya ndi kumwa; ndipo monga m' thupi moteronso mu mzimu: timapatsa mphamvu ku moyo wathu wa uzimu ndi zimene timaganiza.

Mutu wa ciombolo ndiwo umene anglo alakalaka kuonamo; idzakhala nkhani ndi nyimbo ya oomboledwa ku nthawi zonse zosatha. Kodi sitiyenera kuciganizira ndi kuciphunzira tsopano? Cifundo ndi cikondi cosatha ca Yesu, nsembe imene anaipereka

cifukwa ca ife, tiyenera kuziganizira ndi mitima ya cisoni ndi yot-simikiza. Tiyenera kuganizira za makhalidwe a Mombolo wathu wokondedwa ndi Wotipembedzera ife. Tiyenera kuganizira za nchito ya Iye amene anadza kupulumutsa anthu ace ku macimo awo. Tikamaganiza coteru zinthu za kumwamba, cikhulupiriro cathu ndi cikondi cathu cidzakula ndi mphamvu, ndipo mapemphero athu adzalandirika kwa Mulungu, cifukwa adzasanganikira kwambiri ndi cikhulupiriro ndi cikondi. Iwo adzakhala olongosoka ndi otentha. Mu mtima mudzakhala cikhulupiriro cosalekeza ca mwa Yesu, ndi macitidwe a moyo a masiku onse mu mphamvu yace ya kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye.

[66]

Pamene tilingirira za ungwiro wa Mpulumutsi, tidzalakalaka kusinthidwa konse konse, ndi kukonzedwanso m'cifanizo ca ungwiro wace. Moyo udzamva njara ndi ludzu la kufuna kukhala ofanana ndi Iye amene timpembedza. Maganizo athu akamaganiza kwambiri za Kristu, tidzalanikhulanso kwambiri za Iye kwa anzathu, ndi kumuonetsera Iye ku dziko lapansi.

Bible sanalembedwa kwa ophunziritsa okha; koma makamaka analembedwa kwa anthu wamba. Zoonadi zazikuru zoyenera cipulumutso ca anthu zinalembedwa mooneka bwino monga usana; ndipo palibe angaphophonye ndi kusocera koma iwo amene atsata cifuniro cawo m'malo mwa kutsata cifuniro coonetsedwa bwino lomwe ca Mulungu.

Tisamalandira umboni wa munthu kutiuza zimene malembo aphunzitsa, koma tidziphunzira tokha mau a Mulungu. Ngati tingamangolandira maganizo a anzathu, cangu cathu ndi nzeru zathu zidzacepa. Mphamvu za malingaliro zidzacepa cifukwa ca kusacita nawo pa kuganiza zinthu za Mulungu, ndipo tidzataya nzeru zathu za kuzindikira matanthauzo akuya a Mau a Mulungu. Malingaliro adzakula ngati ticita navvo kuphunzira kugwirizana kwa maphunzitsa a Bible, kulinganiza lembo ndi lembo, ndi zinthu za uzimu ndi za uzimu.

Palibe kanthu kenanso kangathe kulimbitsa malingaliro athu koposa kuphunzira malembo a Bible. Palibe bukhu lina la mphamvu kuutsa maganizo ndi kuwapatsa mphamvu, monga zoonadi za Bible. Anthu akadaphunzira mau a Mulungu monga ayenera, akadakhala ndi nzeru zambiri, ndi makhalidwe abwino, ndi nchito yokhazikika imene sionekaoneka masiku ano.

Kuwerenga Bible mofulumira, ungopezamo kaubwino pang’ono. Munthu angathe kuwerenga Bible lonse, koma nalephera kuona kukoma kwace kapena kuzindikira matanthauzo ace akuya obisika. Vesi limodzi litaphunziridwa bwino kufikira matanthauzo ace amveka mu mtima, ndi kuona kugwirizana kwace ndi nzeru ya cipulumutso, liri la mtengo wapitari, koposa kuwerenga macaputara ambiri osapindulamo kanthu kothangata mtima. Sunga Bible wako. Ukapeza nthawi muwerenge; loweza malembo ace. Ngakhale uli kuyenda mu mseu, ungawerenge vesi, ndi kuliganizira, potero lidzakhazikika mu mtima mwako.

[67] Sitingathe kulandira nzeru opanda kuyang’anitsitsa koono ndi kuphunzira pamodzi ndi pemphero. Mbali zina za Malembo ziri zofewa kwambiri inde kuti munthu ali yense angathe kumvetsetsa mofewa; koma ziripo mbali zina, zimene matanthauzo awo sali pamwamba, pooneka msanga. Lembo liyenera kulinganizidwa ndi lembo linzace. Tiyenera kufunafuna mosamalira, ndi kuganiza uli kupemphera mu mtima. Kuphunzira kotere kudzabwezedwa mphotho koposa. Monga wa mumgodi amapeza cuma cobisika pansi pa dziko, coteru iye amene, mwa khama, afunafuna Mau a Mulungu monga cuma cobisika, adzapeza zoonadi za mtengo wapitari, zimene ziri zobisika kwa iye amene afuna mwa mphwayi. Mau a Mulungu, atakhala mu mtima, adzakhala monga mitsinje yotumphuka kucokera ku kasupe wa moyo.

Usamaphunzira Bible wopanda pemphero. Tisanalitsegule, tiyenera kupempha kuwala kwa Mzimu Woyera, ndipo kudzapatsidwa. Pamene Natanieli anadza kwa Yesu, Mpulumutsi ananena, “Ona mu Israyeli ndithu, mwa iye mulibe cinyengo!” Natanieli anati, “Kucokera kuti mundidziwa ine?” Yesu anayankha, “Asanakuitane Filipino, pokhala iwe pansi pa mkuyu, ndinakuona iwe.” (Yohane 1: 47, 48.) Ndipo Yesu adzationa ifenso m’ malo a mtseri a pemphero, ngati tingampempe kuunika, kuti tidziwe cimene ciri coonadi. Angelo a ku dziko lowala, adzakhala ndi iwo amene mu mtima mwawo afuna kutsogozedwa ndi Mulungu.

Mzimu Woyera umakuza ndi kulemekeza Mpulumutsi. Nchito yace ndiyo kuonetsera Kristu, ungwiro wa cilungamo cace, ndi cipulumutso cacikuru cimene tiri naco mwa Iye. Yesu ati, “Iyeyo adzatenga za mwa Ine nadzalalikira kwa inu.” (Yohane 16: 14.) Mzimu wa coonadi ndiye mphunzitsi wa luso wa coonadi. Mulungu

amalemekeza mtundu wa anthu, popeza anapereka Mwana wace kuwafera iwo, ndi kupereka Mzimu wace kukhala mphunzitsi ndi mtsogoleri wawo kosalekeza.

[68]

[69]

MUTU 11—UBWINO WA PEMPHERO

Mulungu amalankhula ndi ife kupyolera mwa cilengedwe ndi Mau ace, mwa ukulu wace, ndi mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Koma ndi zosakwana zimenezi; tifunikanso kutsanulira mitima yathu kwa Iye. Pofuna kuti tikhale naco cangu ndi moyo wa uzimu, tiyenera kulumikizana kweni kweni ndi Atate wathu wa Kumwamba. Kapena mitima yathu ingatembenukire kwa Iye; kapena inde tingamaganizire za nchito zace, za cifundo zace, ndi za madalitso ace; koma kumeneku si kulankhula naye. Kulankhula ndi Mulungu koma tidzimuuza Iye zinthu za moyo wathu weni weni.

Pemphero ndiko kuuza Mulungu zonse za mu mtima monga bwenzi lathu. Maka maka sicifukwa ca kuti Mulungu adziwe za mu mtimazo, koma kuti ife tikhoze kumlandira Iye. Pemphero silimatsitsira Mulungu kwa ife, koma limatikweza ife kunka kwa Iye.

Pamene Yesu anali pa dziko lapansi, anaphunzitsa akuphunzira ace kupemphera. Iye anawalangiza kupereka zosowa zawo za tsiku liri lonse kwa Mulungu, ndi kutaya pa Iye nkhwawa zawo zonse. Ndipo citsimikizo cimene anawapatsa iwo ca kuti mapemphero awo adzamveka, ndi citsimikizo kwa ifenso.

Yesu mwini, pamene anali kukhala pakati pa anthu, kawiri kawiri anali kupemphera. Mpulumutsi wathu anadzilumikiza ndi zosowa ndi zofooka zathu, popeza anasanduka wopemphera ndi wodandaulira, kufuna mphamvu zatsopano kwa Atate wace, kuti aturuke wolimba kukomana ndi nchito ndi mayeso. Iye ndiye citsanzo cathu m'zinthu zonse. Mwa zofooka zathu Iye ndiye mbale wathu, “woyesedwa m'zonse monga momwe ife;” koma monga wopanda ucimo, makhalidwe ace anali opanda ucimo; Iye anapirira mabvuto ndi mazunzo a moyo m'dziko la ucimo. Umunthu wace unaliyesera pemphero cinthu cofunika ndi cabwino. Iye anapeza cisangalatso ndi cimwemwe pa kulankhula ndi Atate wace. Ndipo ngati Mpulumutsi wa anthu, Mwana wa Mulungu, anadziwa kuti asowa pemphero,

anthu ofooka, ocimwa, ayenera kudziwa kuti afunika pemphero loona losalekeza, koposa Iye.

Atate wathu wa kumwamba ali kulindira kutipatsa ife cidzalo ca madalitso ace. Ndi mwai wathu kuganzira kwambiri za kasupe wa cikondi cosatha. Ncozizwitsa ndithu kuti ife timape- mpha [70] pang'ono cotere! Mulungu ali wofulumira ndi wolola kumva pemphero la ana ace onyozeka, koma ife sitifuna kumuuza Mulungu zofuna zathu. Kodi angelo a kumwamba angaganize ciani za anthu osauka, ogonjera mayeso, pamene mtima wa Mulungu wa cikondi cosatha, uli kuwadandaulira iwo, ndi wofulumira kuwapatsa iwo koposa zimene angapemphe, kapena kuziganiza, koma iwo namangopemphera pang'ono cotere, ndi kacikhulupiriro kakang'ono cotere? Angelo amakonda kugwada pamaso pa Mulungu; amakonda kukhala pafupi ndi Iye. Iwo amaciyesera cimwemwe cawo copambana kulankhula ndi Jye. Koma ana a dziko lapansi, amene asowa kwambiri cithangato cimene Mulungu angawapatse, amayang'anika okwanitsidwa kungoyenda okha opanda kuwala kwa Mzimu wace, osatsagana naye kuli konse amukako.

Mdima wa woipayo umaphimba iwo amene aleka kupemphera. Mayeso onong'ona a mdaniyo amawanyenga iwo kucimwa; ndipo zonsezi zimacitika cifukwa iwo samapemphera monga Mulungu anawauza iwo. Kodi cifukwa ciani ana a Mulungu adzikana kupemphera, kwina pemphero liri mfungulo m'dzanja la cikhulupiriro yotsegulira nkhekwe ya kumwamba, kumene kuli cuma cosatha ca Mulungu? Wopanda pemphero losaleka, ndi kuyang'anira mwa cangu, tiri moopsa mwa kuti tidzayamba kugwa mphwayi ndi kupatuka pa njira ya coonadi. Mdaniyo masiku onse ali kufuna kutseka njira ya ku mpando wacifundo, kuti ife ndi pemphero ndi cikhulupiriro tisalandire cisomo ndi mphamvu ya kukana mayeso.

Alipo makhalidwe ace amene ife tingayembekezere kuti Mulungu adzamva ndi kuyankha mapemphero athu. Coyamba ndico kuti timve mu mtima kuti tisowa cithangato cocokera kwa Iye. Iye analonjeza, “Ndidzathira madzi pa amene ali ndi ludzu, ndi mitsinje pa nthaka youma.” (Yesaya 44: 3.) Iwo akumva njara ndi ludzu la cilungamo, amene afunafuna Mulungu, adziwitsitse kuti adzakhuta. Mtima utseguke kulandira mphamvu ya Mzimu, ukaleka kutero sudzalandira madalitso a Mulungu.

Umphawi wathu uli kutipembedzera ife kopambana kwa Mulungu. Koma tiyenera kufunafuna Ambuye tokha, kuti aticitire zinthu zimenezi. Iye ati, “Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu.” Ndipo “Iye amene sanatimana Mwana wace wa Iye yekha, koma anampereka cifukwa ca ife tonse adzalekeranji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?” (Mateyu 7: 7; Aroma 8: 32.)

[71] Ngati tingasamale zopanda pace m’mitima yathu; ngati tingaumirire coipa ciri conse codziwika, Ambuye sadzatimvera; koma pemphero la mtima wolapa ndi wodzicepetsa masiku onse lidzalandiridwa. Pamene takonza macimo onse amene tiwadziwa, tikhulupirire kuti mapemphero athu adzayankhidwa. Ubwino wa ife tokha sungathe kutilandiritsa ife cisomo ca Mulungu; kuyenera kwa Yesu ndiko kudzatipulumutse ife, mwazi wace ndiwo uti udzatsuke ife; komabe iripo nchito imene ife tiyenera kucita pofuna kulandiridwa.

Cinthu cina cimene cimapambanitsa pemphero ndico cikhulupiriro. “Iye wakudza kwa Mulungu adzikhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye.” (Heb. 11: 6.) Yesu anati kwa ophunzira ace, “Zinthu ziri zonse mukazifuna ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira ndipo mudzakhala nazo.” (Marko 11: 24.) Kodi timamkhulupirira Iye?

Citsimikizo cakuti, Ndipo ali wokhulupirika wakulonjezayo, ciri cacikuru ndi copanda malire. Ngati sitidalandire zinthu zomwe tapempha pa nthawi yomwe tapemphayo, tidzingokhulupirirabe kuti Ambuye wamva, ndi kuti adzayankha mapemphero athu. Ife ndife ocimwa ndi osaona za patsogolo kotero kuti nthawi zina timapempha zinthu zimene sizidzakhala madalitso kwa ife, ndipo Atate wathu wa kumwamba cifukwa ca cikondi amayankha mapemphero athu pa kutipatsa za ubwino wathu wopambana, — zimene ngakhale eni acefe tikazikonda, ngati ndi masomphenya a kumwamba tikadaona zinthu monga momwe ziri. Pamene mapemphero athu ayang’anika ngati sali kuyankhidwa, tingoumirira lonjezano; cifukwa nthawi ya kuyankha idzafikadi ndithu, ndipo tidzalandira madalitso amene tiwasowa koposa. Koma kunena kuti masiku onse pemphero lidzayankhidwa monga m’mene tapemphera, ndi kulandira cinthu ceni ceni cimene tacipempha, ndiko kumuyesa Iye. Mulungu ali wa nzeru sangaphophonyei, ndipo ali wabwino sangathe kumana kan-

thu kabwino kwa amene ayenda molunjika. Usaope kumkhulupirira Iye, ngakhale suona kuti mapemphero ako ali kuyankhidwa msanga msanga. Khulupirira lonjezano lace loona, “Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu.” (Mateyu 7: 7.)

Ngati tingamacite uphungu ndi zokaika zathu ndi mantha athu, kapena kuyesayesa kupeza kanthu kamene sitingathe kukaona bwino lomwe, tisanakhale ndi cikhulupiriro, mabvuto ndi nkhwana zidzangocuruka. Koma ngati tidza kwa Mulungu, tiri kumva mu mtima kuti sitingathe kudzithangata tokha monga momwe tiri, ndipo modzicepetsa, ndi cikhulupiriro tifotokoza zosowa zathu kwa Iye amene nzeru zace ziri zosatha, amene amaona zonse, ndi amene amalumulira zonse ndi cifuniro cace ndi mau ace, Iye adzamva kulira kwathu, ndipo adzalola kuunika kuwala m’mitima yathu. Ndi pemphero loona mtima ife timalumikizana ndi mtima wa Mulungu. Ngakhale tipande kudziwa nthawi imene Mombolo wathu ali kuwarama kuticitira cifundo ndi kutikonda ife, koma ziri zoonadi. Ngakhale tipande kumva kapena kuona kukhudza kwace, koma dzanja lace liri pa ife kutikonda ndi kutisamalira ife.

[72]

Pamene tidza kwa Mulungu kudzapempha cifundo ndi madalitso, tidzikhala nawo mzimu wa cikondi ndi wokhululukira m’mitima yathu. Tingathe bwanji kupemphera, “Mutikhululukire ife mangawa anthu, monga ifenso takhululukira a mangawa athu” (Mateyu 6: 12), kwina tiri nawo mzimu wosakhululukira? Ngati tiyembekeza kuti mapemphero athu amveke, tidzikhululukira anzathu cimodzimidzi monga ‘m’mene ife tiyembekeza kukhululukidwa.

Kucita khama m’pemphero ndiwo makhalidwe ena a kulandira. Ngati tifuna kukula m’cikhulupiriro ndi m’macitidwe tidzipemphera masiku onse. Ife “tidzilimbika cilimbikire m’kupemphera.” (“Citani khama m’kupemphera, nimudikire momwemo ndi ciyamiko.” (Aroma 12: 12; Akolose 4: 2.) Petro awadandaulira okhulupirira, “Khalani anzeru, ndipo dikirani m’mapemphero.” (1 Petro 4: 7.) Paulo atilangiza, “Komatu m’zonse ndi pemphero, ndi pembedzero pamodzi ndi ciyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu.” (Afilipi 4: 6.) Yuda ati, “Koma inu, okondedwa, ndi kupemphera mu Mzimu Woyera, mudzisunge nokha m’cikondi ca Mulungu.” (Yuda 20, 21.) Pemphero losaleka ndiyo mfundo yosaduka ya moyo ndi Mulungu, kotero kuti moyo wa Mulungu umadza m’moyo

mwathu, ndipo m'moyo mwathu mumaturuka ungwiro ndi kuyera mtima kubwerera kwa Mulungu.

Kuli kufunika kucita cangu m'pemphero; kanthu kena kasakupingeni inu. Yesetsani kuti kulankhula kwanu kumveke pakati pa Yesu ndi moyo wanu. Funani nthawi iri yonse yabwino yakuti mupite kumene kuyenera kucitika pemphero. Iwo amene ali kufunafunadi kulankhula ndi Mulungu, adzaoneka m'misonkhano yopemphera, ali okhulupirika kugwira nchito yawo, ndi ofunitsitsa kupeza zokoma zonse angathe kuzipeza. Iwo adzapambanitsa nthawi iri yonse ya kudziika okha kumene angalandire kuwala kocokera kumwamba.

[73] Tidzipemphera m'mabanja mwathu, ndipo koposa zonse, ti-saleke pemphero la mtseri; cifukwa ndiwo moyo wa mzimu wathu. Nkosatheka kuti moyo ukule ngati tileka kupemphera. Pemphero la mu msonkhano ndi la m'banja liri losakwana. Mtseri, tiyeni titsegule mitima yathu pamaso pa Mulungu. Pemphero la mtseri limamvedwa ndi Mulungu yekha wakumva pemphero. Khutu la munthu silifunika kumva mapemphero otere. M'pemphero la mtseri moyo uli mu ufulu kopanda zosokosa ndi zokopa maso. Mwa cete, koma moona mtima pemphero limakafika kwa Mulungu. Zidzakhala zokoma ndi zokhalitsa, mphamvu zocokera kwa Iye amene aona mtseri, amene khutu lace liri lotseguka kumva pemphero locokera mu mtima. Ndi cikhulupiriro ca cete ndi kudzicepetsa, moyo umalankhula ndi Mulungu, ndi kusonkhanitsa kuwala kocokera kumwamba kuupatsa mphamvu ndi kuulimbitsa kumenyana ndi Satana. Mulungu ndiye nsanja yathu ya mphamvu.

Pemphera m'cipinda cako; ndipo pamene uli kugwira nchito yako, tukula mtima wako kwa Mulungu nthawi zonse. Enoke anayenda ndi Mulungu coteru. Mapemphero acetewa amakwera monga zonunkhira patsogolo pa mpando wa cisomo. Satana sangathe kumgonjetsa munthu amene mtima wace wakhazikika mwa Mulungu coteru.

Palibe nthawi kapena malo oti mtima wotere sungathe kupemphera kwa Mulungu. Palibe kanthu kangatiletse ife kutukula mitima yathu mu mzimu wa pemphero loona. M'makamu a anthu a mu mseu, pakati pa zinchito, tingatumize pemphero kwa Mulungu, ndi kumpempha kuti atitsogolere, monga anacita Nehemiya pamene anapereka pempho lace patsogolo pa Mfumu Aritasasta. Cipinda

copempherera cingathe kupezeka kuli konse kumene tiri. Tidzitsegula khomo la mitima yathu kosaleka, ndi kumuitana Yesu kuti adze adzakhale monga mlendo wa kumwamba m' moyo mwathu.

Ngakhale potizungulira pali mpweya wowawa ndi wobvunda, sitifunika kupuma mpweya wace wowawawo, koma tingathe kupuma mpweya wangwiro wa kumwamba. Titsekere maganizo asaganize zonyansa ndi zoipa pa kutukula moyo wathu kunka pa maso pa Mulungu mwi pemphero loona. Iwo amene mitima yawo itseguka kulandira cithangato ndi dalitso la Mulungu adzayenda mu mpweya wopatulika koposa wa dziko lapansi, ndipo masiku onse adzalankhulana ndi Kumwamba.

Tisowa kumpenyetsetsa Yesu, ndi kuzindikira kokwana mtengo wa zinthu zosatha. Kukoma kwa kuyera mtima kuyenera kudzaze m' mitima ya ana a Mulungu; ndipo pofuna kucitika izi, tidzifunafuna cidziwitso ca zinthu za kumwamba.

Tiyeni tikweze moyo wathu kumwamba, kuti Mulungu atipatse ife mpweya wa kumwamba. Tiyeni tikhale pafupi ndi Mulungu, kuti mu yeso liri lonse lotidzidzimutsa maganizo athu atembenukire kwa Iye monga duwa limatembenukira ku dzuwa.

[74]

Onetsa zosowa zako, cimwemwe cako, zisoni zako, nkhawa zako, pamaso pa Mulungu. Sungathe kumlemetsa; sungathe kumtopetsa. Iye amene amawerenga tsitsi la pa mutu pako sali wosasamala zosowa za ana ace. “Ambuye ali wodzala cikondi ndi wacifundo.” (Yakobo 5: 11.) Mtima wace wacikondi umakhudzidwa ndi zisoni zathu, ngakhale pamene tizinena. Muuze zonse zakubvuta mtima wako. Palibe cacikuru cosanyamulika ndi Iye, cifukwa Iye amagwiriziza maiko, amalamulira zonse m' maiko onse. Kali konse kotipatsa ife mtendere sikakhala kakang'ono pa maso pace. Palibe mau ena m' zolembedwa za macitidwe athu zimene ziri zozimirira kuti Iye sangathe kuziwerenga; palibe cobvuta cimene Iye sangathe kucikonza. Palibe cobvuta cimagwera ana ace, kapena nkhawa ya mtima, kapena cimwemwe, kapena pemphero, zimene Atate wathu saziona ndi kuzisamala msanga. “Aciritsa osweka mtima namanga mabala awo.” (Salmo 147: 3.) Ciyanjano pakati pa Mulungu ndi moyo uli wonse ndi coona ndi codzaza monga ngati palibenso moyo wina umene Iye anaperekerwa Mwana wace wokonedwa.

Yesu anati, “Mudzapempha m' dzina langa; ndipo sindinena kwa inu kuti Ine ndidzakufunsirani inu kwa Atate; pakuti Atate yekha

akonda inu.” “Ine ndinakusankhani inu... kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m’dzina langa, akakupatseni inu.” (Yohane 16: 26, 27; 15: 16.) Koma kupemphera m’dzina la Yesu kuli koposa kungochula dzinalo poyamba ndi pomariza pemphero. Koma kupemphera mu mtima ndi mu mzimu wa Yesu, tiri kukhulupirira malonjezano ace, kutsamira pa cisomo cace, ndi kugwira nchito zace.

Mulungu satanthauza kuti ali yense wa ife atokhala pa yekha ndi kudzipatula ku dziko m’ malo mwa kudzipereka ku nchito za cipembedzo. Moyo udzikhala monga moyo wa Kristu, — pakati pa mapiri ndi makamu a anthu. Iye amene sacita kanthu kena koma kungopemphera, posacedwa adzaleka kupempherako, kapena mapemphero ace adzangosanduka ngati mwambo. Pamene anthu adzipatula m’ moyo wa kusonkhana, ndi m’ nchito ya Cikristu ndi kunyamula mtanda wace; pamene iwo aleka kugwira mokhulupirika nchito ya Mpu-lumutsi, amene anawagwirira nchito mokhulupirika, iwo amataya mutu wa pemphero, ndipo alibe mtima wa kudzipereka. Mapemphero awo amangokhala a iwo okha. Iwo sangathe kupempherera zosowa za anthu, kapena kumanga ufumu wa Kristu, kupempherera mphamvu zogwira nazo nchito.

[75]

Tiri kumwaza pamene ife sitigwirizana ndi kulimbitsana mphamvu ndi kulimbitsana mitima m’ nchito ya Mulungu. Coonadi ca mau ace cimataya mphamvu yace ndi kufunika kwace m’ mitima yathu. Mitima yathu imaleka kuwalitsidwa ndi kudzutsidwa ndi mphamvu yace ya kuyeretsa, ndipo timafa mwa uzimu. Timataya ciyanjano cathu ca Cikristu cifukwa ca kusowa kucitirana cifundo wina ndi mnzace. Iye amene ali kungodzitsekera kwa iye yekha sali kudzaza malo amene Mulungu afuna kuti iye adzaze. Ngati tingakuze ciyanjano cimene ciri m’ makhalidwe athu cidzatiyanjanitsa ndi anzathu, ndipo cidzaticulitsa ndi kutilimbitsa ife m’ nchito ya Mulungu.

Ngati Akristu angalumikizane pamodzi, namalankhulana za cikondi ca Mulungu, ndi za coonadi ca ciombolo, mitima yawo idzatsitsimuka, ndipo adzatsitsimutsana. Tidziphunzira zambiri tsiku liri lonse za Atate wathu wa kumwamba, ndi kupeza macitidwe atsopano a cisomo cace; pompo tidzafuna kulankhula za cikondi cace; ndipo pamene tiri kucita izi, mitima idzathedwa ndi kulimbitsidwa. Ngati tikadamaganiza ndi kulankhula zambiri

za Yesu koposa za ife tokha, tikadakhala nawo maonekedwe ace ocuruka.

Tikadamaganiza za Mulungu kawiri kawiri, monga momwe timaona cisamaliro cace pa ife, mwenzi tiri kumsunga m’aganizo athu, ndi kukonda kulankhula za Iye, ndi kumlemekeza Iye. Timalankhula za dziko cifukwa timakondwera nazo. Timalankhula za abwenzi athu cifukwa timawakonda; zokondwa zathu ndi zisoni zathu zamangika pamodzi ndi iwo. Koma tiri ndi cifukwa cacikuru coyenera kukonda Mulungu koposa kukonda abwenzi athu a pa dziko lapansi; ndipo ciyenera kukhala cinthu cozolowereka koposa zonse m’dziko lapansi kumuyesa Iye woyamba m’aganizo athu onse, kulankhula za ubwino wace ndi kufotokoza za mphamvu zace. Mphatso zolemera zimene anatipatsa ife sizinali zakuti zimeze cikondi cathu ndi maganizo athu, kuti ife tisakhale ndi kanthu kakupereka kwa Mulungu; izo ziri za kutikumbutsa kosaleka za Iye, ndi kutimanga ife ndi nsinga za cikondi ndi kuyamika Atate wathu wa kumwamba. Tiri kumiriritsa za dziko lapansi. Tiyeni titukule maso athu ku khomo lotseguka la kacisi wa kumwamba, kumene kuwala kwa ulemerero wa Mulungu kumawala m’nkhope ya Kristu, amene “akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye.” (Heb. 7: 25.)

Tifunika kumlemekeza Mulungu kwambiri “cifukwa ca ubwino wace, ndi cifukwa ca nchito zace zodabwitsa kwa ana a anthu.” 2 (Salmo 107: 8.) Macitidwe athu a cipembedzo asama- ngokhala [76] kupempha ndi kulandira kokha. Tisamangoganizira za zosowa zathu zokha, osaganizanso za zabwino tiri kulandira. Si kuti tiri kupfempheretsai, koma kuti tiri kuperewera kupereka mayamiko. Tiri kulandira za cifundo za Mulungu masiku onse, koma timangomthokoza pang’ono pokha, timamtamanda pang’ono cifukwa ca zimene Iye waticitira ife.

Kale Yehova anauza Israyeli, pamene anasonkhana ku utumiki wace, “Muzidya pamaso pa Yehova Mulungu wanu, kukondwera nazo zonse mudazigwira ndi dzanja lanu, inu ndi a pa banja lanu, m’mene Yehova Mulungu wanu anakudalitsani.” (Deut. 12: 7.) Cimene cicitika cifukwa ca kulemekeza Mulungu cidzicitika ndi cikondwerero, ndi nyimbo za kuyamika, osati ndi cis’oni.

Mulungu wathu ali Atate wacifundo. Utumiki wace usamayang’anidwa monga wobvuta ndi womvetsa cisoni. Cidzikhala

cikondwero kupembedza Yehova, ndi kutenga mbali mu nchito yace. Mulungu safuna kuti ana ace, amene anawapatsa cipulumutso cacikuru cotere, kuti iwo adzicita ngati Iye ali Mbuye wobvuta wa nkharwe. Iye ndiye bwenzi lawo lopambana; ndipo pamene iwo ampembedza Iye, Iye ayembekeza kukhala nawo, kuwadalitsa ndi kuwasangalatsa iwo, ndi kudzaza mitima yawo ndi cimwemwe ndi cikondi. Yehova afuna kuti ana ace adzisangalatsidwa mu nchito yace, ndi kupeza cikondwerero koposa zobvuta mu nchito yace. Iye afuna kuti iwo amene adza kumpembedza Iye adzitenga maganizo abwino za cikondi cace ndi cisamaliro cace, kuti adzikondwera ndi nchito zorise za moyo wawo, kuti akhale ndi cisomo cakucita mokhulupirika ndi moona mtima m'zinthu zonse.

Tiyenera kusonkhana kuzungulira mtanda. Kristu ndi Iye wopacikwa adzikhala coganiza cathu cacikuru, colankhula cathu, ndi cimwemwe cathu copambana. Tidzisunga m'maganizo athu dalitso liri lonse limene talandira kwa Mulungu, ndipo pamene ife tizindikira cikondi cace cacikuru, tidzikhala olola kupereka kanthu kali konse ku dzanja limene linakhomeredwa pa mtanda cifukwa ca ife.

Moyo ukwere kuyandikira kumwamba ndi mapiko a ciyamiko. Mulungu amapembedzedwa ndi nyimbo m'mabwalo a kumwamba, ndipo pamene ife tiri kutsimikiza mayamiko athu, tiri kuyandikira ku cipembedzo ca angelo a kumwamba. “Wopereka nsembe ya ciyamiko andilemekeza Ine.” (Salmo 50: 23.) Tiyeni, ndi cimwemwe colemekeza tidze patsogolo pa Mlengi wathu, ndi

[77] “mayamikiro ndi mau a nyimbo yok(? ma.” (Yesaya 51: 3.)

MUTU 12—COCITA NAKO KUKAIKA

AMBIRI, makamaka iwo amene ali atsopano m'moyo wa Cikristu, nthawi zina amabvutika ndi maganizo a cikaiko. Ziripo zinthu zambiri m'Bible zimene sangathe kuzifotokoza, kapena kuzimvetsetsa, ndipo Satana amacita ndi zimenezi kugwedeza cikhulupiriro cawo M'malembo monga ngati ndi bvumbulutso kokokera kwa Mulungu. Iwo amafunsa, “Kodi ndidzaidziwa bwanji njira yabwino? Ngati Bible ali Mau a Mulungudi, nanga ndidzamasolidwa bwanji ku zokaikazi ndi zobvutazi?”

Mulungu samatiuza ife kukhulupirira, wosatipatsa umboni wokwana kukhazikapo cikhulupiriro cathu. Kukhazikika kwace, makhalidwe ace, coonadi ca mau ace, wonsewu ndi umboni wokhazikika umene umatitsimikizira m'mitima yathu; ndipo umboni umenewu uli wocuruka. Komabe Mulungu sanacotse zokaikitsa. Cikhulupiriro cidzikhazikika pa umboni osati pa zosonyeza. Iwo amene afuna kukaika adzaipeza nthawi; pamene iwo amene afunadi kudziwa coonadi, adzapeza umboni wokwana pokhazikitsapo cikhulupiriro cawo.

Ncosatheka nzeru za anthu kuzindikira kokwana makhalidwe kapena nchito za Mulungu Wosatha. Ngakhale kwa anzeru, ndi ophunziritsa, Woyerayo amaoneka mwa cimbuuzi ndi mwa cinsinsi. “Kodi ukhoza kupeza Mulungu mwa kufunafuna? Ukhoza kupeza Wamphamvuyonse motsindika? Kumpeza kutanimpha ngati kumwamba, ungacitenji? Kuzama ngati ku manda ungadziwenji?” (Yobu 11: 7, 8.)

Mtumwi Paulo ati, “Ha! kuya kwace kwa kulemera ndi kwa nzeru ndi kwa kudziwa kwace kwa Mulungu! Osasanthulikadi maweruzo ace, ndi njira zace nzosalondoleka!” (Aroma 11: 33.) Koma ngakhale “pomzinga pali mitambo ndi mdima, cilungamo ndi ciweruzo ndizo zolimbitsa mpando wacifumu wace.” (Salmo 97: 2.) Tingathe kuzindikira macitidwe ace ndi ife, ndi njira zimene agwira nazo nchito, kuti ife tizindikire cikondi ndi cifundo cosatha columikizana ndi mphamvu yosatha. Tingathe kuzindikira zambiri

za nchito zace zonga zomwe ziri za ubwino wathu kuzidziwa; koma koposa izi tidzingozisiya m’manja okhoza kucita zonse, ndi mtima wodzala ndi cikondi.

[78] Mau a Mulungu, monga makhalidwe a Mwini wace, amaonetsa zinsinsi zimene sizingathe kuzindikirika kokwana ndi anthu. Malowedwe a ucimo m’dziko, kubadwa m’thupi kwa Kristu, kubadwanso, kuuka kvva akufa, ndi maphunzitso ena ambiri a m’Bible, ali zinsinsi zakuya zoti munthu sangathe kuzifotokoza, kapena kuzizindikira kokwana. Koma tiribe cifukwa ca kukaikira Mau a Mulungu cifukwa ca kuti sitingathe kuzindikira zinsinsi za ukuru wace. M’dziko lathu lomwe lino tazungulidwa ndi zinsinsi zimene sitingathe kuziyeza. Makhalidwe a moyo ngakhale ang’ono kwambiri ali obvuta kwambiri kotero kuti ngakhale anzeru kopambana alibe mphamvu kuwafotokoza. Kuli konse kuli zozizwa zimene sitingathe kuzidziwa. Nanga tidzizizwa kodi popeza kuti m’dziko la uzimu zirimonso zinsinsi zimene ife sitingathe kuziyeza? Bvuto lace makamaka liri m’kufooka ndi kucepa kwa nzeru za anthu. Mulungu anatipatsa ife M’malembo umboni wokwana za makhalidwe ace a umulungu, ndipo ife tisamakaika Mau ace cifukwa ca kuti sitingathe kuzindikira zinsinsi zonse za ukuru wace.

Mtumwi Petro ati kuti M’malembo “muli zina zobvuta kuzizindikira, zimene anthu osaphunzira ndi osakhazikika apotoza ... ndi kudziononga nawo eni.” (2 Petro 3: 16.) Zobvuta za Malembo zimakakamizidwa ndi kukaika monga zokangana ndi Bible; koma sizotero konse, izo ndizo umboni wolimba kuti adaperekedwa ndi Mulungu. Mukadakhala mopanda ciwerengero ca Mulungu koma zimene tingathe kuzizindikira mofewa; ngati ukuru wace ndi ufumu wace ukadazindikirika ndi nzeru za anthu, Bible sakadanyamula umboni wosalakwa vva ulamuliro wa Mulungu. Kukoma kwace ndi cinsinsi cace ca mitu yolembedwamo, ziyenera kukulitsa cikhulupiriro cathu kuti ndiwo Mau a Mulungu.

Bible amaulula coonadi mofewa ndi mwangwiwo moyenera zosowa ndi zolakalaka za mtima wa munthu, cimene cinadabwitsa anthu ophunzira kwambiri, kvvina cimathangata odzicepetsa ndi osaphunzira kuzindikira njira ya cipulumutso. Ndipo cikhaliirebe coonadi cofewaci ciri ndi maphunzitso okwezeka, ofika patari osatha, opitirira nzeru za anthu, kotero kuti ife tingathe kuwalandira ivvo cifukwa Mulungu ndiye anawafotokoza. Ndimu m’mene

nzeru ya ciombolo inatsegulidwira kwa ife kuti munthu ali yense aone mapazi amene ayenera kuponda pa kulapa kunka kwa Mulungu, ndi cikhulupiriro ca kwa Ambuye wathu Yesu Kristu, kuti tipulumustidwe mu njira yoikika ndi Mulungu; komabe pansipa pa zoonadi izi; zozindikirika mofewa cotere, pali zinsinsi zimene zimabisa ulemerero wace, —zinsinsi zotopesta malingaliro pakuzifunafuna, koma zakumpatsa cikhulupiriro wakufunafuna coonadi ndi mtima woota. Akamasa- nthula Bible kuvvambiri, atsimikizidwanso kwambiri kuti ndiwo mau a Mulungu wa moyo, ndipo ciweruzo ca munthu cimagonja patsogolo pa ukuru wa bvumbulutso la Mulungu.

[79]

Kuzindikira kuti sitingathe kuzindikira kokwana zoonadi zazikuru za Bible, uku ndiko kubvomera kuti nzeru za munthu wopita msanga siziri zokwana kuzindikira zosatha; kuti munthu, ndi nzeru zace zakutha msanga, za umunthu, sangathe kuzindikira nchito za Mulungu Wodziwa zonse.

Popeza sangathe kudziwa zinsinsi zace zonse, okaika ndi osakhulupirira amakana mau a Mulungu; ndipo si onse amene akhulupirira Bible ali opulumuka ku coopsa ici. Mtumwi ati, “Tapenyani, abale, kuti kapena ukakhale mwa wina vva inu mtima wacipa wosakhulupirira, wa kulekana ndi Mulungu wa moyo.” (Heb. 3: 12.) Nkwabwino kuphunzira kolimba maphunzitso a Bible, ndi kusanthula “zakuya za Mulungu” (1 Akor. 2: 10), monga momvve ziri kuonetsedwa M’malembo. Ngakhale “zinsinsi nza Yehova Mulungu vvathu,” “zobvumbuluka nza ife.” (Deut. 29:29.) Koma ndi nchito ya Satana kupatutsa mphanvu ya kusankha ya mtima. Kunyada kumasanganizika ndi maganizo a coonadi ca Bible, kotero kuti anthu amakvviya ndi kugonjetsedwa ngati sangathe kufotokoza mbali iri yonse ya Malembo monga afuna. Ciri ca manyazi kwa iwo kubvomera kuti sali kumvetsetsa mau a Mulungu. Sali olola kulindira mopirira kufikira Mulungu adzaone kuti nkoyenera kuululira coonadi kwa iwo. Ivvo amaganiza kuti nzeru zawo zosathangatidwa za umunthu ziri zokwana kuwazindikiritsa iwo malembo, ndipo polephera kucita izi, iwo amakana konse ulamuliro wace. Nzoonadi kuti maganizo ndi maphunzitso amene anthu ambiri amaganiza kuti amacokera m’ Bible alibe maziko awo m’ maphunzitso ace, ndipo ndithu ali osiyana ndi mau a uzimu. Zinthu izi zidacititsa kukaika ndi nkhwawa m’mitima yambiri. Koma

sizimacitika cifukwa ca Mau a Mulungu, koma cifukwa ca kuti munthuyo ali kupotoza.

Cikadakhala cotheka kuti anthu olengedwa adzilandira nzeru zokwana kudziwa Mulungu ndi nchito zace, pompo atafika pamenepa, si bwenzi ali kupezanso coonadi, kapena kukula m'cidziwitso, kapena kukula m'malingaliro ndi mu mtima. Mulungu sakadakhalanso wamkulu; ndipo munthu, atafika cimaliziro ca cidziwitso, akadaleka kukula. Tiyeni tiyamike Mulungu kuti siziri zotero. Mulungu ali wosatha; mvva Iye muli “zolemera zonse za nzeru ndi cidziwitso.” (Akolose 2: 3.) Ndipo ku nthawi zonse anthu ati adzidzangosanthula, namangophunzira, koma osatsiriza zolemera za nzeru zace, za ubvino wace, ndi za mphamvu zace.

[80]

Mulungu afuna kuti ngakhale m'moyo uno coonadi ca Mau ace cidziululidwa kwa anthu ace. Iripo njira imodzi yokha imene tingalandirire cidziwitsoci. Tingathe kulandira cizindikiritso ca mau a Mulungu ndi kuunika kwa Mzimu amene anapereka Mauwo. “Zinthu za Mulungu palibe wina azidziwa, koma Mzimu wa Mulungu;” “pakuti Mzimu asanthula zonse zakuya za Mulungu zomwe.” (1 Akorinto 2: 10, 11.) Ndipo lonjezano la Mpulumutsi kwa ophunzira ace linali, “Pamene atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi adzat-sogolera inu mwa coonadi conse.... Pakuti adzatenga za kwa Ine nadzazilalikira kwa inu.” (Yohane 16: 13, 14.)

Mulungu afuna kuti munthu adzicita nazo mphamvu zace za kuganiza; ndipo kuphunzira Bible kudzalimbisa ndi kudzutsa malingaliro koposa kuphunzira kanthu kena. Ngati sitifuna kuti Malembo angokundikana m'malingaliro athu, kotero kuti sitingathe kuzindikira coonadi cace, tidzikhala ndi cikhulupiriro conga ca mwana, ofulumira kuphunzira, ndi kupempha cithangato ca Mzimu Woyera. Pozindikira mphamvu ndi nzeru za Mulungu, ndi kuperewera kwathu kuzindikira ukuru wace, zidzitidzaza ife ndi kufatsa, ndipo tidzitsegula mau ace, monga tiri kulowa pamaso pace, ndi kuopa koyera. Pamene tidza ku Bible, maganizo adzizindikira ulamuliro waukuru koposa, ndipo mtima ndi nzeru zidzigwadira INE NDINE wamkuru.

Ziripo zinthu zambiri zobvuta kapena zobisika, zimene Mulungu adzazifotokoza ndi kuzifewetsa kwa iwo amene afuna kuzizindikira. Koma wopanda citsogozo ca Mzimu Woyera, tidzingopotozabe Malembo. Ziripo zowerenga zambiri za Bible zimene sizipindulitsa,

ndipo mwambiri zimapweteka kopambana. Pamene Mau a Mulungu atsegulidwa wopanda ulemu ndi wopanda pemphero; pamene maganizo ndi cikondi sizimangirira pa Mulungu, kapena kugwirizana ndi cifuniro cace, mtima umadzazidwa ndi kukaika; ndipo m'kuphunzira Bible mumaturukanso kusakhulupirira. Mdaniyo amalamulira maganizo, ndipo amatiuza matanthauzo amene sali abwino. Pamene anthu sali kufuna kugwirizana ndi Mulungu m' mau ndi m'nchito zawo, pompo, ngakhale ali ophunzira kwambiri, adzacimwa pozindikira malembo, ndipo si kuli kwabwino kukhulupirira mafotokozo awo. Iwo amene ayang'ana malembo kupezamo zosiyana alibe maso a uzimu. Ndi masomphenya okhota adzaona zinthu zambiri zokaikitsa ndi kusakhulupirira m' zinthu zimene ziri zomveka bwino ndi zofewa.

Ngakhale acite cizimiza mphoyo, cifukwa ceni ceni ca kukaika ndi kusakhulupirira, ndico cikondi ca zoipa. Maphunzitsos ndi malangizo a Mau a Mulungu sali abwino kwa mtima wonyada ndi wokonda zoipa, ndipo amene sali olola kumvera zofunsa zace ali ofulumira kukaika za ulamuliro wace. Ngati tifuna kucifika coonadi, tidzikhala ndi cifuniro coona kudziwa coonadi, ndi mtima wolola kucimvera. Iwo amene aphunzira Bible ndi mzimu wotere, adzapeza umboni wocuruka kut. i ali Mau a Mulungu, ndipo adzapeza cizindikiritso ca coonadi cimene cidzawapatsa iwo nzeru kufikira cipulumutso.

[81]

Kristu anati, “Ngati munthu ali yense afuna kucita cifuniro cace, adzazindikira za ciphunzitsoco.” (Yohane 7: 17.) M'malo mwa kufunsa ndi kupeza zifukwa ndi zimene suzimvetsetsa, samalira kuwala kumene walandira kale, ndipo udzalandira kuwala kocuruka. Ndi cisomo ca Kristu, cita nchito iri yonse imene uli kuizindikira, ndipo udzakhoza kuzindikira ndi kucita zimene uli kuzikaika tsopano.

Ulipo umboni umene uli wotseguka kwa onse, — ophunziritisa, ndi osaphunzira konse, — ndiwo umboni wa macitidwe. Mulungu atiitana ife kuti tiyese tokha kuonadi kwa Mau ace, ndi coonadi ca malonjezano ace. Iye atiuza ife, “Talawani, ndipo muone kuti Yehova ndiye wabwino.” (Salmo 34: 8.) M'malo mwa kutsa mira pa mau a munthu wina, tilawe tokha. Iye ati, “Pempham, ndipo mudzalandira.” (Yohane 16: 24.) Malonjezano ace adzakwanitidwa. Sanalephere ndi kale lonse; ndipo sangalephere konse. Ndipo pamene ife tiri kuyandikira kwa Yesu, ndi kukondwera m'cidzalo ca

cikondi cace, kukaika kwathu ndi mdima zidzakanganuka cifukwa ca kuwala kwa nkhope yace.

Mtumwi Paulo ati kuti Mulungu “anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutilowetsa m’ufumu wa Mwana wa cikondi cace.” (Akolose 1: 13.) Ndipo ali yense amene wapitirira kucokera ku imfa kunka ku moyo, ali wokhoza kuikapo cizindikiro cace kuti Mulungu ali woona.” (Yohane 3: 33.) Angathe kucitira umboni, “Ndinasowa cithangato, ndipo ndinacipeza mwa Yesu. Cosowa ciri conse cinapatsidwa, njala ya mtima wanga inakwanitsidwa; ndipo tsopano kwa ine Bible ali bvumbulutso la Yesu Kristu. Kodi uli kufunsa cifukwa ciani ndimakhulupirira mwa Yesu? —Cifukwa kwa ine ali Mpulumutsi wa kumwamba. Cifukwa ciani ndimakhulupira Bible? — Cifukwa ndapeza kuti ndiwo mau a Mulungu kwa moyo wanga.” Tidzakhala nawo umboni mwa ife tokha kuti Bible ali woona, kuti Kristu ali Mwana wa Mulungu. Ife tidziwa

[82] kuti sitiri kutsata miyambi yocenjerera.

Petro adandaulira abale ace kuti “akule m’cisomo, ndi m’ cidziwitso ca Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu.” (2 Petro 3: 18.) Pamene anthu a Mulungu ali kukula m’cisomo, adzalandira kosaleka cizindikiritso ca Mau ace. Adzazindikira kuwala kwatsopano ndi ubwino m’coonadi copatulika. Zimenezi zinali zoonadi m’mwambi wa mpingo m’mibadwo yonse, ndipo zidzacticabe comweco kufikira cimaliziro. “Koma mayendedwe a olungama akunga kuunika kwa mbanda kuca, kunkabe kuwala kufikira usana woti mbe.” (Miyambo 4: 18.)

Ndi cikhulupiriro tidzaona za mtsogolo, ndi kugwira mapangano a Mulungu a kukula kwa nzeru zathu, mphamvu za munthu kugwirizana ndi za Mulungu, ndi mphamvu zamoyo uli wonse kugwirizana ndi Kasupe wa kuunika. Tidzakondwera kuti zonse zimene zinali kutibvuta m’macitidwe a Mulungu zidzakhala zomveka; zinthu zobvuta kumva zidzafotokozedwa. Ndipo kumene mitima yathu inali kupeza cisokonekero ndi zosagwirizana. tidzaona kugwirizana kwangwiro ndi kwabwino. “Pakuti tsopano tipenya m’kalilore, ngati cimbuzi; koma pomwepo maso ndi maso: tsopano ndizindikira mdera mdera; koma pomwepo ndidzazindikiratu mon-

[83] ganso ndazindikiridwa.” (1 Akor. 13: 12.)

MUTU 13—KUKONDWERERA MWA AMBUYE

Ana a Mulungu aitanidwa kukhala oonetsera Kristu, kusonyeza ubwino ndi cifundo ca Ambuye. Monga Kristu anationetsera ife makhalidwe oona a Atate, coteri ifenso tinonetsere Kristu ku dziko losadziwa cikondi cace ndi cifundo cace. “Monga momwe munandituma Ine ku dziko lapansi,” anatero Yesu, “Inenso ndituma iwo ku dziko lapansi.” “Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine,... kuti dziko lapansi lizindikire, kuti Inu munandituma Ine.” (Yohane 17: 18, 23.) Mtumwi Paulo ati kwa akuphonzira a Yesu, “Popeza mwaonetsedwa kuti muli kalata wa Kristu,” “wodziwika ndi wowerengedwa ndi anthu onse.” (2 Akor. 3: 3, 2.) Mwa mwana wace ali yense, Yesu amatumiza kalata ku dziko lapansi. Ngati uli wotsata Kristu, Iye watumiza kalata mwa iwe kunka ku banja, ku mseu, kumene iwe uli kukhala. Yesu, pokhala mwa iwe, afuna kulankhula ndi mitima ya iwo amene asanamdziwe. Kapena iwo sawerenga Bible, ndi kumva mau amene ali kulankhula nawo m’masamba ace; saona cikondi ca Mulungu mwa nchito zace. Koma ngati iwe uli woonetsera wa Yesu woota, kapena kupyolera mwa iwe iwo adzatsogozedwa kuzindikira za ubwino wace, nakopedwa kumkonda Iye ndi kumtumikira.

Akristu alikidwa monga onyamula miyuni pa njira ya kumwamba. Iwo adzionetsera ku dziko kuunika kumene kuli kuwala pa iwo kucokera kwa Kristu. Moyo wawo ndi makhalidwe awo adzikhala otero kuti kupyolera mwa iwo ena adziona mokoma za Kristu ndi nchito zace.

Ngati tionetseradi Kristu, tidzicititsa nchito yace kukhala yokopa monga momwe iri. Akristu amene amangocita cisoni m’moyo mwawo, namangong’ung’udza ndi kudandaula, ali kuwapatsa anzawo maonekedwe onyenga a Mulungu ndi a moyo wa Cikristu. Iwo ali kupereka citsimikizo ca kuti Mulungu sakondwera kuti ana ace adzikondwa, ndipo mwa ici amacitira umboni wonama kutsutsana ndi Atate wathu wa kumwamba.

Satana amakwezeka pamene iye angathe kutsogolera ana a Mulungu kusakhulupirira ndi kugwa mphwayi. Iye amakondwera ku-

[84] tiona ife tiri kuleka kukhulupirira Mulungu, tiri kukaika za kulola kwace ndi mphamvu zace za kutipulumutsa ife. Iye amakonda kuti ife tidziganiza kuti Yehova adzatipweteka ife ndi mphamvu zace. Nchito ya Satana ndiyo kuonetsera Ambuye ngati wopanda cifundo. Iye amakhotetsa coonadi cace. Amadzaza mitima yathu ndi maganizo onyenga a za Mulungu; ndipo m'malo mwa kuti tidziganizira coonadi za Atate wathu wa kumwamba, kawiri kawiri timamangirira maganizo athu pa zonyenga za Satana, ndi kuny-oza Mulungu pa kusamkhulupirira ndi kumng'ung'udzira. Satana afuna kuti moyo wa cipembedzo udzikhala wa cisoni. Iye afuna kuti udziona kera wa nchito ndi wobvuta; ndipo pamene Mkristu aonetsera m'moyo wace maonekedwe otere a cipembedzo, nayenso, cifukwa ca kusakhulupirira kwace, ali kucitanso bodza la Satana.

Ambiri, poyenda pa njira ya moyo, amangoganiza za zocimwa zawo ndi zolephera zawo ndi zogwiritsidwa mwala zawo, ndipo mitima yawo imangodzazidwa ndi cisoni ndi kugwa mphwayi. Pamene ndinali ku Europe, mlongo wina amene anali kucita zotere, ndi amene anali m'mabvuto akuru, analemba kwa ine, kundipempha mau a kulimbitsa mtima. Usiku wace nditalandira kale kalatayo, ndinalota kuti ndinali m'munda, ndipo amene anali kuoneka ngati mwini wa mundawo, anali kunditsogolera ine m'njira zace. Ndin-ali kusunghanitsa maluwa ndi kukondwera ndi kununkhira kwawo, pamene mlongo ameneyu, amene anali kuyenda pa mbali panga, anandiitana kuti ndione minga yosaoneka imene inapinga mtsogolo mwace. Iye anali kungolira ndi kucita cisoni. Iye sanali kuyenda m'njira, kutsatira mtsogoleri, koma anali kuyenda pakati pa minga. "Mai'ne," iye analira, "Kodi si za cisoni kuti munda wabwinowu udzionongeka ndi minga?" Pompo mtsogoleriyo anati, "Isiye min-gayo, cifukwa ingokupweteka. Sonkhanitsa maluwawo."

Kodi sanalipo maanga ena owala m'macitidwe ako? Kodi unal-ibe nthawi zina zimene mtima wako unali kugunda ndi cimwemwe pa kuyankha Mzimu wa Mulungu? Pamene uyang'ana m'mbuyo mwa macitidwe a moyo wako, kodi sumapeza macitidwe ena okondweretsa? Kodi malonjezano a Mulungu, sali ngati maluwa onunkhira, okula pa mbali iri yonse ya njira yako? Kodi sungalole kuti kukoma kwawo ndi kununkhira kwawo kudzaze mtima wako ndi cimwemwe?

Minga idzangokupweteka ndi kukumvetsa cisoni; ndipo ngati ungosonkhanitsa zokhazi, ndi kuzionetsa kwa ena, kodi pamodzi ndi kucepetsa ubwino wa Mulungu kwa iwe wekha, suli kuwaletsa iwo akukuzungulira kuyenda m'njira ya moyo?

Siciri ca nzeru kusonkhanitsa maganizo onse osakondweretsa a moyo wa kale, — zoipa zace ndi zolephera zace, — kuzilankhula ndi kulira cifukwa ca izo kufikira tigwa nazo mphwayi. Moyo wa kugwa mphwayi uli wodzazidwa ndi mdima, uli kudzitsekera wokha kuwala kocokera kwa Mulungu, ndiponso uli kuponya mthunzi pa njira ya ena. [85]

Thokozani Mulungu cifukwa ca zithunzithunzi zowala, zimene wationetsera ife. Tiyeni tikundike pamodzi zitsimikizo zodala za cikondi cace, kuti tidziziyang'ana nthawi zonse. Mwana wa Mulungu kusiya mpando wa cifumu wa Atate wace, kubveka umulungu wace ndi umunthu, kuti apulumutse munthu ku mphamvu ya Satana; kutigonjetsera ife, kuwatsegulira anthu kumwamba, kuululira anthu cipinda kumene Mulungu amaonetsera ulemmerero wace; kutukulidwa kwa mtundu wolephera kuuturutsa m'dzenje limene ucimo udauponyamo, ndi kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu wosatha, ndipo atapirira yeso la kumwamba mwa cikhulupiriro ca mwa Mombolo wathu, abvekedwa m'cilungamo ca Kristu, ndi kukwezedwa kunka ku mpando wace wa cifumu — izi ndizo zithunzithunzi zimene Mulungu afuna kuti tidziziganizira.

Pamene tiri kukaika za cikondi cace, ndi kusakhulupirira malonjezano ace, tiri kumnyoza Iye ndi kumvetsa cisoni Mzimu wace Woyera. Kodi mai nkumva bwanji za ana ace amene masiku onse ali kungodandaula za iye, monga ngati iye sali kuwacitira zabwino, kwina moyo wace wonse ali kuyesetsa kuwacitira zabwino ndi za kuwasangalatsa? Kapena atakaika za cikondi cace; mtima wace udzasweka. Kodi kholo liri lonse nkumva bwanji ngati ana ace alicitira coteru? Nanga Atate wathu wa kumwamba adzaganiza bwanji za ife, pamene ife sitikhulupirira cikondi cace, cimene cinamtso-golera Iye kupereka Mwana wace wobadwa yekha, kuti ife tipeze moyo? Mtumwi alerriba cotere, “Iye amene sanatimana Mwana wace wa yekha, koma anampereka cifukwa ca ife tonse, adzalekeranji kutipatsanso ife zinthu zonse pamodzi ndi iye?” (Aroma 8: 32.)) Ndipo cikhaliirebe ambiri, ndi nchito zawo, ngakhale sali kunena

ndi mau awo, ali kunena kuti, “Ambuye sali kutanthauza izi kwa ine. Kapena akonda ena, koma sandikonda ine.”

[86] Zonsezi ziri kupweteka moyo wako womwe; cifukwa mau ali onse akukaika amene uli kulankhula, ali kuitana mayeso a Satana; ali kungokulimbikitsa kukaika, ndipo ali kukucotsera angelo otumikira. Pamene Satana akuyesa, usalankhule mau a kukaika kapena a mdima. Ngati usankha kumtsegulira, mtima wako udzadzazidwa ndi kusakhulupirira ndi mafunso opanduka. Ngati ulankhula maganizo ako, kukaika kuli konse kumene uli kulankhula si kumangobwerera pa iwe wekha, koma ndi mbeu imene idzamera ndi kubala zipatso m’moyo wa ena, ndipo cingadzakhale cosatheka kubweza citsanzo ca mau ako. Iwe wekha kapena ungapulumuke ku mayeso a Satana ndi ku msampha wace, koma ena, amene asocera ndi citsanzo cako, kapena sangakhoze kupulumuka ku kusakhulupirira kumene udawatsogolera. Nkofunika nanga kuti tidzilankhula zinthu zokhazokha za kupatsa mphamvu ndi moyo wa uzimu!

Angelo ali kumvetsera kuti amve mbiri imene uli kunyamula ku dziko za Ambuye wako wa kumwamba. Zolankhula zako zikhale za Iye amene ali nawo moyo wace cikhalire wa kukupembedzera kwa Atate. Ukagwira dzanja la bwenzi lako, m’milomo yako ndi mu mtima mwako mukhale zolemekeza Mulungu. Zimenezi zidzakopa maganizo ace kunka kwa Yesu.

Onse ali nawo mabvuto awo; za cisoni zobvuta kuzipirira, mayeso obvuta kuwakana. Usafotokoze mabvuto ako kwa anzako, koma fotokoza zonse kwa Mulungu m’pemphero. Uliyese lamulo lako kuti usalankhule konse ngakhale mau amodzi a kukaika kapena a kugwa mphwayi. Ungathe kucita zambiri kukondweretsa moyo wa ena ndi kulimbitsa nchito zawo, ndi mau a ciyembekezo ndi a cimwemwe coyera.

Alipo anthu ambiri olimba mtima amene ali kukanikizidwa ndi mayeso, ali pafupi kukomoka m’nkondo yomenyana ndi cifuniro cawo ndi mphamvu ya zoipa. Usamgwetse mphwayi wotereyu m’nkondo yace kobvuta. Mkondweretse ndi mau olimbika a ciyembekezo, akumlimbitsa pa njira yace. Potoero kuwala kvva Kristu kudzawala mwa iwe. “Palibe wina wa ife akhala kvva iye yekha.” (Aroma 14: 7.) Ndi citsanzo cathu cosadziwika ena adzalimbikitsidwa, kapena adzagwetsedwa mphwayi, ndi kulekana ndi Kristu ndi coonadi.

Alipo ambiri amene ali ndi maganizo oipa za moyo ndi makhalidwe a Kristu. Iwo amaganiza kuti Iye anali wopanda cikondi ndi cimwemwe, ndi kuti ali waukari, wa nkharwe, ndi wosakondwa. Mwambiri macitidwe onse a cipembedzo amacitidwa mawanga ndi maganizo acisoniwa.

Kawiri kawiri zimanenedwa kuti Yesu analira, koma sanaoneke ali kumwetulira. Zoonadi Mpulumutsi wathu anali munthu wa zisoni, ndi wozolowerana ndi zobvuta, cifukwa anatsegulira mtima wace ku matsoka a anthu. Koma ngakhale moyo wace unali wodzikana, ndi wakumva zowawa ndi nkhwawa, mzimu wace sunaphwanyike. Nkhope yace sinali kuonetsa cisoni ndi kubvutika, koma inali ya mtendere. Mtima wace unali kasupe wa moyo; ndipo kuli konse kumene Iye anapita, ananyamula mtendere, cimwemwe ndi kukondwa.

[87]

Mpulumutsi wathu anali woona mtima ndi wolimbikira, koma sanali wa cisoni ndi wa nkhope yoti lende. Moyo wa iwo amene amtsanza Iye udzakhala wodzazidwa ndi nchito yooka mtima; iwo adzazindikira katundu wawo. Cimpepulo cidzacotsedwa; sikudzakhalapo kukondwa kodzitama, kapena kujeda kwa cipongwe; koma cipembedzo ca Yesu cimapatsa mtendere wonga mtsinje. Sici-macotsa kuwala kwa cimwemwe, sicimaletsa kukondwa, kapena kudetsa nkhope yosangalala. Kristu sanadze kutumikiridwa, koma kutumikira; ndipo pamene cikondi cace cilamulira mu mtima, tidzatsatira citsanzo cace.

Ngati ife tingamaganiziritse za kusakoma mtima ndi zosalungama za ena, tidzapeza kuti ncosatheka kuwakonda iwo monga Kristu anatikonda ife; koma ngati tingamaganiziritse za cikondi cozizwitsa ndi cifundo ca Kristu ca kwa ife, mzimu womwewo udzapidanso kwa ena. Tidzikondana ndi kucitirana ulemu, osasamala zifukwa ndi zophophonya zimene sitingalephere kuziona. Tidzikhala odzicepetsa ndi osadzikhulupira tokha, ndipo tidzikhala opirira ndi zoipa za ena. Zimenezi zidzapha umbombo wonse, ndi kutipanga ife a mtima wacifundo ndi wopatsa.

Davide ati, “Khulupirira Yehova, ndipo cita cokoma, khala m’dziko ndipo tsata coonadi.” (Salmo 37: 3.) “Khulupirira Yehova.” Tsiku liri lonse liri nawo akatundu ace, nkhwawa ndi zobvuta zace; ndipo pamene ife tikomana, timakhala ofulumira kulankhula za mabvuto athu ndi mayeso athu. Coteru mabvuto ambiri amene

sali athu amalowa mu mtima, ndipo timacita mantha ambiri, ndi kulemedwa ndi nkhawa, koterokuti wina nkuganiza kuti tiribe Mpu-lumutsi wacifundo, wokonda, wofulumira kumva zofunsa zathu, ndi kutikhalira ife thandizo lopezekeratu m' nthawi iri yonse ya kusowa.

Ena masiku onse ali kungoopa ndi kubwerekera mabvuto. Tsiku liri lonse amazingidwa ndi zizindikiro za cikondi ca Mulungu; tsiku liri lonse ali kulandira ubwino wace koma iwo sasamala madalitso amenewa. Mitima yawo nthawi zonse iri kungoganiza za kanthu kena koipa, kamene ali kuopa kuti kadzaoneka; kapena kobvuta kena kangaonekedi, kamene, ngakhale kali kakang'ono, kamatseka maso awo osaona zinthu zambiri zimene ayenera kuyamikira. Zobvuta zimene amakomana nazo, m' malo mwa kuti ziwapitikitsire kwa Mulungu, amene ali kasupe wa cithangato cawo, zimawalekanitsa ndi Iye, cifukwa iwo amangobvutika ndi kung'ung'udza.

[88] Kodi tiri kucita bwino pa kukhala osakhulupirira coterokuti? Kodi cifukwa ciani tidzikhala osayamika ndi osakhulupirira? Yesu ndiye bwenzi lathu; Kumwamba konse kumakondwera kuticitira ife zabwino. Tisamalola zobvuta ndi nkhawa za tsiku liri lonse kubvuta mtima ndi kuticititsa tsinya. Ngati titero, masiku onse tidzakhala nako kanthu kakutibvuta ndi kutitopetsa. Tisamangocita nkhawa zimene zimangotibvuta ife ndi kutitopetsa, koma zosatithangata kupirira mayeso.

Ungakhale ubvutike m' nchito yako; ciyembekezo cako cimanka cideradera, nuopsedwa kuti udzataya; koma usagwe mphwayi taya nkhawa zako pa Mulungu, nungokhala cete ndi kukondwera. Pemphera nzeru kuti udzicita nchito yako mwa luso, ndipo potero, udzaletsa kutaika ndi kuonongekako. Cita zonse monga ungakhoze kupeza zabwino. Yesu analonjeza kuti adzatithangata, ngati ife tiyetsa. Ngati, utatsamira pa Mthandizi wakoyo, wacita zonse monga ungate, landira zomwe wapezazo mokondwa.

Si cifuniro ca Mulungu kuti anthu ace adziponderezedwa ndi nkhawa. Koma Ambuye wathu satinyenga ife. Samanena kwa ife, "Usaope; mulibe zoopsa m' njira mwako." Iye adziwa kuti alipo mayesero ndi zoopsya, ndipo amacita nafe bwino lomwe. Iye samanena kuti adzawaturutsa anthu ace m' dziko la zoipali, koma amangowalozera ku cikopa cosalephera. Pemphero lace kwa akuphunzira ace linali la kuti, "Sindipempha kuti muwacotse iwo m' dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo." "M' dziko lapansi,"

Iye anatero, “mudzakhala naco cibvuto; koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine.” (Yohane 17: 15; 16: 33.)

M’ciphunzitsa cace ca pa phiri, Kristu anaphunzitsa akuphunzira ace maphunziro a mtengo wapatari za kufunika kwace kwa kukhulupirira Mulungu. Maphunziro amenewa anaperekedwa kulimbitsa ana onse a Mulungu m’ mibadwo yonse, ndipo afikira nthawi yathu ino odzazidwa ndi malangizo ndi cisangalatso. Mpu-lumutsi anawalozera akuphunzira ace mbalame za mlengalenga, pamene zinali kuyimba nyimbo zawo zoyamika, zosabvutika ndi nkhawa, cifukwa “sizimafesa ai, kapena sizimatema ai.” Ndipo cikhalirebe Atate wamkuru amazipatsa zosowa zawo. Mpulumutsi afunsa, “Nanga inu mulibe kusiyana nazo kuziposa kodi?” (Mateyu 6: 26.) Wogawira Wamkuru wa munthu ndi nyama amatsegula dzanja lace, ndi kukhutitsa zilengedwe zace zonse. Amasamalira mbalame za mlengalenga. Samaponya cakudya m’ milomo yawo, koma amazipatsa zosowa zawo. Zidzitola zokha zakudya zimene Iye adazimwazira. Zidzimanga zokha zisa zawo. Zidzidyetsa ana awo. Zimanka ziri kuyimba ku nchito yawo, cifukwa, “Atate wanu wa kumwamba azidyetsa.” Ndipo “Nanga inu mulibe kusiyana nazo, kuziposa kodi?” Kodi inu, anthu a nzeru, ompembedza mu mzimu, simuli a mtengo wapatari koposa mbalame za mlengalenga? Kodi Mlengi wathu, Wosungira wa moyo wathu, Yemwe anatilenga ife m’ cifaniziro cace, sadzatipatsa ife zosowa zathu ngati ife timkhulupirira?

[89]

Kristu analozera akuphunzira ace maluwa a m’thengo okula bwino ndi onunkhira, ndi okongola mu ubwino umene Atate wa kumwamba anawapatsa monga citsimikizo ca cikondi cace kwa munthu. Iye anati, “Tapenyetsani maluwa a kuthengo makulidwe awo.” Kukongola kwa maluwa a kuthengowa kwapitirira ulemerero wa Solomo. Zobvala zokongola koposa, zopangidwa ndi anthu a luso, sizingathe kulingana ndi kukongola kwa maluwa amene Mulungu adawalenga. Yesu afunsa, “Koma ngati Mulungu abveka coteru maudzu a kuthengo, akhala lero, ndi mawa aponyedwa pa moto, nanga si inu kopambana ndithu, inu akukhulupirira pang’ono? (Mateyu 6: 28, 30.) Ngati Mulungu, m’ misiri wa kumwamba, amapatsa maluwa amene angoonongeka m’ tsiku limodzi, maanga awo abwino osiyanasiyana, kodi sadzawasamalira kopambana iwo amene adawalenga m’ cifanizo cace comwe? Phunziro la Yesuli

liri kudzudzula mtima woda nkha-wa, wobvutika ndi wokaika, ndi wopanda cikhulupiro.

Yehova afuna kuti ana ace onse amuna ndi akazi adzikhala okondwa, a mtendere, ndi omvera. Yesu ati, “Mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa. Mtima wanu usabvutike, kapena usacite mantha.” “Izi ndalankhula ndi inu, kuti cimwemwe canga cikhale mwa inu, ndi kuti cimwemwe canu cidzale.” (Yohane 14: 27; 15: 11.)

Cimwemwe cimene cimacokera mu umbombo, osati mu nchito, ncacabe ndi cosakhalitsa; cimangocoka, ndi kusiya moyo woun-gulumwa ndi wa cisoni; koma muli cimwemwe ndi kukwanit-sidwa m’nchito ya Mulungu; Mkristu sadasiyidwe kuyenda m’njira zosadziwika; sadasiyidwe m’zisoni zopanda pace, ndi zogwiritsa mwala. Ngati sitilandira zokondweretsa za moyo uno, tidzin-gokondwerabe pa kuyembekezera moyo ulinkudza.

[90] Koma ngakhale pansi pano Akristu adzakhala ndi cimwemwe ca kulankhula ndi Kristu; adzakhala ndi kuunika kwa cikondi cace, cisangalatso cosatha ca nkhope yace. Phazi liri lonse m’moyo lidzatitengera cifupi ndi Yesu, lidzatipatsa ife macitidwe oona a cikondi cace, ndipo tidzasuntha phazi limodzi kuyandikira kwathu kodala kwa mtendere. Tiyeni tsono, tibataye cilimbiko cathu, koma citsimikizo cathu cikhale colimba koposa kale. “Kufikira pano Yehova anatithandiza” (1 Sam. 7: 12), ndipo adzatithandizabe ku-fikira cimariziro. Tiyeni tiyang’ane ku zinthu zokumbutsa, zokum-butsa zimene Yehova anacita kutisangalatsa ndi kutipulumutsa ife ku dzanja la woonongayo. Tiyeni tikumbukire m’mitima yathu za cifundo zimene Yehova waticitira ife, — misozi imene waipukuta, zowawa zimene wazitonhoza, nkhwawa zimene wazicotsa, man-tha amene wacotsa, zosowa zimene watipatsa, madalitso amene wapereka, — potero tidzadzilimbitsa tokha kwa zonse zimene ziri patsogolo pathu kupyola kotsala kwa ulendo wathu.

Sitingathe kuleka kuyang’ana zobvuta zatsopano zimene ziri kudza m’nkondo yathu ya mtsogolo, koma tiyenera kuyang’ana zam’mbuyo, cimodzimodzi za mtsogolo ndi kunena, “Kufikira pano Yehova anatithandiza.” “Monga masiku ako momwemo mphamvu yako.” (Deut. 33: 25.) Mayeso sadzakhala optirira mphamvu zimene zidzapatsidwa kwa ife za kupirira nazo. Pompo tiyeni titenge

nchito yathu komwe taipezera, tiri kukhulupirira kuti ciri conse comwe cingadze, adzatipatsa mphamvu zokwanira ndi mayesowo.

Ndipo patsogolo pace zipata za kumwamba zidzatsegulidwa kulowetsa ana a Mulungu, ndipo m’ milomo ya Mfumu ya ulemerero mudzaturuka dalitso longa nyimbo yokometsetsa, “Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi.” (Mateyu 25: 34.)

Pompo oomboledwa adzaloledwa kulowa m’zinyumba zimene Yesu ali kuwakonzera. Kumeneko anzawo sakakhala zonyenga za dziko, a mabodza, opembedza mafano, onyansa, ndi osakhulupirira; koma akazolowerana ndi iwo amene anagonjetsa Satana, ndi amene mwa cisomo ca Mulungu anapanga makhalidwe angwiro. Coipa ciri conse, conyansa ciri conse cimene cinali kuwabhuta pansu pano, cinacotsedwa ndi mwazi wa Kristu, ndipo ukulu ndi kuwala kwa ulemerero wace, wowala koposa dzuwa, udzapatsidwa kwa iwo. Ndipo makhalidwe ace abwino ndi angwiro adzawala mwa iwo koposa kunja kwawo. Adzakhala opanda cifukwa patsogolo pa mpando wacifumu woyera, ali kugawana nawo ulemu ndi mwayi wa angelo.

Poyang’ ana cuma ca ulemerero cimene cidzakhala cace, “Kodi munthu adzaperekanji cosintha naco moyo wace?” Mateyu 16: 26.) Ngakhale ali wosauka, koma adzalandira mwa iye yekha cuma ndi ulemu zimene dziko silingathe kumpatsa. Moyu woomboledwa ndi wotsukidwa mu zoipa, ndi mphamvu zace zonse zoperekedwa ku utumiki wa Mulungu, uli wa mtengo wapataru; ndipo kuli cimwemwe m’mwamba pamaso pa Mulungu ndi angelo oyera cifukwa ca moyo umodzi woomboledwa, cimwemwe cimene cimatsimikizidwa m’nyimbo za cigonjetso coyera.